

Republic of Zambia

MINISTRY OF EDUCATION

PRIMARY EDUCATION

LITERACY AND LANGUAGE

M'CINYANJA

BUKU LOTHANDIZILA MPHUNZITSI

GILEDI 1: TEMU 3

Developed by the Curriculum Development Centre

Lusaka

April 2025

UMWINI

Umwini wonse ndi wotetezedwa. Osalembanso bukuli kapena zigawo zake mnjila ina iliyonse popanda cilolezo cocokela kwa eni ake a Curriculum Development Center.

© Curriculum Development Center

Linasindikizidwa koyamba m'Cinyanja

mu 2025 ndi a Curriculum Development Center.

First Published 2025 by

Zambia Educational Publishing House

Light Industrial Area

Chishango Road

P. O. Box 32708

Lusaka, Zambia

Printed by:

Zambia Educational Publishing House (ZEPH)

MASOMPHENYA

Maphunzilo ophindulitsa moyo wonse wamunthu, omwe apezeka mosabvuta, opelekedwa mopanda tsankho, ndiponso othandiza popeleka zotsowa zonse zopindulitsa munthu molingana ndi m’mene maphunzilo amaiko ena alili.

ALEMBI

Ms. Rabecca Tembo	Head of Department, Nyamphande Boarding, Lusangazi
Joshua Zulu	Lecturer, Chalimbana University, Chongwe
Belita Sakala	Lecturer, Chipata college of Education, Chipata
Elizabeth Banda	Mngoza Primary, Petauke
Jonathan Ngoma	Kabvuma Primary School, Nyimba
Thomas Zulu	Masomphenya Primary School, Lusangazi
Mary Phiri	Kanjala Primary, Chipata

Zamkatimu

UMWINI 2
MASOMPHENYA 3
ALEMBI 4
Zamkatimu 5
MAU OYAMBA 6
CIYAMIKO 7
LAMBULO 8
MOGWILITSILA NCHITO BUKULI 9
MATANTHAUZO A MAU 10
CAPAMUTU 1: KULONGOSOLA MALO 13
CAPAMUTU 2: KUFOTOKOZA MAONEKEDWE A ZINTHU 41
CAPAMUTU 3: SEWELO 69
CAPAMUTU 4 : KUKAMBA ZILAPI 101
CAPAMUTU 5 KUMVETSELA NDI KULANKHULA 139
CAPAMUTU 6: KULOWEZA MAU OPINDA LILIME 173
BIBLIOGRAPHY 207

MAU OYAMBA

Kubwela kwa maphunziro opindulitsa opatsa maluso ochedwa Competence Based Curriculum (CBC) kwabweletsanso msintho pa kaphunzilidwe katsopano komanso kothandiza. Maphunzilowa atsopano ali ndi zophunzitsila zomwe zimapangitsa aphunzi kukhala ndi maluso amakono. Kusinthaku kuonetsanso ciyambi cotukula maphunzilo komanso kufunikila kwake.

Buku lophunzitsila Cinyanja geledi 1 yapangidwa mogwilizana ndi mfundo za amaphunzilo omwe akufuna kulumikiza maphunzilo ndi umoyo watsiku ndi tsiku. Maluso onse omwe apelekedwa mbuku yoonetsa ndondomeko yonse yamaphunzilo ya 2023 (Curriculum framework) ndi wogwilizana ndi bukuli.

Colinga ca bukuli ndikuthandiza aphunzitsi a maphunzilo giledi 1 (primary Education) kucilikiza maphunzilo atsopano a CBC Pamene mabuku ololedwa akali osowekela. Bukuli likuonetsa kudzipeleka kosasunthika kwa cigawo ca zamaphunzilo kuti nchito ya aphunzitsi ikhale yapafupi, pakupatsa ndondomeko ya uphungu, ntchito zoyeselela ndi mayeso ogwilizana ndi zolinga za CBC. Komabe, aphunzitsi alimbikitsidwa kuonjezele zida zophunzitsila kupyolela mkafuku-fuku kao kuti athane ndi zotsowekela zilizonse pomwe agwilitsa nchito CBC.

Ndikhulupilila kuti aphunzitsi azagwilitsa ncito buku limeneli moyenela.

Kelvin Mambwe (PhD)

Permanent Secretary-Education Services

Ministry of Education

CIYAMIKO

Buku lakuwelenga ndi kulemba m'Cinyanja lapangidwa kupyolela mkugawana nzelu ndi kugwilila nchito pamodzi ndi ena. Anthu ambili, zigawo ndi mabungwe anafunsidwa ndi kupatsidwa mpata woti apeleke maganizo ao pa uthenga womwe unafunika kukhala mbukuli. Mwaico ndifuna kupeleka mathokozo anga kwa anthu , zigawo ndi mabungwe omwe anapeleka thandizo ya ndalama ndi ukaswili wao kuti buku limeneli lophunzitsila lilembedwe moyenelela. Awa ndi aphunzitsi, aphunzitsi amasukulu apamwamba kwambili, mabungwe oimilila ziphunzitso (subject associations), Mabungwe akunja kwa boma ndi mabungwe ogwilizana nao.

Pomaliza, ndithokozanso anyanchito a cigawo ca Curriculum Development Centre pakusimikizila kuti nchito yolemba bukuli yamalizidwa moyenela.

Charles K. Ndakala, (Dr.)

Director Curriculum Development

Ministry of Education

LAMBULO

Buku lophunzitsila aphunzi a geledi 1 lapangidwa mozama kuti lithandizile aphunzitsi kuphunzitsa maphunzilo a Cinyanja mogwilizana ndi maphunzilo osinthidwa. Bukuli lapangidwa molingana ndi ndondomeko yobvomelezeka ya kaphunzitsidwe ka Cinyanja ya caka ca 2023. Ndondomeko imeneyi ikufuna kuwongolela kusiyana komwe kunapangidwa cifukwa ca kusowa kwa mabuku obvomelezeka komanso kupatsa aphunzitsi zida zophunzitsila zothandiza, zocita, ndi mayeso yopangidwa kulingana ndi kalasi la ophunzila ndi zosowa zao.

Cigawo ca zamaphunzilo cidziwa zobvuta zomwe zimabwela cifukwa cosintha maphunzilo. Kusankha ndondomeko yamaphunzilo opatsa ana maluso osiyana-siyana (Competence Based Curriculum) ndi ciyambi ca kusintha kopititsa patsogolo maphunzilo ndi kufunikila kwake. Bukuli lionetsa kudzipeleka ndi cidwi ca cigawo ca zamaphunzilo kupanga nchito ya aphunzitsi kuti ikhale yotheka pakuwapatsa ndondomeko ya uphungu, nchito ndi mayeso omwe alunjikidwa ndi ndondomeko ya zolinga za maphunzilo atsopano. Komabe, aphunzitsi alimbikitsidwa kuti naonso angathe kuwonjezela pakucita kafuku-fuku wawo komanso Kupanga zida zao zophunzitsila kuti athane ndi zotsowa zina zomwe zingabuke pogwilitsa nchito ndondomeko yatsopanoyi.

Zocita ndi mayeso zomwe zapelekedwa zapangidwa kuti zizilimbikitsa ndi kukulitsa maluso eni-eni anchito zamanja ndi maluso oganiza mwakuya mwa aphunzi pomwe akuwonetsa kufunikila kwa kugonjela msintho kumalo amaphunzilo osiyana-siyana. Aphunzitsi alimbikitsidwa kugwilitsa nchito uphungu uwu mumakalasi awo osiyana-siyana ndi kufufuza njila zina zololedwa, zobvomelezeka pakafunika kutelo. Kusintha kumeneku ndi kofunikila pakuonetsetsa kuti aphunzi onse, ocokela kumalo osiyana-siyana aphindula ndi maphunzilo abwino atsopano.

Ciyembekezo ndi cakuti bukuli lidzakhala cida cofunikila kwambili kwa aphunzitsi pomwe asewenzetsa ndondomeko yamaphunzilo atsopano yochedwa Competence Based Curriculum, kukulitsa luso lao lopatsa aphunzi cidziwitso cokwanila cokhudza cilankhulo ca Cinyanja maluso omwe angathandize aphunzi kukhala ndi cidwi comwe cingapangitse maphunzilo kukhala aphindu.

MOGWILITSILA NCHITO BUKULI

Bukuli lipeleka uthenga womwe uyenela kuphunzitsidwa mu temu laciwili la giledi 1. Bukuli ndilogawidwa mzigawo ndipo cigawo ciliconse cili ndi maphunzilo ocokela muzigawo zina zosiyana-siyana zomwe ndi Kumvetsela ndi Kulankhula, kuwelenga, matanthauzo a mau, mvetso, ndi kulemba. Uthenga womwe waikidwa mbukuli siunalembedwe mumaphunzilo (lesson plans), koma uyenela kugwilitsidwa nchito kulemba maphunzilo (lessons). Popanga maphunzilo, muyenela kutenga uthenga kucokela kuzigawo zosiyana-siyana kupanga phunzilo limodzi. Mwacitsanzo, Phunzilo lingakhale ndi kumvetsela ndi kulankhula, matanthauzo a mau, kuwelenga ndi kulemba. Popanga phunzilo, muyenela kusankha mfundo zophunzitsa zomwe muzagogomezapo m'phunzilo ndi nchito zocita aphunzi pa luso lapadela lililonse. Apa zikutanthauza kuti phunzilo linzakhala ndi maluso apadela oposa limodzi. Koma, mphunzitsi adzasankha kuti ndi gawo iti yomwe adzagogomezapo mphunzilo lake ndi kuipatsa nthawi yaitali koposa ena. Moonjezela, nchito zopatsidwa pa luso lapadela siziyenela kucitidwa zonse mu phunzilo limodzi ai. Zimenezi zingacitidwe mumaphunzilo osiyana-siyana.

NJILA YOPHUNZITSILA

Kaphunzitsidwe kayenela kulondola njila yapang-ono-pang'ono yomwe inena kuti poyamba, mphunzitsi acite nchito yoonetsela potsatila pake, acitile nchitoyo pamodzi ndi aphunzi ndipo pothela aphunzi acite aliyense payekha (Gradual Release Model (GRM), Moonjezela, njila zosiyana-siyana zakaphunzitsidwe ziyenela kugwilitsidwa nchito kuti zotsowa zosiyana-siyana za aphunzi zikwanilitsidwe.

MATANTHAUZO A MAU

1. Asanayambe Kulemba- Pre-writing

2. Asanayambe kuwelenga- Pre-Reading

3. Capamutu-Theme

4. Cidule - Overview

5. Cigawo- Component / section

6. Lambulo-Introduction

7. Gwelo la Uthenga- Reference

8. Kayendetsedwe ka maso ndi katsegulidwe ka buku powelenga ndi polemba-Directionality

9. Kudziwa za Zolembedwa-Concept of Print

10. Kuganiza mwakuya- Critical Thinking

11. Kusanthula maganizo Mwakuya- Analytical Thinking

12. Mgwilizano-Collaboration

13. Kukambitsilana- Communication

14. Kudziwa kugwilitsa nchito zinthu za kompyuta- Digital Literacy

15. Kupanga Zatsopano ndi kuonjezela pa zakale- Creativity and Innovation

16. Zokhuza mwini komanso ena- Emotional intelligence

17. Zamalonda- Entrepreneurship

18. Kuthetsa bvuto-Problem Solving

19. Kukambilana-Discussion

20. Kulemba cimodzi- cimodzi- Manuscript Form

21. Mau acikoka –Hook

22. Kulemba mokhotesa-Cursive Form

23. Kumvetsela ndi Kulankhula- Listening and Speaking

24. Kuzindikila Mvekelo- Phonological Awareness

25. Kuzindikila ubale wa lembo ndi Mvekelo- Phonemic awareness

26. Luso lapadela - Specific Competence

27. Luso Lonse-General Competence

28. Luso loyembekezeleka-Expected Standard

29. Malembedwe- Handwriting

30. Masilabe-Syllables

31. Chati yamasilabe- Syllabic Chart

32. Mau ofunika kwambili- Key terms

33. Mayeso-Assessment Activities

34. Mutu- Topic

35. Mutu waung'ono- Sub-Topic

36. Kasungidwe ka nyama- Animal farming

37. Mvekelo za zinthu zosiyana-siyana-Sounds made by different objects

38. Mwacidule- Summary

39. Nchito- Learning activities

40. Ocita Sewelo- Characters

41. Zinthu Zophunzilila ndi Zophunzisila- Teaching and Learning Materials

42. Zindikilani- Note

43. Zocita-Exercise

44  Ciyambi

45  **Mau ofunikila kudziwa**

46  **Nchito**

47  **mwacidule**

CAPAMUTU 1: KULONGOSOLA MAONEKEDWE A MALO

 **Ciyambi:** Mutu uyu uzaona pa kulongosola malo osiyana-siyana. Kulongosola malo kudzathandiza aphunzi kutukula luso la kumvetsela ndi kulankhula, kuzindikila matanthuzo a mau omwe adzagwilitsa nchito m'maphunzilo ena.

CAPAMUTU 1: KUMVETSELA NDI KULANKHULA

Mutu: Kulongosola Maonekedwe

Mutu Waung'ono: Malo

Luso Lapadela: Kulongosola Malo.

 **Mau Ofunikila Kudziwa**: Kulongosola, malo, kuzindikila

Mfundo Zophunzitsa:

- Kufotokoza za malo
- Kulongosola mbali za malo

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Mabuku**,** machati ndi zina

 **Nchito A: Apeleke mau omwe amagwilitsidwa nchito polongosola malo** (Kukula, kucepa, utali wa pansi ndi utali wa m'mwamba)

I. **Mphunzitsi:**

- Uzani aphunzi kalongosoledwe ka mbali za malo.
- Onetsani zizindikilo za mbali za malo (mapili, mitengo, mitsinje, miseu)
- Fotokozani pamodzi ndi aphunzi za ukulu kapena kucepa kwa malo.
- Uzani aphunzi afotokoze za utali kapena ufupi wa malo.

II. Aphunzi:

- Aphunzile mbali za malo.
- Aphunzile zizindikilo za mbali za malo (mapili, mitengo, mitsinje, miseu)
- Amvetsele za ukulu kapena kucepa kwa malo.
- Amvetsele za utali kapena ufupi wa malo
- Alongosole zizindikilo za malo a kwao pakujambula.

Muyeso Woyembekezeleka: Mau olongosolela malo apelekedwa moyenela.

Nchito B: **Kulongotsola malo kugwilitsa nchito mau azindikilidwa.**

I. Mphunzitsi:

- Apeleke citsanzo cakalongosoledwe ka malo pogwilitsa nchito mau ozindikilidwa polongosola malo mwakujambula.
- Gwilitsani nchito ndi aphunzi mau azindikilidwa polongosola malo a kunyumba kwao mwa kujambula.
- Auze aphunzi kuti agwilitse nchito mau azindikilidwa polongosola malo a kusukulu kwao mwa kujambula.

II. **Aphunzi:**

- Amvetsele bwino pomwe aphunzitsi akupeleka citsanzo cakalongosoledwe ka malo.
- Alongosole malo a kunyumba kwa pogwilitsa nchito mau azindikilidwa.
- Alongosole malo a ku sukulu kwao pogwilitsa nchito mau azindikilidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Mau azindikilidwa agwilitsidwa nchito moyenela polongosola malo.

Nchito C: Kucita masewela olongosolela malo monga ukazitape ndi ndine yani.

I. Mphunzitsi:

- Phunzisani aphunzi kaseweledwe ka masewela aukazitape ndi ndine yani polongosola mbali za malo.
- Ikani aphunzi m'magulu ndi kusewela nao masewela aukazitape ndi ndine yani olongosolela mbali za malo.
- Funsni aphunzi kucita masewela aukazitape ndi ndine yani polongosola malo a kunyumba ndi kusululu kwao m'magulu ao.

II. **Aphunzi:**

- Amvetsetse pomwe aphunzi akuphunsitsa maseweledwe a masewela aukazitape ndi ndine yani polongosola mbali za malo.
- Asewele masewela aukazitape ndi ndine yani olongosolela mbali za malo.
- Acita masewela aukazitape ndi ndine yani polongosola malo a kunyumba ndi kusululu kwao m'magulu ao.
- .

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela olongotsola maonekedwe azinthu yaseweledwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kulongosola malo pogwilitsa nchito mau ozindikilidwa

KUWELENGA

MUTU 1: KUZINDIKILA MASILABE

Mutu Waung'ono 1: Kuzindikila masilabe opangidwa ndi **gw-_, mf-_, ms-_, _oo-.**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse masilbe amvekelo amalemba ophatikizana imodzi-imodzi kufikila onse owonetsedwa pa mwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila masilabe gwa, gwe, gwi, gwo, gwu**.**

Ciyambi: Mutu uyu uzaona pa masilabe kucokela ku mau okambidwa, kusewela masewela akuwelenga masilabe omwe ali mu mau pakuomba m'manja, ndi masewela akupanga mau pa kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

Luso Lapadela: Kuzindikila ndi kusintha masilabe.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: zipangizo zogwilika.

Mau Ofunikila Kudziwa: masilabe, vawelo, mvekelo**.**

Mfundo zophunzitsa:

- Kuzindikila masilabe m'mau okambidwa.
- Kusewela masewela owelenga masilabe.
- Kusewela masewela opanga mau okambidwa kugwilitsa nchito masila.
- Kusewela masewela opanga mau posinthanisa ndi kucotsa masilabe.

Kumbukilani kuphunzitsa mamvekelo onse awa: (/gw/, /mf/, /ms/, /oo/)**.**

Nchito A: Kuzindikila masilabe m'mau okambidwa

I. Mphunzitsi:

- Phunzitsani aphunzi kazindikilidwe ka masilabe m'mau.
- Zindikilani pamodzi ndi aphunzi kazindikilidwe ka masilabe m'mau opangidwa **Citsanzo**: gwila = **gwi** ndi **la**
- Uzani aphunzi kuti azindikile masilabe m'mau okambidwa.

Gwada Gwa/wa, Gwapo gwa/po, Gwada gwada,

II. Aphunzi:

- Aphunzile kuzindikila masilabe.

- Aphunzitsi azindikile masilabe m’mau okambidwa pamodzi ndi aphunzi.
- Azindikile masilabe m’mau okambidwa.

Muyeso Woyembekeleka: Aphunzi azindikila masilabe m’mau okambidwa moyenela.

Nchito B: kusewela masewela akuwelenga masilabe

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi kaseweledwe ka masewela owelenga mau.
- Welengani mau omwe ali ndi masilabe gwa, gwe, gwi, gwo, gwu pamodzi ndi aphinzi.
- Ikani aphunzi m'magulu ndipo muwauze kuti awelenge mau opatsidwa omwe ali ndi masilabe gwa, gwe, gwi, gwo, gwu.

II. Aphunzi:

- Amvetsele pomwe aphunzitsi akuphunzitsa kawelengedwe ka mau.
- Awelenge mau omwe ali ndi masilabe gwa, gwe, gwi, gwo, gwu pamodzi ndi aphunzitsi.

  Citsanzo: Gwelo, gwaila, gwada, gwendeza
- Awelenge mau opatsidwa m'magulu ao.

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela owelenga masilabe poomba m’manja acitidwa moyenela.

Nchito C: **Kupanga mau okambidwa kugwilitsa nchito masilabe.**

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi kapangidwe ka mau pogwilitsa nchto masilabe opangidwa ndi mvekelo /gw/.
- Pangani mau okambidwa pogwilitsa nchito masilabe ali ndi mvekelo /gw/ pamodzi ndi aphunzi.

  Citsanzo: Gwa/da = gwada, Gwi/la = gwila, Gwe/tsa = gwetsa
- Ikani aphunzi m'magulu ndipo muwauze kuti apange mau okambidwa pogwilitsa nchito masilabe opangidwa ndi mvekelo /gw/

II. Aphunzi:

- Amvetsetse pomwe citsanzo cikupelekedwa.
- Apange mau pamodzi ndi aphunzitsi.
- Apange mau m'magulu ao omwe ali ndi masilabe opangidwa ndi mvekelo /gw/.

Muyeso Wombekezeleka: Mau okambidwa apangidwa moyenela pogwilitsa nchito masilabe.

Nchito D: kusewela masewela akusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi mosinthila ndi mocotsela masilabe popanga mau ena.
- Yetselelani pamodzi ndi aphunzi kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe m'mau
- Uzani aphunzi kuti akhale awili-awili ndipo asewele masewela opanga mau atsopano posintha ndi pocotsa masilabe.

  Citsanzo

  KUSINTHA

  1. **Gwi**la = sinthani **gwi,** ikamponi **gwe** ndi kupanga **Gwe**la
  2. Gwadula = sinthani **gwa** ikani **gwe** kupanga **gwedula**

  KUCOTSA

  1. Gwilila = lila
  2. Anagwada = gwada
- Uzani aphunzi kuti asinthe ndi kucotsa masilabe m'mau opatsidwa aliyense payekha.

II. Aphunzi:

- Amvetsele bwino masinthidwe ndi macotsedwe amasilabe.
- Apange mau pamodzi ndi aphunzi posintha ndi pocotsa mvekelo monga mcitsanzo cili pamwambapa.
- Asinthe ndi kucotsa masilabe m'mau opatsidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: kusintha ndi kucotsa masilabe kwacitika moyenela.

MUTU 2: Kupanga Masilebe.

Mutu Waung'ono 1: Masilabe.

Ciyambi: mutu uyu udzaona pakulumikiza malemba ndi mavawelo kupanga masilabe.

Luso Lapadela: kulumikiza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe

Mau Ofunikila Kudziwa: Makonsonanti, masilabe, mavawelo.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: mafulashi khadi, , silabiki chati

Mfundo Zophunzitsa:

- kupanga masilabe
- kulumikiza makonsonanti ndi mavawelo

 **Nchito A: Kupanga masilabe pa kulumikiza makonsonanti ndi mavawelo**

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi kasakanizidwe kamakonsonanti ndi mavawelo popanga masilabe.
- Pangani masilabe ndi aphunzi kugwilitsa nchito makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.
- Uzani aphunzi kuti apange makonsonanti ndi mavawelo pogwilitsa nchito mvekelo /gw/.

II. Aphunzi:

- Aonelele masakanizidwe a masilabe ndi mavelo pogwilitsa nchito makonsonanti ndi mavawelo pogwilitsa nchito mvekelo /gw-/.
- Apange masilabe ndi aphunzitsi kugwilitsa nchito makonsonanti ndi mavawelo.
- Apange masilabe kulingana ndi makonsonanti omwe apatsidwa.

 **Zocita:**

Aphunzi apange masilabe kugwilitsa nchito makonsonanti ndi mavawelo apatsidwa.

Gw/a, Gw/e, Gw/i, Gw/o, Gw/u

Muyeso Woyembekezedleka: Kusakaniza kwa makonsonanti ndi mavawelo kwacitidwa moyenela.



Nchito B : Kuwelenga chati yamasilabe.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani chati ya masilabe kwa aphunzi.
- Sonyezani kuwelenga masilabe ali pa chati.
- Uzani aphunzi awelenge masilabe.
- Thandizilani aphunzi kuwelenga m'magulu masilabe ali pa chati.

II**. Aphunzi:**

- Aone chati ya masilabe.
- Amvetsele kuwelenga masilabe ali pa chati.
- Awelenge masilabe.
- Awelenge m'magulu masilabe ali pa chati.

Zocita

1. Lembani masilabe osowa mwa awa.

gwa gwe ….. gwo gwu.

2. Welengani masilabe ali pa 1

Muyeso Woyembekezeleka: Chati ya masilabe yawelengedwa moyenela.



Nchito C : Kusankha masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Sankhani masilabe kucokela pa makhadi ya malembo.

- Udzani aphunzi kuti asankhe masilabe kucokela pa makhadi ya malembo

  Citsanzo:

  Gwila, gwa, bwela, gwada, gwe, gula, gwi, nzelu, gwu, mwana, gwo.

  Yankho : gwa gwe gwi gwo gwu

II. Aphunzi:

- Aonelele masankhidwe a masilabe pakati pa malembo pakati pa malembo, mau ndi masilabe.
- Asankhe masilabe pakati pa mau.

Zocita:

1. Sankhani masilabe kucokela pa malembo, masilabe ndi mau.

   gwa, mwano, gwelo, gwada, gwe, gwila, gwo, bwela, gwu, gwi

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe asankhidwa moyenela.



Nchito D : Kusintha Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Achule mau monga gwila
- Sonyezani kasinthidwe kamasilabe mu mau.

  Citsanzo:

  Gwila– khala– sinthani ‘gwi’ ikani ‘kha’ kupanga khala.

II. **Aphunzi:**

- Aone ndi kumvetsela kasinthidwe ka masilabe m’mau.
- apange mau atsopano pa kusintha masilabe m’magulu ao.

  gwetsa – tsitsa— sinthani ‘gwe’ ikani ‘tsi’ kupanga ‘tsitsa’

gwelo — bwalo —- sinthani ‘gwe’ ikani ‘bwa’ kupanga bwalo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kusintha masilabe m’mau ndikupanga mau atsopano kwacitika moyenela.

 Nchito E: Kulumikidza malembo ophatikizana koma omveke mosiyana amakonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

I. Mphunzitsi:

- pelekani citsanzo ca makonsonanti omwe sali ndi mvekelo imodzi kupanga masilabe polumikiza ndi mavawelo.

  Citsanzo:

  a e i o u

  gwa gwe gwi gwo gwu

II. Aphunzi:

- Aone citsanzo ca makonsonanti amwe sali ndi mvekelo imodzi
- Amvetsele molumikizila makonsonanti omwe sali ndi mvekelo imodzi ndi mavawelo kupanga masilabe.
- m’magulu ao apange masilabe polumikiza makonsonanti omwe sali ndi mvekelo imodzi ndi mavawelo kupanga masilabe.

Muyeso Woyembekezeleka: Malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti ndi mavawelo alumikizidwa ndi kupanga masilabe moyenela.

 **Mwacidule**: Mutu uyu unali kuona pa kupanga masilabe kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo, kuwelenga masilabe pa chati la masilabe, kusankha masilabe ndi kusintha malembo.

B. KUWELENGA

MUTU 1: Kupanga Mau ndi g**wa, gwe, gwi, gwo , gwu**

Mutu Waung'ono 2: Mau

**Ciyambi:** Mutu uyu uzaona pa kulumikidza masilabe kupanga mau, kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano, kuzindikila masilabe mu mau ndi kuwelenga masilabe.

Luso Lapadela 1: Aphunzi apange mau osiyana-siyana polumikidza masilabe.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Silabiki chati, mafulashi khadi

**Mau Ofunikila Kudziwa:** Makonsonanti, mavawelo, masilabe, kulumikidza

Mfundo Zophunzitsa:

- Kulumikidza masilabe kupanga mau
- Kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano ndi aphunzi
- Kupenda masilabe m'mau.

**Nchito A Kulumikaza masilabe popanga mau**

Mphunzitsi:

- Onettsani aphunzi mapangidwe a mau kugwilitsa nchito masilabe.
- Pangani ndi aphunzi mau kugwilitsa nchito masilabe.
- Uzani aphunzi kuti apange mau pogwilitsa nchito masilabe m'magulu ao.

Aphunzi:

- Aphunzile mapangidwe a mau.

- Apange masilabe ndi aphunzi
- Apange mau kugwilitsa nchito masilabe m’magulu ao.

1. Gwe/sa gwesa
2. Gwa/za gwaza
3. Gwa/po gwapo

Muyeso Wombekeleka: Masilabe aphatikizidwa kupanga mau moyenela



Nchito B: Kucotsa ndi kuika masilabe ena m’mau

I. Mphunzitsi:

- Onetsani kacotsedwe ndi kaikidwe ka masilabe m'mau.
- Ccotsani ndi kuika masilabe pamodzi ndi aphunzi
- Uzani aphunzi kuti acotse ndi kuika masilabe ali ndi mvekelo /gw/ m'magulu ao.

1. Gwa**wa** gwa**da**
2. Gwa**po** gwa**pe**
3. **Ku**gwila gwila

II. Aphunzi:

- Aonelele mocotsela ndi kuika masilabe kupanga mau ena
- Apange mau ena pamodzi ndi mphunzitsi
- Apange mau ena pocotsa masilabe ena

Muyeso Woyembekezeleka: Nchito zopanga mau zakwanitsidwa moyenela



Nchito C: Kuzindikile masilabe m’mau.

I. Mphunzitsi:

- Onetsni aphunzi mazindikilidwe a masilabe m'mau.
- Citani nchito ndi aphunzi ya kuzindikila masilabe m’mau.

- Uzani aphunzi kuti azindikile masilabe onenedwa m’mau poika kamzele munsi mwa silabe m'magulu ao.

II. Aphunzi:

- Aphunzile mozindikilila masilabe m'mau.
- Azindikile masilabe m’mau ndi aphunzitsi ndiponso okha.

  Citsanzo

  Gwa/mpó/ni, gwe/ lo, gwe/nde/ za

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe azindikilidwa moyenela.



Nchito D: Kuwelenga masilabe

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi kazindikilidwe ka masilabe m'mau.
- Welengani masilabe m’mau ndi aphunzi.
- Uzani aphunzi kuti azindikile nambala ya masilabe m’mau opatsidwa.

II. Aphunzi :

- Amvetsele bwino pomwe aphunzitsi akuphunzitsa kazindikilidwe ka mau.
- Awelenge ndi aphunzitsi masilabe ali m’mau.
- Azindikile nambala ya masiabe m’mau.

1. Gwadani 3
2. Gwamula 3
3. Gwaza → 2

Muyeso Woyembekezeleka: Aphunzi azindikila namabala ya masilabe m’mau osiyana-siyana moyenela.



Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kulumikidza masilabe kupanga mau, kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano, kuzindikila masilabe mu mau ndi kuwelenga masilabe.

Luso Lapadela 2: Kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau koyenela.

 **Nchito: Kuwelenga mau**

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau koyenela powelenga mau pa bolodi ndi pogwilitsa nchito timabuku ta nthano.
- Welengani ndi aphunzi mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka bwino.
- Ikani aphunzi awili-awili ndi kuwauza kuti awelenge mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau koyenela monga m'citsanzo ca mphunzitsi.

II Aphunzi:

- Amvetsele bwino pomwe citsanzo cili kupelekedwaa.
- Awelenge mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau koyenela.
- Akhale m'magulu ndi kuwelenga mau monga m'citsanzo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga mau mofulumila ndi kuchulila mau komveka bwino kwacitika moyenela.

Luso Lapadela 3: Kuwelenga ndime mokweza ndi kachulidwe ka mau koyenela.

 **Nchito A: Kuwelenga ndi kumvetsa ziganizo**

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kuwelenga ndime mofulumila ndi kuonetsa kayankhidwe ka mafunso kucokela ku ndime yowelengedwa.
- Welengani ndime pamodzi ndi aphunzi.
- Funsani aphunzi mafunso kucokela mu ndime yowelengedwa.

II Aphunzi:

- Amvetsele bwino pomwe aphunzitsi akuwelenga.
- Awelenge ndi kuyankha mafunso kucokela ku ndime yowelengedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga ndime mofulumila, kuimvetsetsa ndi kuyankha mafunso kucokela m'ndimeyo kwacitika moyenela.

 **Nchito B: Kuwelenga ndime kucoka pa ziganizo ziwili (2) kufika pa ziganizo zisanu (5) (kuwelenga kwa gulu, kubwelezela zomwe wina wawelenga kale, kuwelenga awili-awili).**

I Mphunzitsi:

- Welengani ndime mokweza pomwe aphunzi akumvetsela modekha.
- Welengani Pamodzi ndi aphunzi (Choral Reading).
- Uzani aphunzi kuti azibwelezela zomwe mphunzitsi akuwelenga (Echo Reading).
- Uzani aphunzi kuti awelenge awili-awili (Paired Reading).

II. Aphunzi:

- Amvetsele modekha pomwe aphunzitsi akuwelenga.
- Awelenge pamodzi ndi mphunzitsi,
- Abwelezele zomwe mphunzitsi akuwelenga.
- Awelenge awili-awili.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga ndime yokwanila mizela iwili kufika pa isanu kwacitika moyenela

 **Nchito C: Kuzindikila zolembedwa zili ndi mvekelo zosiyana-siyana ndi zolumikidzana.**

I. Mphunzitsi

- Pelekani mabuku omwe ali ndi nkhani zosiyana-siyana
- Onetsani mowelengela nkhani
- Welengani nkhani ndi aphunzi
- Uzani aphunzi kuti awelenge nkhani**.**

II. Aphunzi

- Alandile mabuku ali ndi nkhani zowelenga.
- Aonelele mowelengela
- Awelenge nkhani aliyense payekha.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga mokuwa ndime yomwe ili masilabe osiyana-siyana kwacitidwa moyenela

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa kuwelenga masilabe, mau ndi nkhani momveka ndi kaculidwe ka mau koyenela.

MVETSO

MUTU 1: MVETSO YA KUMVETSELA

Mutu Waung'ono 1: Ganizo Leni-Leni.

 **Ciyambi:** Mutu uyu udzayangana pa kuzindikila ndi kutulutsa ganizo leni-leni pa zomwe amva.

Luso Lapadela: Azindikile ndi kupeleka maganizo leni-leni kulingana ndi zomwe zamva.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Makhadi a ziganizo, mabuku.

 **Mau Ofunikila Kudziwa:** Maganizo, mvetselo.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuphunzitsa m’mene aphunzi angapelekele maganizo ao pa zomwe amva kapena kuwelenga.
- Kuwelenga nkhani kwa aphunzi ndi kuwafunsa mafunso mwakulankhula cabe.

Kuuza aphunzi kuti apeleke cigamulo kulingana ndi zomwe amva.



Nchito A: Kuzindikila ndi kupeleka ganizo leni-leni pa zomwe amva

I. **Mphunzintsi:**

- Uzani aphunzi kuti amvetsele ku nkhani yapamtima yomwe izakambidwa kapena kuwelengwedwa.
- Citani nchito ndi aphunzi ya kulingalila nkhani yakambidwa.
- Funsani aphunzi kuti apeleke maganizo ao kulingana ndi zomwe azamva.

II. Aphunzi:

- Amvetsele bwino ku nkhani zokambidwa kapena zowelengedwa.
- Acitate nchito ya kulingalila nkhani yakambidwa.
- Apeleke maganizo ao kulingana ndi zomwe azamva.

Muyeso Woyembekezeka: Ganizo leni-leni lazindikilidwa ndi kupelekedwa moyenela.



Nchito B: Kufupikitsa uthenga.

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani kwa aphunzi yosavuta
- Yeselelani kufupikisa uthenga wa nkhani yawelengedwa pamozi ndi aphunzi.
- Uzani aphunzi kuti afotokoze nkhani zomwe amva mwakutengamo cabe mfundo zeni-zeni.

II. Aphunzi:

- Amvetsele nkhani yapafupi
- Aye tselele kufupukitsa nkhani ya welengedwa.
- Afotokoze nkhani zomwe amva mwakutengamo cabe mfundo zeni-zeni.

Muyeso Woyembekezeleka: Nkhani yafupikitsidwa moyenela.

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa kufupikitsa maganizo kulingana ndi zomwe aphunzi amva.

D. MVETSO

MUTU 1: Kumvetsela

Mutu Waung'ono 2: Zazoona ndi Malingalilo Cabe.

 **Ciyambi:** Mutu uyu uzayangana pakuzindikila malingalilo cabe kucokela mnkhani yazoona.

Luso Lapadela: Kusiyanitsa pakati pa zazoona ndi malingalilo cabe.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Makhadi a ziganizo, mabuku.

 **Mau Ofunikila Kudziwa:** Maganizo, malingalilo, kuzindikila, kusiyanitsa.

Mfundo zophunzitsa:

- Kuphunzitsa m'mene aphunzi angazindikilile maganizo cabe pa nkhani zazoona zomwe amva.
- Kuwelenga nkhani kwa aphunzi ndi kuwafunsa mafunso mwakulankhula cabe.
- Kuuza aphunzi kuti apeleke maganizo ao kulingana ndi zomwe amva

 **Nchito A: Kuzindikila lingalilo mnkhani.**

I. **Mphunzitsi:**

- Welengani nkhani kwa aphunzi yapafupi
- Yeselelani ndi aphunzi kuzindikile lingalilo cabe.
- Uzani aphunzi kuti azindikila ligalilo/ganizo mnkhani yokambidwa kapena yowelengedwa.

II. **Aphunzi:**

- Amvesele nkhani yawelengedwa ndi aphunzi
- Ayeselele kuzindikila lingalilo.
- Amvetsele bwino ku nkhani ndipo azindikilo lingalilo cabe ili mnkhaniyo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila lingalilo mnkhani kwacitidwa moyenela.

 **Nchito B: Kuzindikila zoona za nkhani.**

I. **Mphunzitsi:**

- Welengani nkhani kwa aphunzi
- Yetsanni kuzindikila cazoona mnkhaniyi pamodzi ndi aphunzi
- Uzani aphunzi kuti azindikila cazoona mnkhani yokambidwa kapena yowelengedwa.

II. **Aphunzi:**

- Amvetsele nkhani kwa aphunzitsi
- Ayetselele kuzindikila cazoona mnkhaniyi pamodzi ndi aphunzi
- Azindikile cazoona mnkhani yokambidwa kapena yowelengedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Cazoona casiyanitsidwa ku ganizo cabe moyenela.

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa kusiyanitsa cazoona ku malingalilo cabe.

MUTU 2: MVETSO YA KUWELENGA

Mutu Waung'ono 2: Zoona za nkhani

**Ciyambi:** Mutu uyu udzayangana pa kupeleka uthenga kulingana ndi zomwe zamveka mnkhani yawelengedwa.

Luso Zapadela: Kupeleka uthenga omveka bwino kucokela nkhani.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: makhadi a ziganizo, mabuku.

**Mau Ofunikila Kudziwa:** uthenga, kupeleka, kufotokoza.

Mfundo zophunzitsa:

- Phunzitsani m'mene aphunzi angapelekele uthenga omvekka kucokela ku nkhani yowelengedwa.
- Yetselelani ndi aphunzi kupeleka uthanga.
- Fotokozani kuti popeleka uthenga umatenga cabe mitu yeni-yeni a nkhaniyo.

**Nchito A: Kufotokoza zomwe zawelengedwa.**

I. **Mphunzitsi :**

- Welengani nkhani ndipo muwauze aphunzi kuti amvetsele modekha pamene mukuwelenga nkhaniyo.
- Uzani aphunzi kuti naonso awelengeko nkhaniyo m'modzi-m'modzi, m'magulu ang'ono-ang'ono ndiponso kalasi yonse.
- Uzeni aphunzi kuti afotokoze zomwe amva mnkhani.

II. **Aphunzi :**

- Amvetsele modekha pamene nkhani ikuwelengedwa.
- Awelenge nkhani mm'magulu ang'ono-ang'ono ndiponso kalasi yonse.
- Afotokoze zomwe amvamo mnkhani.

Nkhani

Gwendezani ndi Batizani anali kutsutsana kuti gwada sindiwo.

Amai ao atamva zakutsutsana, anaganiza zophika ndiwo za gwada kuti athese mkangano.

Tsikulo Gwendezani ndi Batizani onse anadya nsima ya gwada.

Muyeso Woyembekezeleka: Zomwe zawelengedwa zafotokozeddwa moyenela.

 **Nchito B: Kuyankha Mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa**.

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti muzawawelengela nkhani ndipo azafunika kumvetsa cifukwa muzawafunsa mafunso
- Uzani aphunzi kuti ayankhe mafunso kucokela ku zomwe zawelengdwa mnkhani.

II. Aphinzi:

- Amvetsele ku nkhani
- Ayankhe mafunso kulingana ndi zomwe awelenga.

Mafunso

1. Kodi Batizani anali kukangana ndiyani?

2. Anali kukangana cifukwa ca ciyani?

3. Amai ao anacita ciani kuti athese mkangano?

4. Kodi unakakhala iwe, unakacita ciyani kuti uthetse mkangano?

Muyeso Woyembekezeleka: Mafunso ayankhidwa moyenela.

Nchito C: Kufotokoza molondola momwe zinacitika mnkhani.

I. **Mphunzitsi:**

- Fotokozani cimodzi mwa zithu zomwe zinacitika mnkhani
- Uzani aphunzi kuti afotokoze zimene zawelengedwa mnkhani ili pa nchito A.

II. **Aphunzi:**

- Amvetsele ku zofotokozedwa
- Afotokoze molondola momwe zinthu zinacitikila mnkhani yomwe awelenga.

Muyeso Woyembekezeleka: Nkhani yafotokozedwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuyangana pakuwelenga nkhani, kuyankha mafunso ndi kufotokoza zomwe zawelengedwa.

B. KULEMBA.

MUTU 1: MALEMBEDWE

Mutu Waung'ono 1: Malembedwe Okhazikika

Ciyambi: Mutu uyu uzayangana pa malembedwe okhazikika ndi kuzindikila pipata m'mau.

Luso Lapadela: Kulemba mau m'malembedwe okhazikika.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Silabiki chati, mafulashi khadi, makhadi a ziganizo, mabuku.

Mau Ofunikila Kudziwa: Kulemba, kukhazikika, lembo, malembedwe.

Mfundo Zophunzitsa:

- Uzani aphunzi kuti malembedwe ali ndi malamulo omwe afunika kulondoledwa polemba.
- Fotokozani za lamulo lamicila yopita kumwamba komanso micila obwela pansi mumalembedwe

Nchito A: Kujambula mau m'malembedwe okhazikika.

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca malembedwe a mau polondola malembedwe okhazikika ndiponso polemekeza micila opita kumwamba komanso pansi.
- **Citani cimodzi-modzi ndi mvekelo zina.**

II. Aphunzi:

- Aonelele ku citsanzo copelekedwa
- Alembe mau molondola bwino zomwe aphunzitsidwa pakalembedwe ka malembo.

Zocita:

1. Nkhono.

2. Nkhumba.

3. Nkhani

Muyeso Woyembekezeleka: Mau alembedwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuyangana pakalembedwe ka mau kokhazikika.

MUTU 1: Malembedwe

Mutu Waung'ono 2: Mipata a mau.

Ciyambi: Mutu uyu uzaona pa malembedwe okhazikika.

Luso lapadela: Kusiya mipata m'mau.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Fulashi khadi, makhadi a ziganizo, mabuku.

Mau Ofunikila Kudziwa: Kulemba, kukhazikika, lembo, mipata.

Mfundo zophunzitsila:

- Uzani aphunzi kuti malembedwe abwino aziganizo ayenela kukhala ndi mipata pakati opa mau.
- Fotokozaninso za lamulo lamicila yopita kumwamba komanso micila obwela pansi mumalembedwe.

Nchito A: Kujambula ziganizo m'malembedwe okhazikika.

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca malembedwe a ziganizo pozindikila ndi kusiya mipata pakati pa mau.
- **Citani cimodzi-modzi ndi mvekelo zina.**

II. Aphunzi :

- Alembe ziganizo ndi kulemekeza kusiya mipata pakati pa mau.

Zocita:

1. Nkhono ipezeka kumtunda ndi m'madzi.

2. Nkhumba ndi nyama yoweta.

Muyeso Woyembekezeleka: malembedwe okhazikika alembedwa moyenela.

**Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa malembedwe okhazikika ndi kuzindikila mipata ya mau m'ziganizo.

Mutu 2: Cimangilizo

Mutu Waung'ono 1: Zopumila

**Lambulo:** Mutu uyu uzaona pa kuzindikila zomupila, kulemba ziganizo zathunthu ndi kupanga nkhani yapafupi.

Luso lapadela: Kugwilitsa nchito zopumila zeni-zeni. (Malemba akulu-akulu, copumila kothela kwa liu)

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Chati ya ziganizo, buku la nkhani.

**Mau Ofunikila Kudziwa:** Zopumula, cimangilizo. Nkhani,

Mfundo zophunzitsa:

- Kuphunzitsa zopumila.
- Kuphunzitsa ziganizo.
- Kuphunzitsa nkhani yapafupi.

**Nchito A: Kuzindikila lembo lalikulu ndi copumila cacikulu**

I. **Mphunzitsi:**
   - Uzani aphunzi kuti ciganizo cimayamba ndi lembo lalikulu ndipo cimatha ndi copumila.
   - Patsani citsanzo caciganizo comwe cili ndi lemba lalikulu ndi copumila.

- Patsani aphunzi ziganizo zolembedwa moyenela ndipo muwauze kuti azindikile lemba laikulu ndi copumila polemba kamzele munsi mwake.
-

II. Aphunzi:

- Avetsetse pomwe aphunzitsi akufotokoza za lemba loyamba ndi copumula.
- Aone citsanzo ca ciganizo ca lembo lalikulu ndi copumula.
- Azindikile lembo lalikulu ndi copumila polemba kamzele munsi mwake.

Citsanzo

1. Atate atyola msale.
2. Mfumu yagwidwa ndi cisoni.

Muyeso Woyembekezeleka: Lembo lalikulu ndi copumila cazindikilidwa moyenela.

Nchito B: Kuika lembo lalikulu ndi zopumila m'ziganizo.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi kaikidwe ka lembo lalikulu ndi zopumila m'ziganizo.
- Patsani aphunzi ziganizo zomwe zilibe malembo aakulu ndi zopumila ndipo muwauze kuti aikemo.

II. Aphunzi:

- Aonetsetse kaikidwa ka lembo lalikulu ndi copumila.
- Aike malembo aakulu ndi zopumila mziganizo.

Citsanzo

1. **atate agwila mfuko**
2. **ana akudya magwawa**

Muyeso Woyembekezeleka: Ziganizo zaikidwa zopumila moyenela.

Mutu Waung'ono 2: Ziganizo

Lambulo: Mutu waung'ono uyu uzaona pakulemba ziganizo zathunthu.

Luso Lapadela: Kulemba ziganizo zathunthu.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Chati ya ziganizo, mafulashi khadi aziganizo

Mau Ofunikila Kudziwa: ziganizo, zathunthu

Mfundo zophunzitsa:

- Kuphunzitsa kulemba ziganizo zathunthu.

Nchito: Kulemba ziganizo zathunthu

I. **Mphunzitsi:**
    - Onetsani aphunzi malembedwe aziganizo zathunrhu.
    - Funsani aphunzi kuti alembe ziganizo zathunthu m'magulu ao.

II. **Aphunzi:**
    - Aone malembedwe aziganizo zathunthu.
    - M'magulu ao, alembe ziganizo zathunthu.

Muyeso Woyembekezeleka: Ziganizo zathunthu zalembedwa moyenela.

Mutu Waung’ono 3: Nkhani yosavuta

Ciyambi: Mutu waung'ono uyu uzaona pakutsilizitsa ziganizo za nkhani ndi kupanga nkhani yasabvuta.

Luso Lapadela: Kulemba nkhani yosabvuta

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Chati ya nkhani, buku la nkhani.

Mau Ofunikila Kudziwa: yosabvuta, kupanga,,

Mfundo zophunzitsa:

- Kuphunzitsa kasilizidwe ka ziganizo za nkhani.
- Kuphunzitsa kapangidwe ka nkhani yosabvuta.

Nchito A: **Kusilizitsa ziganizo za nkhani.**

I. Mphunzitsi:

- Aonetse katsilizidwe ka ziganizo za nkhani.

Citsanzo:

Dzulo amai anapita kumunda.

Popita ananyamula……

Atafika kumunda……

- Aonetsenso kapangidwe ka nkhani yosabvuta.
- Auze aphunzi kuti apange nkhani yosabvuta m'magulu ao.

II. Aphunzi:

- Aone katsilizidwe ka ziganizo za nkhani
- Aonenso kapangidwe ka nkhani yosabvuta
- Apange nkhani yosabvuta m'magulu ao.

Muyeso Woyembekezeleka: Nkhani yapafupi yapangidwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kuzindikila zomupila, kulemba ziganizo zathunthu ndi kupanga nkhani yapafupi.

CAPAMUTU 2: KUFOTOKOZA MAONEKEDWE A ZINTHU

**Ciyambi:** Mutu uyu uzaona pa kufotokoza za maonekedwe a zinthu, mau ogwilitsa nchito pakufotokoza za zinthu zochulidwa, kuzindikila mvekelo, ubale wa lembo ndi mvekelo, masilabe, mau, kuwelenga mofulumila, matanthauzo a mau, mvetso, malembedwe ndi cimangilizo.

CIGAWO: KUMVETSELA NDI KULANKHULA

MUTU: Kufotokoza Za Maonekedwe

Mutu Waung'ono: Zinthu

Luso Lapadela: Fotokozani maonekedwe a zinthu.

**Mau Ofunika Kudziwa:** Maonekedwe, kufotokoza, zinthu.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Chati yoonetsa zinthu zosiyana-siyana, zinthu zooneka komanso zogwilika ndi manja.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuphunzitsa kulemba mau omwe agwilitsidwa nchito pofotokoza za zinthu.
- Kuphunzitsa kugwilitsa nchito mau ozindikilidwa kuti afotokoze za zinthu.

**Nchito A: Kulemba mau omwe agwilitsidwa nchito pofotokoza za zinthu.**

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti alembe mau omwe amagwilitsidwa nchito pofotokoza za maonekedwe a zinthu (cacikulu, cacifupi, cacing'ono, cacitali).

- Afunse aphunzi kuti achulenso utoto wa zinthuzo (fiira, dwambe, yela, cikasu, mtambo).
  Citsanzo:
  Mnyamata wa mtali.
  Nyumba yofiila.

II. Aphunzi:

- Alembe mau omwe amagwilitsidwa nchito pofotokoza za maonekedwe a zinthu.
- Achulenso utoto wa zinthu zomwe zilikufotokozedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Mau ogwilitsidwa nchito pofotokoza maonekedwe a zinthu achulidwa moyenela.



Nchito B: Kugwilitsa nchito mau azindikilidwa kufotokoza za maonekedwe a zinthu.

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti azindikile mau ogwilitsa nchito pofotokoza za maonekedwe a zinthu mu sukulu lao komanso kunyumba.
- Auze aphunzi kuti afotokoze maonekedwe a zinthu za mu sukulu monga;
  Kalasi, bolodi, desiki, buku
- Uzani aphunzi kuti afotokozenso maonekedwe a zinthu za ku nyumba monga;
  Nyumba yao, ziweto, mipando ndi zina zotele.

II. Aphunzi:

- Azindikile mau ogwilitsa nchito pofotokoza za maonekedwe a zinthu.
- Afotokoze maonekedwe a zinthu za mu sukulu lao .
- Afotokozenso maonekedwe a zinthu za kunyumba kwao.

Muyeso Woyembekezeleka: Mau ozindikilidwa adwilitsidwa nchito moyenela pofotokoza za zinthu.

Nchito C: Kusewela masewela ofotokoza zinthu.

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti asewele masewela ofotokoza za maonekedwe a zinthu zosiyana-siyana.

II. Aphunzi:

- Asewele masewela ofotokoza za maonekedwe a zinthu zosiyana-siyana (masewela monga; I spy, who am I?).

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela ofotokoza maonekedwe a zinthu aseweledwa moyenela.

Mwacidule: Aphunzi aphunzila kufotokoza maonekedwe a zinthu zosiyana-siyana.

CIGAWO: KUWELENGA

MUTU: KUZINDIKILA MASILABE

Mutu Waung'ono 1: Kuzindikila masilabe opangidwa ndi**; ii-, uu-, ng- , bv-**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse masilabe amvekelo imodzi mpaka onse owonetsedwa pa mwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila masilabe bva, bve, bvi, bvo, bvu.

Ciyambi: Cigawoci cizaona pa kuzindikila masilabe mu mau okambidwa. Mau awa azathandiza aphunzi kuzindikila kuti mau ali ndi masilabe, ndipo azazindikila mvekelo pa silabe lililonse.

Luso lapadela: Kuzindikila ndi kusintha masilabe.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Fulashi khadi, silabiki chati.

Mau Ofunika Kudziwa: Masilabe, mvekelo, vawelo.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuzindikila masilabe mu mau okambidwa.
- Kusewela masewela owelenga masilabe.
- Kusewela masewela opanga mau.

Nchito A: Kuzindikila masilabe m'mau olankhulidwa.

I. Mphunzitsi:

- Alankhule mau ndi kuuza aphunzi masilabe omwe alimo.
- Anene mau ndi kufunsa aphunzi kuzindikila masilabe alimo.

Citsanzo:

1. Ng'o/mbe ◂ ng'o/mbe
2. Bvuula ▾ bvu/u/la

II. **Aphunzi:**

- Amvetsele mau olankhulidwa.
- Azindikile masilabe m'mau olankhulidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe m'mau olankhulidwa azindikilidwa moyenela.

Nchito B: Kusewela masewela akuwelenga masilabe poomba m'manja.

I. Mphunzitsi:

- Aonetse aphunzi kacitidwe ka masewela akuwelenga masilabe poomba m'manja.

Auze aphunzi kuti acite masewela akuwelenga masilabe poomba m'manja.

II Aphunzi:

- Aonelele kacitidwe ka masewela akuwelenga masilabe poomba m’manja.
- Asewele masewela akuwelenga masilabe poomba m’manja.

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela owelenga masilabe aseweledwa moyenela.

Nchito C: Kupanga mau olankhulidwa pogwilitsa nchito masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Phunzitsani kapangidwe ka mau pogwilitsa nchito masilabe.
- Uzaze aphunzi kuti apanga mau olankhulidwa pogwilitsa nchito masilabe m’magulu ao.

II. Aphunzi:

- Aone kapangidwe ka mau olankhulidwa pogwilitsa nchito masilabe.
- Apange mau olankhulidwa m’magulu ao pogwilitsa nchito masilabe.

Muyeso Woyembekezeleka: Mau olankhulidwa apangidwa moyenela pogwilitsa nchito masilabe.

Nchito D: **Kusewela masewela opanga mau (Kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe)**

I. **Mphunzitsi:**

- Onetsani aphunzi masewela akupanga mau pa kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe.
- Ikani aphunzi m’magulu kuti acite masewela akupanga mau pa kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

II. **Aphunzi:**

- Aone masewela a kapangidwe ka mau pa kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe.
- Acite masewela a kupanga mau pa kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

Zitsanzo:

Kusinthanitsa

i. **Ng'o**na **bvi**na.

ii. **Ng'a**mbe **ng'o**mbe.

Kucotsa

i. **Ng'a**mbako mbako

ii. **Ma**bvuto bvuto

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela opanga mau aseweledwa moyenela.

Mwacidule: Aphunzi a zindikila masilabe ndi kucita masewela akuomba m'manja. Acitanso masewela opanga mau kugwilitsa nchito masilabe kucokela ku mau okambidwa.

MUTU 2: Kulumikiza Makonsonanti ndi Mavawelo

Mutu waung'ono 1: Masilabe

Lambulo: Mutu waung'ono uyu uzaona pa kupanga masilabe kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo.

Luso Lapadela: Kulumikiza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

Mau Ofunikila Kudziwa:

- Makonsonanti, mavawelo, masilabe, kulumikiza.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuphunzitsa kulumiza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

- Kuwelenga silabiki chati .
- Kusankha masilabe mu mau.
- Kucotsa malembo mu mau ndi kupanga mau atsopano.

Nchito A: Kulumikiza makonsonant ndi avawelo kupanga masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Sonyezani molumikizila makonsonanti ndi mavawelo popanga masilabe.

Citsanzo: b/ii **bii**, ph/ ii **phii**, f /ii **fii.**

- Ikani aphunzi m'magulu apange masilabe pogwilitsa nchito vawelo 'ii' ndi mvekelo /s/, /b/, /bv/, /f/.
- Uzani aphunzi kuti awelenge masilabe yomwe apanga monga awa; sii, bii, bvii,fii.

II. Aphunzi:

- Alumikize makosonanti ndi mavawelo
- M'magulu apange masilabe pogwilitsa nchito mvekelo /bv/ ndi mavawelo.
- Awelenge masilabe omwe apangidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe apangidwa moyenela kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo

Nchito B: Kuwelenga chati ya masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Asonyeze aphunzi kawelengedwe ka chati ya masilabe.
- Akumbutse aphunzi njila zosiyana-siyana zowelengelamo chati ya masilabe monga; kucokela kudzanja la manzele kupita ku dzanja la manja ndi kucokela kumwamba kutsikila pansi.

- Awelenge chati ya masilabe m'magulu ao.

II. Aphunzi:

- Aonelele kawelengedwe ka chati ya masilabe.
- Akumbukile mawelengedwe ocokela kudzanja la manzele kupita ku dzanja la manja ndi kucokela kumwamba kutsikila pansi.
- M’magulu ao awelenge silabiki chati m’njila zosiyana-siyana monga;
    1. Kucokela kudzanja la manzele kupita kudzanja la manja.
    2. Kucokela kumwamba kutsikila pansi.
    3. Kuwelenga mwa zigi-zagi komanso mosakaniza.

Muyeso Woyembekezeleka: Silabiki chati yawelengedwa moyenela.



Nchito C: Kusankha masilabe

I. Mphunzitsi:

- Asonyeze mosankhila masilabe kucokela m'mau.
- Afunse aphunzi kuti akhale awili-awili ndipo asankhe masilabe kucokela m'mau opelekedwa.
  Citsanzo: bvuula, bviika

II. Aphunzi:

- Aphunzile mosankhila masilabe kucokela ku mau.
- Akhale awili-awili ndipo asankhe masilabe kucokela ku mau opatsidwa.
  Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe asankhidwa moyenela.



Nchito D: Kusintha masilabe

I. Mphunzitsi:

- Auze aphunzi kuti awelenge mau opelekedwa.
- Aonetse mosinthanitsila malembo.
  Citsanzo: Bvi**n**a ◥ bvi**k**a ‘
- Auze aphunzi kuti asinthanitse lembe zocita posinthanitsa malembo.

II. Aphunzi:

- Awelenge mau opelekedwa.
- Aphunzile mosinthanitsila malembo kupanga mau atsopano.
- Alembe zocita posinthanitsa malembo.

Muyeso Woyembekezeleka: Malembo asinthanitsidwa moyenela.



Nchito E: Kulumikiza makonsonanti a mvekelo zosiyana ndi mavawelo popanga masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Aonetse aphunzi molumikizila makonsonanti a mvekelo zosiyana ndi mavawelo kupanga masilabe.
  Citsanzo:
  -bv/a◥ bva
  -bv/i ▼ bvi.
- Afunse aphunzi kukhala awili-awili kuti ayeselele kulumikiza makonsonanti a mvekelo zosiyana ndi mavawelo kupanga masilabe.

II. **Aphunzi:**

- Aone molumikizila makonsonanti a mvekelo zosiyana popanga masilabe.
- Akhale awili-awili kuti ayeselele kulumikiza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.
  Muyeso Woyembekezeleka: Makonsonanti a mvekelo zosiyana-siyana ndi mavawelo alumikizidwa moyenela.

Mutu waung’ono 2: Mau

Lambulo: Mutu uyu uzaona pakulumikiza masilabi kupanga mau, kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano, kuzindikila masilabe mu mau ndi kuwelenga masilabe.

Luso lapadela: Kulumikiza masilabe popange mau.

Zipangizo zophunzila ndi zophunzilila: Silabiki chati, mafulashikhadi.

Mau ofunika kudziwa: Makonsonanti, mavawelo, masilabe, kulumikiza.

Mfundo zophunzitsa:

- Kulumikiza masilabe kupanga mau
- Kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano
- Kudzindikila masibe mu mau
- Kupenda silabe mu mau

Nchito A: Kulumikiza masilabe kupanga mau

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi mapangidwe a mau kugwilitsa nchito masilabe.

Zitsanzo: Bi/i ▼ bii

Bvi/ni/ki/la ▼ bvinikila

- Funsani aphunzi kuti apange mau kugwilitsa nchito masilabe opatsidwa m'magulu ao.
- Uzani aphunzi kuti azindikile nambala ya masilabe m’mau opatsidwa.

  Zitsanzo:

  1. Bii 2
  2. Bviika 3
  3. Bvindikila 4

II. Aphunzi:

- Aphunzi aone kapangidwe ka mau pogwilitsa nchito masilabe.
- Apanga mau kugwilitsa nchito masilabe.
- Azindikile nambala ya masilabe m'mau.

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe alumikizidwa moyenela kupanga mau.

Nchito B: Kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

I. Mphunzitsi:

- Aphunzitse kasinthidwe ka masilabe kupanga mau.

Kusintha masilabe kupanga mau

- Bvika bvina (cotsani /bvi/ ikani /bvu/)

- Aonetsa aphunzi kapangidwe ka mau pocotsela masilabe.

Kucotsa masilabe kupanga mau.

ii. Kubviika bviika (cotsani silabe / ku/)

- Ikani aphunzi m’magulu kuti apanga mau pa kusintha ndi kucotsa masilabe.

II. Aphunzi:

- Aphunzile kasinthidwe ka masilabe kupanga mau.
- Aonelele kapangidwe ka mau pa kusintha masilabe.
- M’magulu ao apanga mau atsopano pa kusintha ndi kucotsa masilabe.

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe asinthanitsidwa moyela.

Nchito C: Kuzindikila masilabe m'mau.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani zithunzi kwa aphunzi.
- Funsani aphunzi kuti afotokoze zomwe aona pa zithunzi monga;

- mnyamata a kubvika nyumba,
- mai aku bviika zobvala.

- Uzani aphunzi kuti azindikile masilabe m'mau omwe apelekedwa.

- kubvika

- bviika

II. Aphunzi:

- Aone zithunzi zomwe zapelekedwa.
- Afotokoze zomwe aona pa zithunzi.
- Azindikile masilabe mu mau omwe apelekedwa.

  -kubvika ku/bvi/ka

  -bviika → bvi/i/ka

  Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe mu mau azindikilidwa moyenela.



Nchito D: kuwelenga masilabe

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi momwe angawelengele masilabe m'mau.
- Uzani aphunzi kuti awelenge nambala ya masilabe mu mau awa:

II. Aphunzi:

- Aphunzile momwe angawelengele masilabe m'mau.
- Awelenge nambala ya masilabe mu mau opelekedwa.

  Zitsanzo:

  1. Bvala 2
  2. Wa/bva/la 3

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga masilabe kwacitidwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kulumikiza masilabe kupanga mau, kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano, kuzindikila masilabe mu mau ndi kuwelenga masilabe.

MUTU 3: KUWELENGA MOFULUMILA

Luso Lapadela 1: Kuwelenga mau mokuwa ndiponso molungama

Nchito : Kuwelenga mau

I. Mphunzitsi:

- Akambe mau.
- Alembe mau pa bolodi.
- Auze aphunzi kuti awelenge mau awa;
  -siila, cofiila, ng'ombe, kuula, bvuta.

II. Aphunzi:

- Amvetsele mau okambidwa
- Awelenge mau mokuwa m'magulu ao.
- Awelenge mau opatsidwawo ndi machulidwe oyenela.

  Zocita:

  Welengani mau awa mokuwa komanso mofulumila awili-awili;

  1. Bvundula
  2. Bviika

  Muyeso woyembekezeleka: Mau awelengedwa moyenela

Luso Lapadela: Kuwelenga nkhani mokuwa pozindikila kachulidwe ka mau

Nchito A: **Kuwelenga ndi kumvetsetsa ziganizo.**

I. Mphunzitsi:

- Onetsani chati ya ziganizo kwa aphunzi.
- Funsani aphunzi kuti awelenge ziganizo momvetsetsa m'modzi-m'modzi pa nthawi .
- Uzani aphunzi kuti alembe m'mabuku ao.

Zitsanzo:

-Malita wabvala delesi lofiila.

II. Aphunzi:

- Aone chati ya ziganizo yoonetsedwa ndi mphunzitsi.
- Awelenge ziganizo m'modzi-m'modzi pa nthawi momvetsetsa ndipo ayankhe mafunso.
- Alembe ziganizo m'mabuku ao.

Muyeso Woyembekezeleka: Ziganizo zawelengedwa ndiponso zayankhidwa moyenela.



Nchito B: Kuwelenga nkhani ya ziganizo za pakati pa ziwili ndi zisanu. (Kuwelenga kwa gulu, kolondola mphunzitsi komanso kwa awili-awili).

I. Mphunzitsi:

- Awelenge nkhani yaifupi ili pa chati kuti aphunzi amvetsele.
- Auze aphunzi kuti ayeselele kuwelenga nkani yomwe yawelengedwa ndi mphunzitsi.

Nkhani:

Fumbani anafuna kupita ku msika. Asanapite anaganizila zotenga ng'ombe zake ndi ngolo. Fumbani anagula ufa, malaya ofiila ndi bulangeti.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani.

- Ayeselele kuwelenga nkhani.

Muyeso Woyembekezeleka: Nkhani ya ziganizo zifupi-zifupi za pakati pa ziwili ndi zisanu zawelengedwa moyenela.



Nchito C: Kuwelenga nkhani zili ndi mvekelo zosiyana-siyana komanso zolumikizidwa.

I. Mphunzitsi:

- Pelekani mabuku omwe ali ndi nkhani zosiyana-siyana.
- Uzani aphunzi kuti awelenge nkhani.

II. Aphunzi:

- Alandile mabuku ali ndi nkhani zowelenga.
- Awelenge nkhani payekha-payekha.

Muyeso Woyembekezeleka: Nkhani za mvekelo zosiyana-siyana komanso zolumikizidwa zamvetsedwa moyenela.



Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kuwelenga masilabe ndi mau mokuwa ndiponso mofulumila. Wayangananso pakuwelenga nkhani ya ziganizo zifupi-zifupi za pakati pa ziwili ndi zisanu.

MATANTHAUZO A MAU

MUTU: MAINA

Mutu waung'ono: Maina Osaculukitsidwa ndi Oculukitsidwa.

Lambulo: Mutuyu uzaona pa kupanga maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa. Kulinganiza komanso kusewela masewela a maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa.

Luso Lapadela: Kupanga maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.

Mau Ofunika Kudziwa: Maina, maina oculukitsidwa, maina osaculukitsidwa.

Mfundo Zophunzitsa:

Kuphunzitsa kupanga maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila:

Mafulashi khadi, machati ndi zipangizo zogwilika.

Nchito A: Kupanga maina oculukitsidwa kucoka ku osaculukitsidwa

I. Mphunzitsi:

- Funsani aphunzi kuti apeleke zitsanzo za maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.
- Uzani aphunzi kuti apange maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.
- Auze aphunzi kuti apangenso maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

Zitsanzo:

MAINA OSACULUKITSIDWA	MAINA OCULUKITSIDWA
Bvuto	Mabvuto

II. Aphunzi:

- Apeleke zitsanzo za maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.
- Apange maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.
- Apangenso maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Maina oculukitsidwa apangidwa moyenela kucokela ku maina osaculukitsidwa.

Nchito B:

Kupanga maina osaculukitsidwa kucoka ku maina oculukitsidwa.

I. Mphunzitsi:

- Afunse aphunzi kuti achule maina osaculukitsidwa.
- Auze aphunzi kuti apeleke zitsanzo za maina osaculukitsidwa kucokela kuli oculukitsidwa.

MAINA OCULUKITSIDWA	**MAINA OSACULUKITSIDWA**
Cobvala	Zobvala

- Auze aphunzi kuti apange maina osaculukitsidwa kucokele ku maina oculukitsidwa.

II. Aphunzi:

- Achule maina osaculukitsidwa.
- Apeleke maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.
- Apange maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Maina osaculukitsidwa apangidwa moyenela.

Nchito C: **Kulinganiza maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.**

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa pa chati.
- Uzani aphunzi kuti aculukitse maina osaculukitsidwa.
- Funsani aphunzi kuti alinganize maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.

Zitsanzo:

1. Bvuto mabvuto

2. Cobvala zobvala

II. Aphunzi:

- Aone maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa pa chati.
- Aculukitse maina osaculukitsidwa.
- Alinganize maina oculukitsidwa nd osaculukitsidwa.

Zocita:

Linganizani maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa

1. Bvumbwe asing'ang
2. Bvuto abvumbwe
3. Sing'anga mabvuto

Muyeso Woyembekezeleka: Maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa alinganizidwa moyenela.



Nchito D: Kusewela masewela a maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi kaseweledwe ka masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.
- Sewelani pamodzi ndi aphunzi masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.
- Uzani aphunzi kuti asewele masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa pogwilitsa nchito ma fulashi khadi m'magulu ao. (Plural bingo ndi plural scavenger).

II. Aphunzi:

- Aonelele kaseweledwe ka masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.
- Asewele pamodzi ndi aphunzitsi masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.
- Asewele masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa m'magulu ao.

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa aseweledwa moyenela.

**Mwacidule:** Phunziloli laphunzitsa aphunzi kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa komanso maina oculukitsidwa kucokela ku osaculukitsidwa.

MVETSO

MUTU 1: KUMVETSELA NKHANI.

Mutu Waung'ono 1: Ganizo Leni-Leni.

**Lambulo:** Mutu uyu uzaona pa kumvetsela nkhani ndi kupeleka maganizo pa zomwe zamveka pa nkhaniyo.

Luso Lapadela: Kuzindikila ndi kupeleka ganizo leni-leni la uthenga womwe iwo amva.

**Mau Ofunika Kudziwa:** Mvetselo, nkhani, mvetso, maganizo.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuphunzitsa m'mene aphunzi angapelekele maganizo pa nkhani yomwe amva.
- Kuwelenga nkhani kwa aphunzi ndi kuwafunsa mafunso mwakulakhula cabe.
- Kuuza aphunzi kuti apeleke maganizo kulingana ndi zomwe amva.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Makhadi a ziganizo, mabuku, mafulashi khadi.

**Nchito A: Kuzindikila ndi kupeleka ganizo leni-leni la uthenga womwe amva.**

I. Mphunzitsi:

- Awelenge nkhani kwa aphunzi ndi kuwafunsa mafunso mwakulakhula cabe.
- Auze aphunzi kuti apeleke maganizo ao kulingana ndi zomwe amva.

II. Aphunzi:

- Amvetsele khani yowelengedwa ndi aphunzitsi ndipo ayankhe mafunso.
- Apeleke maganizo ao kulinga ndi zomwe amva.

Muyeso Woyembekezeleka: Ganizo leni-leni lazindikilidwa ndipo la nenedwa moyenela.

 **Nchito B: Kufupikitsa Uthenga.**

I. Mphunzitsi:

- Awelenge kapena afotokoze nkhani kwa aphunzi.
- Afunse aphunzi kuti anene uthenga omwe amva mnkhani.
- Auze aphunzi kuti afupikitse uthenga mwakujambula zithunzi zofotokoza uthenga omwe amva.

II. Aphunzi:

- Aone zili pa cithunzi.
- Anene zomwe aona pa cithunzi.
- Alembe uthenga wopatsidwa mwakufupikitsa.

Muyeso Woyembekezeleka: Uthenga wafupikitsidwa moyenela.

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa kumvetsela nkhani ndi kupeleka maganizo pa nkhani yomwe yawelengedwa komanso kufupikitsa uthenga.

Mutu waung'ono 2: Coona ndi Lingalilo.

 **Lambulo:** Mutu uyu uzaona pa kuzindikila lingalilo ndi coonadi mnkhani.

Luso Lapadela: Kusiyanitsa pakati pa coona ndi lingalilo.

Mau Ofunika Kudziwa: Coona, lingalilo, kusiyanitsa.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Mabuku, makhadi.

Nchito A: Kuzindikila Lingalilo Mu Nkhani.

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti mudzawawelengela nkhani ndipo ayenela kumvetsetsa
- Kambani kapena welengani nkhani kwa aphunzi ndipo muonetse mozindikilila lingalilo cabe mnkhaniyo.
- Kambani kapena welengani nkhani zina ndipo muwauze aphunzi kuti azindikile lingalilo cabe mnkhaniyo.

II. Aphunzi:

- Amvetsele nkhani ndipo aonelele mozindikilila lingalilo cabe m'nkhani.
- Awelenge ndi kumvetsele ku nkhani
- Azindikile lingalilo pokambilana m'magulu.

Muyeso Woyembekezeleka: Malingalilo m’nkhani yazindikilidwa moyenela.

Nchito B: Kuzindikila Coona M’nkhani.

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani kwa aphunzi ndipo muonete mozindikilila zoona za nkhani.
- Pelekani mabuku a nkhani kwa aphunzi kuti awelenge m'magulu ao ndipo azindikile coona mnkhaniyo.

II. Aphunzi:

- Alandile mabuku ali ndi nkhani zowelenga.
- Awelenge nkhani m'magulu ndipo azindikile coona mnkhaniyo.

Muyeso Woyembekezeleka: Coona casiyanitsidwa kulingalilo moyenela.

 **Mwacidule:** Phunziloli linali kuona pa kuzindikila lingalilo ndi coonadi mnkhani.

MUTU 2: MVETSO YA KUWELENGA

Mutu Waung'ono: Zoona Za Nkhani

 **Lambulo:** Mutu uyu uzana pa kupeleka uthenga wonenedwa m'nkhani yaifupi yopatsidwa.

Luso Lapadela: Kupeleka uthenga wonenedwa m'nkhani yaifupi yopatsidwa.

 **Mau Ofunika Kudziwa:** Uthenga, nkhani, ifupi.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuphunzitsa momwe aphunzi angapelekele uthenga wonenedwa m'nkhani.
- Momwe angafotokozele zomwe zawelengedwa.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Mabuku, makhadi aziganizo.

 **Nchito A: Kufotokoza Zomwe Zawelengedwa M'nkhani.**

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani kwa aphunzi.
- Phunzitsani aphunzi momwe angafotokozele zomwe zawelengedwa mnkhani.
- Patsani aphunzi nkhani kuti awelenge ndipo afotokoze zomwe zawelengedwa.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani yowelengedwa.
- Aphunzile momwe angafotokozele zomwe zawelengedwa mnkhani.
- Awelenge ndipo afotokoze zomwe zawelengedwa mnkhani.

  Muyeso Woyembekezeleka: Uthenga wawelengedwa ndipo wafotokozedwa moyenela.



Nchito B: Kuyankha Mafunso Kucokela Ku Zomwe Zawelengedwa.

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani kwa aphunzi.
- Auze aphunzi kuti awelenge nkhaniyo m'magulu ao.
- Funsani aphunzi kuti ayankhe mafunso kucokela ku zomwe awelenga paokha (Nciani? Ndani? N'kuti? Liti? Zinacitika bwanji?).

II. Aphunzi:

- Amvetsele poimwe aphunzitsi akuwelenga.
- Awelenge nkhani m'magulu ao.
- Ayankhe mafunso kucokela ku zomwe awelenga.

  Muyeso Woyembekezeleka: Mafunso ayankhidwa moyenela.



Nchito C: Kufotokoza Molunjika Momwe Zinthu Zinacitikila Mu Nkhani.

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani kwa aphunzi ndipo mufotokoze molunjika momwe zinthu zinacitikila mnkhani.
- Patsani aphunzi nkhani yina kuti awelenge m'magulu ao
- Funsani aphunzi kuti afotokoze molunjika momwe zinthu zinali kucitikila mu nkhani.

II. Aphunzi:

- Amvetsela pomwe aphunzitsi akuphunzitsa mawelengedwe ndi mafotokozedwe azocitika mnkhani.
- Awelenge nkhani yopatsidwa m'magulu ao.
- Afotokoze molunjika momwe zinthu zinacitikila mnkhani.

Muyeso Woyembekezeleka: Zocitika mu nkhani zafotokozedwa molunkika bwino.

**Mwacidule:** Aphunzi aphunzila kuwelenga ndi kufotokoza uthenga wowelengedwa kapena wokambidwa mnkhani.

B. KULEMBA.

MUTU: MALEMBEDWE

Mutu Waung'ono 1: Kupanga Lembo

**Lambulo:** Mutuyu uzaona pa kapangidwe ka lembo.

Luso Lapadula: Kulemba lembo.

**Mau Ofunika Kuziwa:** Malembedwa, lembo, kujambula.

Mfundo Zophunzitsa: Kuphunzitsa kapangidwe ka malembo osiyana-siyana.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Mafulashi khadi, mabuku, silabiki chati.

**Nchito A: Kujambula Malembo**

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi kalembedwa ka lembo koyenela.
- Funsani aphunzi m'modzi-m'modzi kuti ayeselele kulemba malembo opatsidwa pa bolodi kapena padothi.
- Patsani aphinzi malembo ndipo muwauzse kuti ajambule m'mabuku ao.

II. Aphunzi:

- Aonelele kalembedwe ka lembo koyenela.
- Ayeselele kulemba malembo opatsidwa pa bolodi ndi padothi.
- Ajambule nchito malembo apatsidwa m'mabuku ao.

Muyeso Woyembekezeleka: Malembo alembedwa moyenela.



Nchito B: Kulemba Malembo

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi m’mene malembo alembedwela m’mizele.
- Funsani aphunzi kuti ayeselele kulemba malembo yalembedwa pa bolodi.
- Uzani aphunzi kuti alembe malembo paokha m’mabuku ao.

Zitsanzo:

Malembo a micila itali-itali yokwezeka…….d, b ,k ,h.

Malembo a micila yotsikila pansi……f, g, h, j

II. Aphunzi:

- Aonelele m’mene malembo alembedwela m’mizele.
- Ayeselele kulemba malembo yolembedwa pa bolodi.
- Alembe malembo paokha m’mabuku ao.

Muyeso Woyembekezeleka: Malembo alembedwa moyenela.

Mutu Waung'ono 2: Malembedwe okhazikika

 **Lambulo:** mutu uyu uzayangana pa malembedwe okhazikika ndi kuzindikila pipata m'mau.

Luso lapadela: Kulemba mau m'malembedwe okhazikika.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Silabiki chati, mafulashi khadi, makhadi a ziganizo, mabuku.

 **Mau Ofunikila Kudziwa:** kulemba, kukhazikika, lembo, malembedwe.

Mfundo zophunzitsa:

- Uzani aphunzi kuti malembedwe ali ndi malamulo omwe afunika kulondoledwa polemba.

Fotokozani za lamulo lamicila yopita kumwamba komanso micila obwela pansi mumalembedwe

 **Nchito: Kujambula mau m'malembedwe okhazikika.**

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca malembedwe a mau polondola malembedwe okhazikika ndiponso polemekeza micila opita kumwamba komanso pansi.
- **Citani cimodzi-modzi ndi mvekelo zina.**

II. Aphunzi:

Alembe mau molondola bwino zomwe aphunzitsidwa pakalembedwe ka malembo.

Zocita:

1. Nkhono.

2. Nkhumba.

3. Nkhani

Muyeso Woyembekezeleka: Mau alembedwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pakalembedwe ka mau kokhazikika.

MUTU 1: Malembedwe

Mutu Waung'ono 3: Mipata a mau.

Lambulo: Mutu uyu uzaona pakusiya mipata m'mau.

Luso lapadela: kusiya mipata m'mau.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Fulashi khadi, makhadi a ziganizo, mabuku.

Mau Ofunikila Kudziwa: kulemba, kukhazikika, lembo, mipata.

Mfundo zophunzitsila:

- Uzani aphunzi kuti malembedwe abwino aziganizo ayenela kukhala ndi mipata pakati opa mau.
- Fotokozaninso za lamulo lamicila yopita kumwamba komanso micila obwela pansi mumalembedwe.

Nchito: Kujambula ziganizo m'malembedwe okhazikika.

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo cakuzindikila mipata m'ziganizo zomwe zilibe mipata m'malembedwe okhazikika.

- Funsani aphunzi kuti ayeselele kulemba ziganizo zopatsidwa zomwe zilibe mipata m'magulu ao.
- Patsani aphunzi ziganizo zomwe zilibe mipata ndipo muwauza kuti azindikile mipata paokha polemba ziganizozo m'[mabuku ao.

II. Aphunzi:

- Aone kasiyidwe ka mipata m'ziganizo zomwe zilibe mipata m'malembedwe okhazikika.
- Ayeselele kulemba ziganizo zopatsidwa zomwe zilibe mipata m'magulu ao.
- Azindikile mipata paokha polemba ziganizozo m'mabuku ao.

Muyeso Woyembekezeleka: Ziganizo zajambulidwa ndipo mipata asiyidwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa malembedwe okhazikika a lembo, mau ndi kuzindikila mipata ya mau m'ziganizo.

MUTU 2: Cimangilizo
Mutu Waung'ono: Kujambula.

Ciyambi: mutu uyu uzayangana pakujambula zinthunzi zomwe zidzapeleka uthenga yomangilizidwa pamodzi.

Luso lapadela: Kufotokoza malingalilo mwakujambula.
Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Phensulo, pepala, makileyoni.

Mau Ofunikila Kudziwa: zithunzi, uthenga, kujambula.

Mfundo zophunzitsila:

- Phunzitsani aphunzi kuti tingathe kufotokoza malingalilo pakujambula zomwe tiganiza.

Nchito: Kujambula zocitika popanga nkhani.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi majambulidwe azithunzi zomwe zingapange nkhani ataziona.
- Uzani aphunzi kuti ajambule zithunzi za zocitika popanga nkhani.
- Pelekani nkhani yomwe izathandiza aphunzi kujambula zithunzi kuti apange nkhani.

  NKHANI

  Tsiku lina, mwana wa mfumu anapita kumstinje kukasambila.

  Ali mkusambila anaona ng'ona ili kubwela kwa iye.

  Anagwidwa ndi mantha kuopa kuti angadyedwe.

  Mwamwai anatenga mwala ndi kupha nayo ng'ona.

II. Aphunzi:

- Aonelele majambulidwe a **zithunzi zomwe zingapange nkhani ataziona.
- Ajambule zithunzi za zocitika popanga nkhani.
- Alondole nkhani popanga zithunzi.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula zinthunzi zosonyeza nkhani kwacitika moyenela.

Mwacidule: Mutuyu unali kuona pakujambula zinthunzi zomwe zipeleka uthenga yomangilizidwa pamodzi.

CAPAMUTU 3: SEWELO

 **Ciyambi:** Cigawo ici cizaona pa kucita sewelo zosiyana siyana kulingana ndi zocitika ku nyumba ndi kusukulu. Cigawoci cizaonanso pa Kuwelenga, Mvetso komanso Kulemba. Izi zidzathandiza aphunzi muumoyo wao watsiku ndi tsiku.

CIGAWO 1: KUMVETSELA NDI KULANKHULA

MUTU 1: Sewelo

Mutu Waung'ono 1: Kusewela

 **Ciyambi:** Mutu uyu uzaona pa kucita sewelo. Sewelo lidzathandiza aphunzi kudziwa mau ambili omwe adzagwilitsa nchito mphunzilo la kuwelenga ndi kulemba. Sewelo lidzathandizanso aphunzi kuganiza mwakuya pokulankhula.

Luso Lapadela: Kutengako mbali kusewelo kugwilitsa nchito mau oyenela.

 **Mau Ofunika Kudziwa:** Sewelo, kusewela, kumvetsela.

Mfundo Zophunzitsila:

- Kupatsa aphunzi mutu umene adzacitila sewelo.
- Kufotokoza maseweledwe a sewelo.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila:

Mutu ofotokoza mfundo yasewelo, chati yowoonetsa mwana akulandila mphatso kucokela ku makolo ndi mphunzitsi.

 **Nchito: Kucita sewelo zosiyana siyana kulingana ndi zocitika ku nyumba ndi kusukulu.**

I. Mphunzitsi :

- Ikani aphunzi m’magulu
- Fotokozelani aphunzi tanthauzo la sewelo.
- Apatseni mfundo yomwe azagwilitsa nchito pocita sewelo lao. (Ena acite sewelo loonetsa zocitika kunyumba pomwe ena acite sewelo loonetsa zocitika ku sukulu)

Citsanzo

- Mwana ocita zabwino ku nyumba amakondweletsa makolo.
- Mwana ocita za bwino kusukulu akondweletsa aziphunzitsi.

II. Aphunzi:

- Akhale m'magulu.
- Amvetsele kutanthauzo la sewelo.
- Acite sewelo molingana ndi zigao zomwe apatsidwa.

Muyeso Woyembekezeleka

Masewelo acitidwa moyenela.

 **Mwacidule**

Mutuyu unali kuona pakucita sewelo zosiyana. Aphunzi aonetsa luso la kumvetsela ndi kulankhula pakucita sewelo.

CIGAWO 2: KUWELENGA

MUTU 1: Kuzindikila Masilabe

Mutu Waung’ono 1: Kuzindikila Masilabe opangidwa ndi; nz-, sh-, zy-, nkh- m’mau okambidwa.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pa mwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila masilabe nkha, nkhe, nkhi, nkho.

**Ciyambi:** Mutu uyu uzaona kuzindikila masilabe m'mau okambidwa, kusewela masewela akuwelenga masilabe omwe ali m'mau pakuomba m'manja, ndi masewela akupanga mau pa kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

Luso lapadela

Kuzindikila ndi kusewenzetsa masilabe.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila

Zithunzi, zida zogwilika.

**Mau Ofunika Kudziw**a

Masilabe, vawelo, mvekelo.

Mfundo zophunzitsa:

- Kuzindikila masilabe m'mau okambidwa.
- Kusewela masewela owelenga masilabe.
- Kusewela masewela osintha ndi kucotsa silabe kupanga mau atsopano.

**Nchito A: Kuzindikila masilabe m'mau okambidwa.**

I. Mphunzitsi :

- Onetsani cithunzi kapena zinthu zogwilika zili ndi mau ali ndi ali ndi masilabe opangidwa ndi /nkh/ mongan nkhuku.
- Fotokozani mazindikilidwe a masilabe mu liu monga khungu, khungwa, khasu, khoswe
- **Citanzo:**

nkhuku ili ndi zigawo ziwili - **nkhu** ndi **ku**(2).

- Zindikilani masilabe ali mu liu khungu pamodzi ndi aphunzi.

II. Aphunzi :

- Apenye zithunzi kapena zinthu zogwilika zili ndi mau ali ndi mvekelo /nkh/ monga nkhuku.
- Amvetsele kufotokoza mazindikilidwe a masilabe mu liu monga nkhuku.

Citanzo:

nkhuku ili ndi zigawo ziwili (2).

- Azindikile masilabe ali mu liu nkhuku mothandizidwa ndi Mphunzitsi.

Zocita:

Zindikilani masilabe m’mau okambidwa awa:

1. nkhuku– nkhu/ku
2. nkhuni- nkhu/ni

Muyeso Woyembekezeleka

Masilabe ali m'mau okambidwa azindikilidwa moyenela.



Nchito B: Kusewela masewela ozindikila masilabe m’mau poomba m’manja.

I. Mphunzitsi:

• Achule mau ali ndi mvekelo /nkh/.

Nkhata, nkhuni, nkhono.

- Sonyezani kuzindikila masilabe poomba m'manja.

- Uzani aphunzi awelenge masilabe ali m'mau poomba m'manja.

II. Aphunzi :

- Achule mau ali ndi mvekelo /nkh/.
- Amvetsetse mazindikilidwe a masilabe poomba m'manja.
- Awelenge masilabe ali m'mau poomba m'manja.

Zocita

Chulani mau ndi kupeza nambala ya masilabe poomba m'manja.

Nkhumba - kuomba kawili (2), ili ndi masilabe 2.

Nkhululu - kuomba katatu (3), ili ndi masilabe 3.

Nkhulungila - kuomba katatu (4), ili ndi masilabe 4.

Muyeso woyembekezeleka

Masewela ozindikila masilabe aseweledwa moyenela.



Nchito C: Kupanga mau okambidwa pogwilitsa nchito masilabe.

I. Mphunzitsi :

- Chulani masilabe nkha, nkhe, nkhi, nkho, nkhu ndi nda, ndo,
- Pelekani citsanzo cakapangidwe ka mau posewenzetsa masilabe.

Zitsanzo:

1. Nkha ndi nda apanga nkhanda.

2. Nkho ndi nda apanga nkhondo

- Uzani aphunzi apange mau ndi masilabe.Thandizani aphunzi alikupeza bvuto.

II. Aphunzi :

- Amvetsele kumachulidwe amasilabe nkha, nkhe, nkhi, nkho, nkhu ndi nda, ndo.
- Amvetsele ku citsanzo cakapangidwe ka mau posewenzetsa masilabe.

Zitsanzo

Nkha ndi nda apanga nkhanda.

Nkho ndi nda apanga nkhondo

Zocita

1. Nkha ndi ndo ipanga nkhando.
2. Nkhu ndi mba ipanga nkhumba
3. Nkho ndi no ipanga nkhono

Muyeso woyembekezeleka

Mau okambidwa kusewenzetsa masilabe apangidwa moyenela.

Nchito D: Kusewela masewela opanga mau pakucotsa ndi kusintha masilabe.

I. Mphunzitsi :

- Chulani mau awa ; nkhondo, nkhuni, nkhono.
- Uzani aphunzi kuti achule mau.
- Pelekani :citsanzo cakucotsa ndi kusintha masilabe.

Zitsanzo:

1. Nkhando – cotsani ndo ndi kuikapo nga liu tsopano ndi nkhanga.

I. Aphunzi:

- Amvetsele ku mau awa ochulidwa awa ; nkhondo, nkhuni, nkhono.
- Achule mau.

- Amvetsetse kucotsa ndi kusintha masilabe.
- Asinthe masilabe ndi kupanga mau atsopano.

Zocita

Sinthani silabe ndi kuikapo lina.

1. Nkhono – kucotsa no kuikapo silabe ko ipanga liu nkhoko.

Muyeso woyembekezeleka

Masewela opanga mau aseweledwa moyenela.

 **Mwacidule**: Aphunzi aphunzila kuzindikila mvekelo, kucita masewela a kuomba m’manja popanga masilabe ndi masewela opanga mau kugwilitsa nchito masilabe kucokela ku mau okambidwa.

KUWELENGA

MUTU 2: Ubale wa lembo ndi mvekelo.

Mutu Waung’ono 1: Masilabe

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse kupanga masilabe pa kulumikidza makonsonanti amodzi ndi mavawelo mpaka onse oonetsedwa pa mwambapa atatha.Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo.

 **Ciyambi:** Mutu uyu uzaona pa kupanga masilabe kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo, kuwelenga masilabe pa chati la masilabe, kusankha masilabe ndi kusintha malembo.

Luso Lapadela

Kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.



Mau Ofunika Kudziwa

Makonsonanti , mavawelo, masilabe, kulumikidza.

Zipangizo Zophunzitsila Ndi Zophunzilila

Silabiki chati, mafulashi khadi.

Mfundo zophunzitsa:

- kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.
- Kuwelenga silabiki chati.
- Kusankha masilabe mu mau.
- Kucotsa malembo mu mau ndi kupanga mau atsopano.



Nchito A: Kupanga masilabe kugwilitsa nchito makonsonanti ndi mavawelo.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani chati la ma consonant ndi mavawelo.

Makansonanti: nz, sh, zy, nkh

Mavawelo: a e i o u

- Welengani, aphunzi naonso awelenge.
- Onetsani aphunzi molumikidzila makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

Nkh kulumikidza ndi a ipanga liu nkha.

II. Aphunzi:

- Apenye pa chati la ma consonant ndi mavawelo.

Makansonanti: nz, sh, zy, nkh

Mavawelo: a e i o u

- Awelenge makonsonanti ndi mavawelo.
- Apenyelele malumikidzidwe a makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

Nkh kulumikidza ndi a ipanga liu nkha.

nkh/a nkha

Muyeso Woyembekezeleka

Masilabe apangidwa moyenela.



Nchito B : Kuwelenga chati yamasilabe.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani chati ya masilabe kwa aphunzi.
- Sonyezani kuwelenga masilabe ali pa chati.
- Uzani aphunzi awelenge masilabe.
- Thandizilani aphunzi kuwelenga m’magulu masilabe ali pa chati.

II. Aphunzi:

- Aone chati ya masilabe.
- Amvetsele kuwelenga masilabe ali pa chati.
- Awelenge masilabe.
- Awelenge m’magulu masilabe ali pa chati.

Zocita

1. Lembani masilabe osowa mwa awa.

Nkha nkhe ___nkho nkhu

2. Welengani masilabe ali pa 1

Muyeso woyembekezeleka

Chati ya masilabe yawelengedwa moyenela.

 **Nchito C : Kusankha masilabe.**

I. Mphunzitsi:

- Chulani mau ali ndi masilabe awili ndi atatu

Nkhuni (2), nkhalango (3)

- Welengani mau achulidwa.
- Muuze aphunzi kuti mau ali ndi zigawo. Zigawo izi ndi masilabe. Sonyezani kusankha masilabe m'mau tsopano.

Citsanzo

1. Nkhuni – nkhu/ni

2. Nkhalango – nkha/la/ngo

- Uzani aphunzi asankhe masilabe ndipo muwathandize kutelo.

II. Aphunzi:

• Achule mau ali ndi masilabe awili kapena atatu

Nkhuni – masilabe 2, nkhalango – masilabe 3

- Awelenge mau achulidwa.
- Amvetsele kuzofotokoza mphunzitsi kuti mau ali ndi zigawo. Zigawo izi ndi masilabe.
- Asankhe masilabe.

Zocita

1. lembani mau ali ndi masilabe atatu mwa awa;

nkhasi, nkhongono, nkhululu, nkhoko, nkhalango.

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe asankhidwa moyenela.

 **Nchito D : Kusintha masilabe**

I. Mphunzitsi:

- Achule mau monga nkhuni ndi nkhoko.
- Sonyezani aphunzi kusintha lembo.

Citsanzo:

Nkhuni – sinthani lembo la n ndi kuikapo lembo la l.

Liu likhala nkhuli.

- Uzani aphunzi asinthe lembo mu mau kupanga liu latsopano m'magulu. Thandizani aphunzi.

II. Aphunzi:

- Amvtsele kuchulidwa kwa mau.

Achule mau nkhuni ndi nkhoko.

- Amvetsetse kasinthidwe ka lembo ku citsanzo copelekedwa.
- Asinthe lembo m'mau kupanga liu latsopano m'magulu.

Zocita

Pezani mau atatu (3) ndi kusintha lembo kupanga mau atsopano.

1. Nkhoko sinthani lembo la k lili kufupi ndi kothela kuikapo n.

Liu latsopano ndi ___

2. Nkhando sinthani a kuikapo o liu latsopano _____

Muyeso Woyembekezeleka

Malembo asinthidwa moyenela.

 **Nchito E: Kulumikidza malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.**

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti monga nkh.
- Lumikidzani makonsananti ndi mavawelo kupanga silabe.

Citsanzo

nkh ndi a ipanga silabe nkha

- Uzani aphunzi apange masilabe kugwilitsa nchito makonsonanti nkh ndi mavawelo a e i o u. awili awili.

Zocita

Lumikidzani malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

a e i o u

nkh

Muyeso Woyembekezeleka

Malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti ndi mavawelo alumikizidwa ndi kupanga masilabe moyenela.

Cidule: Mutu uyu unali kuona pa kupanga masilabe kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo, kuwelenga masilabe pa chati la masilabe, kusankha masilabe ndi kusintha malembo.

B. KUWELENGA

MUTU 1: Kupanga Mau

Mutu Waung'ono 2: Mau

Ciyambi: Mutu uyu uzaona pa kulumikidza masilabe kupanga mau, kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano, kuzindikila masilabe mu mau ndi kuwelenga masilabe.

Luso Lapadela: Kulumikiza masilabe popanga mau.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Silabiki chati, mafulashi khadi

Mau Ofunikila Kudziwa: Makonsonanti, mavawelo, masilabe, kulumikidza

Mfundo zophunzitsa:

- Kulumikidza masilabe kupanga mau
- Kusinthanitsa ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano
- Kuzindikila masilabe m'mau
- Kuwelenga masilabe m'mau

Nchito A: Kusakaniza masilabe popanga mau

I. Mphunzitsi:

- Onetsani aphunzi mapangidwe a mau pogwilitsa nchito masilabe opangidwa ndi mvekelo /nkh/.

Citsanzo:

1. Nkho/ndo nkhondo

2. Nkhe/zyo nkhezyo

- Uzani aphunzi kuti apange mau m'magulu ao pogwilitsa nchito masilabe opangidwa ndi mvekelo /nkh/.
- Uzani aphunzi kuti apange mau paokha pogwilitsa nchito masilabe opangidwa ndi mvekelo /nkh/

II. Aphunzi:

Aonetsetse mapangidwe a mau pogwiltsa nchito masilabe opangidwa ndi mvekelo /nkh/

- Apange mau m'magulu ao pogwilitsa nchito masilabe opangidwa ndi mvekelo /nkh/.
- Apange mau paokha pogwilitsa nchito masilabe opangidwa ndi mvekelo /nkh/

Muyeso woyembekezeleka: Masilabe asakanizidwa moyenela popanga mau.



Nchito B: Kusinthanitsa ndi kucotsela masilabe

I. Mphunzitsi

- Onetsani aphunzi kasinthidwe ndi kacotsedwe ka masilabe popanga mau ena.
- Ikani aphunzi m'magulu ndipo muwauze kuti asinthe ndi kucotsa masilabe popanga mau.

Citsanzo

Kusintha

1. Nkhawa nkhanza

Kucotsa

2. Nkholoko Loko

- Funsani aphunzi kuti apange mau posinthanitsa ndi kucotsela masilabe m'mau.

II. **Aphunzi**

- Aonelele kasinthidwe ndi kacotsedwe ka masilabe popanga mau ena.
- Asinthe ndi kucotsa masilabe popanga mau.
- Apange mau posintha ndi kucotsa masilabe m'mau.

Muyeso woyembekezeleka: kusinthanitsa ndi kucotsela masilabe kupanga mau kwacitika moyenela

 **Nchito C: Kuzindikile masilabe m’mau.**

I. Mphunzitsi

- Phunzitsani kazindikilidwe ka masilabe m'mau.
- Patsani aphunzi mau omwe ali ndi masilabe opangidwa ndi mvekelo /nkh/ ndipo muwauze kuti azindikile zigao za masilabe zomwe zimveka m'mauwo.

Citsanzo

1. Nkhalango nkha/la/ngo
2. Nkhuku nkhu/ku

Uzani aphunzi kuti azindikile masilabe onenedwa m’mau poika kamzele munsi mwa silabe.

Citsanzo

1. Mankhama
2. Nkhulungo

II. Aphunzi

- Amvetsele pomwe aphunzitsi akuphunzitsa kazindikilidwe ka masilbe.
- Azindikile zigao za masilabe zomwe zimveka m'mau.
- Azindikile masilabe onenedwa m’mau poika kamzele munsi mwa silabe.

Muyeso woyembekezeleka: Masilabe azindikilidwa moyenela.



Nchito D: Kuwelenga masilabe

I. Mphunzitsi

- Phunzisani kawelengedwe ka masilabe m'mau.
- Uzani aphunzi kuti awelenge nambala ya masilabe m’mau opatsidwa omwe ali ndi mvekelo /nkh/ m'magulu ao.

Citsanzo

1. Nkhondowosi 4
2. Nkhuzyeni 3

- Patsani aphunzi nchito yowelenga masilabe m'mau omwe ali ndi mvekelo /nk/ paokha.

  Aphunzi

- Amvetsetse pomwe aphunzitsi akuphunzitsa kawelengedwe ka masilabe m'mau.
- Awelenge nambala ya masiabe m’mau ali ndi mvekelo /nkh/ m'magulu ao.
- Awelenge nambala ya masilabe m'mau ali ndi mvekelo /nk/ paokha.

Muyeso woyembekezeleka: Aphunzi azindikila namabala ya masilabe m’mau osiyana-siyana moyenela.



Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kulumikidza masilabe kupanga mau, kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano, kuzindikila masilabe mu mau ndi kuwelenga masilabe.

KUWELENGA

MUTU 3: Kuwelenga mofulumila

Luso lapadela1: Kuwelenga mau mokweza ndi kaculidwe ka mau koyenela.

 **Nchito : Kuwelenga mau**

I. Mphunzitsi:

- Phunzitsani aphunzi kawelengedwe ka mau omwe ali ndi mvekelo /nkh/ mokweza komanso mosamala kaculidwe ka mau.
- Ikani aphunzi m'magulu ndipo muwapatse mau omwe ali ndi mvekelo /nkh/ kuti awelenge mosamala kaculidwe ka mau.
- Patsani aphunzi mau ndipo muwauze kuti awelenge paokha mosamala kaculidwe ka mau.

II. Aphunzi:

- Aphunzile kawelengedwe ka mau omwe ali ndi mvekelo /nkh/ mokweza komanso mosamala kaculidwe ka mau.
- Awelenge mau ali ndi mvekelo /nkh/ mokweza komanso mosamala kaculidwe ka mau.
- Awelenge mau ali ndi mvekelo /nkh/ paokha mosamala kaculidwe ka mau.

Muyeso woyembekezeleka: Mau awelengedwa moyenela.

Luso Lapadela 2: Kuwelenga nkhani mokweza ndi kaculidwe ka mau koyenela.

 **Nchito A:Kuwelenga ndi kumvetsetsa nkhani.**

I. Mphunzitsi:

- Phunzitsani kawelengedwe ka nkhani ndi kayankhidwe ka mafunso mokweza ndi mosamala kaculidwe ka mau.
- Patsani aphunzi nkhani ndipo muwauze kuti awelenge m'magulu ao.

Nkhani:

Mnkhalango mumapezeka nyama zosiyana-siyana.

Nkhandwe ndi imodzi mwa nyama zazikali nkhalango.

Tiyenela kusamalila nkhalango.

- Funsani aphunzi mafunso pazomwe awelenga.

II. Aphunzi:

- Amvetsetse pomwe aphunzitsi akuphunzitsa kawelengedwe ka nkhani ndi kayankhidwe ka mafunso mokweza ndi mosamala kaculidwe ka mau.
- Awelenge nkhani m'magulu ao
- Ayankhe mafunso ocokeloa mnkhani yomwe awelenga.

Mafunso

1. Kodi nyama zikhala kuti?
2. Chulani nyama yomwe mwamva mnkhani.
3. Fotokozani ubwino umodzi cabe wosamalila nkhalango.

Muyeso woyembekezeleka: Ziganizo zawelengedwa ndipo mafunso ayankhindwa moyenela.

Nchito B: Kuwelenga nkhani ya ziganizo zapakati pa ziwili ndi zitatu. (Kuwelenga kwa bgulu, kubwelezela zomwe wina akuwelenga ndi kuwelenga awili-awili.

I. Mphunzitsi :

- Onetsani aphunzi kawelengedwe ka nkhani mokweza ndi maculidwe a mau oyenela
- Patsani aphunzi nkhani kuti awelenge m'magulu ao.

Nkhani:

Tsiku lina, atate anapita ku nkhalango kukatema nkhuni.

Alikutema nkhuni, anaona nthudza zakupsa mu mtengo.

Anakondwela kwambili cifukwa anli ndi njala.

- Uzani aphunzin kuti akhale awili-awili ndipo muwapatse kabuku ka nkhani kuti awelenge.

II. Aphunzi

- Amvetsetse pomwe aphunzitsi akuphunzitsa kawelengedwe ka nkhani mokweza ndi maculidwe a mau oyenela
- Awelenge nkhani m'magulu ao.
- Awelenge nkhani awili-awili mokweza ndi maculidwe a mau oyenela.

 **Nchito C: Kuwelenga nkhani zili ndi mvekelo zosiyana-siyana komanso zolumikizidwa.**

I. Mphunzitsi

- Phunzitsani kawelengedwe ka nkhani ili ndi mau ali ndi mvekelo/nkh/ polata masilabe ndi mau ali m'nkhani.
- Ikani aphunzi m'magulu kapena awili-awili ndipo muwapatse nkhani kuti awelenge polata masilabe ndi mau omwe ali kuwelenga.
- Uzani aphunzi kuti alembe nkhani ndi kuika kamzele munsi mwa mau omwe ali ndi silabe ya mvekelo /nkh/.

II. Aphunzitsi:

- Amvetsetse pomwe aphunzitsi ali kuphunzitsa kawelengedwe ka nkhani ili ndi mau ali ndi mvekelo/nkh/ polata masilabe ndi mau ali mnkhani.
- Awelenge awili-awili polata masilabe ndi mau omwe ali m'nkhani.
- Alembe ziganizo ndi kuika kamzele munsi mwa mvekelo /nkh/ m'mau.

Muyeso Woyembekezeleka: Nkhani zili ndi mvekelo zosiyana-siyana komanso zolumikizidwa yawelengedwa moyenela.

 **Mwacidule**: mutu uyu unali kuona pa kuwelenga mau mokweza ndi maculidwe a mau oyenela komanso pa kuwelenga ziganizo mokweza ndi maculidwe a mau oyenela.

CAPAMUTU 4: MVETSO

MUTU 1: Mvetselo ya Kumvetsela

Mutu Waung'ono 1: Maganizo yeni-yeni.

 **Ciyambi:** Mutu uyu uzaona pa kuzindikila ndi kutulutsa maganizo yeni-yeni pa zomwe amva.

Luso Lapadela: Kupeleka maganizo eni-eni kulingana ndi zomwe zamva.

Zipangizo Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Makhadi a ziganizo, mabuku.

 **Mau Ofunikila Kudziwa:** Maganizo, mvetselo.

Mfundo zophunzitsa:

- Kuphunzitsa m'mene aphunzi angapelekele maganizo ao pa zomwe amva kapena kuwelenga.
- Kuwelenga nkhani kwa aphunzi ndi kuwafunsa mafunso mwakulankhula cabe.
- Kuuza aphunzi kuti apeleke cigamulo kulingana ndi zomwe amva.

 **Nchito A: Kuzindikila ndi kupeleka maganizo yeni-yeni pa zomwe amva**

I. Mphunzintsi:

- Uzani aphunzi kuti amvetsele ku nkhani yomwe muzanena cabe ndipo apeleke maganizo ao kulingana ndi zomwe azamva.
- Nenani nkhani yapamtina ndipo aphunzi amvetsele ndi kupeleka maganizo ao.
- **Aphunzi**
- Amvetsele ku nkhani ndi kupeleka maganizo ao kulingana ndi zomwe amva.

Muyeso Woyembekezeka: Aphunzi apeleka maganizo eni-eni kulingana ndi zomwe amva moyenela.

Nchito B: Kufupikitsa uthenga.

I. **Mphunzitsi:**
- Uzani aphunzi kuti afotokoze nkhani yomwe amva mwakutengamo cabe mfundo zeni-yeni.

II. **Aphunzi:**
- Afupikitse nkhani kulingana ndi zomwe amva.

Muyeso Woyembekezeleka: Nkhani yafupikitsidwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kufupikitsa maganizo kulingana ndi zomwe amva.

Mutu Waung'ono 2: Zoona ndi malingalilo

Ciyambi: Mutu uyu udzaona pa kuzindikila malingalilo mu nkhani ndi kuzindikila zoona mu nkhani.

Luso Lapadela: Kusiyanitsa zoona ndi malingalilo.

Mau Ofunika Kudziwa: zoona, malingalilo, maganizo, kusiyanitsa nkhani.

Mfundo Zophunzitsa:

- Tanthauzo la mau "malingalilo, maganizo", zoona.
- Kusiyanitsa zoona ndi malingalilo kapena kuti maganizo.

Nchito A: Kuzindikila zotuluka m'maganizo mu nkhani

I. Mphunzitsi:

- Kambani kankhani kosangalatsa kwa aphunzi.

Nkhalango ya akalulu

Kalulu ndi kanyama kokhala m’nkhalango.

Anthu ambili amakonda nkhani zake.

Iwo amati “Kakalulu ndi kocenjela kwambili”.

Iko kamanamiza nyama zinzake nthawi zambili.

Kalinso ndi liwilo loculuka zedi.

- Funsani aphunzi ngati kalulu amamudziwa.
- Afunseni za maonekedwe ake.
- Afunseni za nkhani zomwe anamva zokhudza kalulu.
- Uzani aphunzi kuti nkhani zomwe amamva zokhudza kalulu monga yakuti “kalulu ndi mfumu ya m’nkhalango” ndi malingalilo cabe a anthu.
- Uzani Aphunzi kuti anene nkhani zomwe adziwa yokhudza Kalulu.

II Aphunzi:

- Amvetsele kwa mphunzitsi pomwe akusimba kankhani kosangalatsa.
- Anene ngati Kalulu amamudziwa.
- Anene za maonekedwe a kalulu.
- Anene nkhani zomwe anamva zokhudza kalulu.
- Amvetsele modekha kwa mphunzitsi pomwe akufotokoza za malingalilo a anthu.
- Anene nkhani zomwe adziwa yokhudza kalulu.

Muyeso Woyembekezeleka: Malingalilo a m’nkhani azindikilidwa moyenela.

Nchito B: Kuzindikila zoona mu nkhani.

I Mphunzitsi:

- Kambani kankhani kosangalatsa kwa aphunzi.

Nkhani:

Nkhalango ya akalulu

Kalulu ndi kanyama kokhala m’nkhalango.
Anthu ambili amakonda nkhani zake.

Iwo amati “Kakalulu ndi kocenjela kwambili”.

Iko kamanamiza nyama zinzake nthawi zambili.

Kalinso ndi liwilo loculuka zedi.

Funsani aphunzi ngati kalulu amamudziwa.

- Afunseni za maonekedwe ake.
- Afunseni za nkhani zomwe anamva zokhudza kalulu.
- Uzani aphunzi kuti zeni-zeni za Kalulu monga maonekedwe ndi zakudya zake ndi zimene timati zoona.
- Uzani Aphunzi kuti anene zoona za kalulu zimene adziwa.

II Aphunzi:

- Amvetsele kwa mphunzitsi pomwe akusimba kankhani kosangalatsa.
- Anene ngati Kalulu amamudziwa.
- Anene za maonekedwe a kalulu.
- Anene nkhani zomwe anamva zokhudza kalulu.
- Anene zeni-zeni zokhudza kalulu.
- Anene nkhani zoona zimene adziwa zokhudza kalulu.

Muyeso Woyembekezeleka: Zoona zasiyanitsidwa ndi malingalilo moyenela.

Mutu uyu unali kuona pa kusiyanitsa zoona ndi malingalilo ndiponso kuzindikila zoona mu nkhani.

MVETSO

Mutu 2: Mvetso ya kuwelenga.

Mutu Waung’ono: Zoona za nkhani.

**Ciyambi:** Mutu Waung'ono uyu udzaona pa Kufotokoza zomwe zawelengedwa, kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa ndi kufotokoza zocitika m'nkhani molondola.

Luso Lapadela: Kupeleka uthenga wocokela m'nkhani wofotokozedwa mokwanila.

**Mau Ofunika Kudziwa:** Kufotokoza, nkhani, molondola, mokwanila.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Mabuku a Aphunzi owelenga, mabuku a nthano.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuwelenga nkhani.
- Kufufuza zoona za nkhani.
- Kuzindikila zoona za nkhani.

**Nchito A: Kufotokoza zomwe zawelengedwa m'nkhani.**

II. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani yosonyeza amene anacita nkhani, kumene nkhani inacitikila ndi m'mene nkhani inacitikila pomwe aphunzi akumvetsela modekha.
- Fufuzani zoona za nkhani mwa kukambilana ndi aphunzi zomwe zawelengedwa.
- Pezani mfundo zothandiza kuti muzindikile zoona za nkhani.
- Uzani Aphunzi kuti Awelenge nkhani ndi kuyankha mafunso kucokela ku nkhani yomwe yawelengedwa.

II Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani yomwe mphunzitsi wawelenga yosonyeza amene anacita nkhani, kumene nkhani inacitikila ndi m'mene nkhani inacitikila.
- Kufufuza nkhani mwa kukambilana ndi mphunzitsi.
- Kupeza mfundo zothandiza kuti azindikile zoona za nkhani.

- Awelenge nkhani ndi kuyankha mafunso.

Muyeso Woyembekezeleka: Kufotokoza zomwe zawelengedwa m'nkhani kwacitidwa moyenela.

 **Nchito B: kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa.**

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kuwelenga nkhani.
- Pamodzi ndi aphunzi, kambilanani zomwe zawelengedwa.
- Funsani Aphunzi mafunso kucokela ku nkhani yomwe yawelengedwa.

II Aphunzi:

- Amvetsele ku citsanzo ca kuwelenga kwa mphunzitsi.
- Akambilane ndi mphunzitsi zomwe zawelengedwa.
- Ayankhe mafunso kucokela ku nkhani yomwe yawelengedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuyankha mafunso kucokela ku nkhani yomwe yawelengedwa kwacidwa moyenela

 **Nchito C: Kufotokoza zocitika m'nkhani molondola.**

I Mphunzitsi:

- Welengani nkhani kwa aphunzi.
- Uzani aphunzi kuti awelenge nkhani yomwe yawelengedwa ndi mphunzitsi.
- Pamodzi ndi aphunzi, kambilanani ndi aphunzi zomwe zawelengedwa.
- Funsani aphunzi mafunso kucokela ku nkhani yowelengedwa.

II Aphunzi:

- Awelenge nkhani yomwe mphunzitsi wawelenga.
- Akambilane zomwe zawelengedwa m'nkhani.

- Amvetsele ku nkhani pomwe mphunzitsi akuwelenga.

Muyeso Woyembekezeleka: Kufotokoza zocitika m'nkhani kwacitidwa

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa Kufotokoza zomwe zawelengedwa m'nkhani , kuyankha mafunso kucokela ku nkhani yomwe yawelengedwa ndi kufotokoza zocitika m'nkhani molondola.

CIGAWO 5: MALEMBEDWE

Mutu: Malembedwe

Mutu waung'ono 1: Mapangidwe a Lembo

 Ciyambi: Mutu uyu udzaona pa kujambula malembo, kulemba malembo, kulemba mam'malembedwe okhazikika ndi kujambula ziganizo m'malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

Luso Lapadela: Kulemba malembo

 **Mau Ofunika Kudziwa**: Malembedwe, owelengeka, okhazikika, mpata, kujambula.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Coko, phensulo, mabuku olembamo aphunzi.

Mfundo zophunzitsa:

- Kusonyeza majambulidwe a malembo kucokela koyambila polemba mpaka kumapeto poonetsa mayendedwe a dzanja lomwe lili ndi colembela.
- Malembedwe a malembo opatsidwa.
- Kujambula ziganizo m'malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

 **Nchito A: Kujambula malembo**

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kulemba malembo awa /n, k, h / m'malembedwe okhazikika m'mizela olembedwelatu pa bolodi.

  nnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnnn

  Kkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkk

  kkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkkk

- Uzani aphunzi kuti ajambule malembo monga m'citsanzo canu pa bolodi ndipo muwaongolele pomwe akujambula.
- Uzani aphunzi kuti ajambule malembo omwe alembedwa pa bolodi m'mabuku ao olembamo.

II. Aphunzi:

- Aonetsetse pomwe mphunzitsi akulembela malembo m'malembedwe okhazikika m'mizela olembedwelatu pa bolodi.
- Ajambule malembo monga m'citsanzo ca mphunzitsi pa bolodi mothandizidwa ndi mphunzitsi..
- Ajambule malembo omwe alembedwa pa bolodi m'mabuku ao olembamo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula malembo kwacitika moyenela.



Nchito B: Kulemba malembo (nz, zy, sh, nkh)

I. Mphunzitsi:

- Sonyezani m'mene malembo alembedwela m'malembedwe okhazikika m'mizela olembedwelatu pa bolodi.
- Onetsani aphunzi mayambidwe a kulemba malembo kucokela koyambila mpaka kumapeto.
- Uzani aphunzi kuti adzalembe malembo m'mizela ali pa bolodi.
- Uzani aphunzi kuti alembe malembo opatsidwa m'mabuku ao olembamo.

II Aphunzi:

- Aonetsetse m'mene mphunzitsi akulembela malembo pa bolodi m'mizela olembedwelatu.
- Aonetsetse mayambidwe a kulemba lembo kucokela koyambila mpaka kumapeto kwa lembo.
- Uzani aphunzi kuti adzalembe malembo m'mizela omwe ali pa bolodi.
- Alembe malembo omwe apatsidwa m'mabuku ao olembamo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kulemba malembo kwacitika moyenela.

M**utu Waung'ono 2:** Malembedwe Okhazikika

 **Ciyambi:** Mutu uyu uzaona pa malembedwe okhazikika.

Luso lapadela: Kulemba mau m'malembedwe okhazikika.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Silabiki Chati, Mafulashi Khadi, Makhadi a Ziganizo, Mabuku.

**Mau Ofunikila Kudziwa**: Kulemba, Kukhazikika, Lembo, Malembedwe.

Mfundo Zophunzitsa:

- Uzdani aphunzi malamulo amalembedwe omwe afunika kulondoledwa polemba.
- Fotokozani za lamulo La malembo amucila wopita kumwamba komanso micila wopita pansi mumalembedwe

 **Nchito A: Kujambula Mau M'malembedwe Okhazikika.**

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca malembedwe a mau polondola malembedwe okhazikika ndiponso polemekeza micila yopita kumwamba komanso pansi.

Citani cimodzi-modzi ndi Malemba ena.

II. **Aphunzi:**

- Amvetsele citsanzo ndiponso alembe mau molondola bwino zomwe aphunzitsidwa pakalembedwe ka malembo.

 **Zocita**

Jambulani mau awa m'malembedwe okhazikika.

1. Nkhono.

2. Nkhumba.

3. Nkhani

Muyeso Woyembekezeleka: Mau alembedwa moyenela.

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pakalembedwe ka mau kokhazikika.

Mutu Waung'ono 3: Mipata ya mau.

 **Ciyambi:** Mutu uyu uzayangana pa malembedwe okhazikika.

Luso lapadela: kusiya mipata m'mau.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Fulashi khadi, makhadi a ziganizo, mabuku.

 **Mau Ofunikila Kudziwa**: Kulemba, Kukhazikika, Lembo, Mipata.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kusiya mipata polemba mau m'ziganizo.
- Lamulo La malembo amucila wopita kumwamba komanso pansi.

 Nchito A: Kujambula Ziganizo M’malembedwe Okhazikika.

I. **Mphunzitsi:**

- Pelekani citsanzo ca malembedwe a ziganizo pozindikila ndi kusiya mipata pakati pa mau.

Citani cimodzi-modzi ndi mvekelo zina.

II. Aphunzi:

- Alembe ziganizo ndi kulemekeza kusiya mipata pakati pa mau.

 **Zocita**

Jambulani ziganizo izi m’malembedwe okhazikika.

1. Nkhono ipezeka kumtunda ndi m’madzi.

2. Nkhumba ndi nyama yoweta.

Muyeso woyembekezeleka: Malembedwe okhazikika alembedwa moyenela.

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pakalembedwe ka mau kokhazikika.

MUTU 2: Cimangilizo

Mutu Waung’ono: Nkhani Yapafupi

 **Ciyambi**: Mutu uyu uzayanga’na pakujambula zinthunzi zomwe zidzapeleka uthenga womangilizidwa pamodzi.

Luso Lapadela: Kulemba nkhani yapafupi

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Phensulo, Pepala, Makileyoni.

**Mau Ofunikila Kudziw**a: Zithunzi, Uthenga, Kujambula.

Mfundo Zophunzitsila:

- Fotokozelani aphunzi kuti tingathe kufotokoza malingalilo pakulemba nkhani yapafupi yomwe tiganiza.
- Patsani citsanzo camalingalilo omwe angalembedwe mkankhani kapafupi.

 **Nchito: composing a simple story**

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti alembe kankhani kapafupi pa cinthu comwe akonda kwambili
- Pelekani citsanzo ca nkhani yapafupi

Nkhani

Amai apita kumunda.

Popita ambeleka mwana ndiponso anyamulanso thadza la manga pamutu.

Mwatsoka, poyenda akhumudwa ndipo thadza lagwa pansi.

II. Aphunzi:

- Amvetsele nkhani yokambidwa ndi mphunzitsi.
- Alembe nkhani yao-yao yapafupi

Muyeso Woyembekezeleka: Kulemba nkhani yaifupi kwacitika moyenela.

 **Mwacidule:** Mutuyu unali kuona kulemba nkhani yapafupi yao-yao aphunzi

CAPAMUTU 4 : KUKAMBA ZILAPI

 **Ciyambi:** Cigawo cidzaona pa Kumvetsela ndi Kulankhula, Kuwelenga, Kuwelenga Mofulumila ndi Matanthauzo a Mau. Cidzaonanso pa ku Mvetsela, Mvetso, Kulemba ndi Cimangilizo.

Kumvetsela Ndi Kulankhula

Mutu 1: Zilapi ndi Zopindika Lilime

Mutu Waung'ono 1 : Zilapi

Lambulo: Mutu uwu udzayanga pakukamba ndi kuyankha zilapi.

Luso lapadela: Kukamba ndi kuyankha zilapi

 **Mau ofunika kudziwa:** Zilapi, matanthauzo.

Zida Zophunzitsila ndi Kuphunzilila: Zithunzi

Mfundo Zophunzitsa:

- Kunena zilapi.
- Matanthauzo a zilapi**.**

 **Nchito :** Kukamba ndi kuyankha zilapi.

I. Mphunzitsi:

- Fotokozani za zilapi kuti zili ndi matanthauzo obisika.
- Onetsani cithunzi ca nyumba. Funsani ngati cili ndi khomo.
- Pelekani citsanzo.
  Nyumba ya amai ilibe khomo.

Yankho ndi dzila.

- Nenani zilapi zina. Aphunzi ayankhe.
- Uzani aphunzi acite mpikisano m'magulu.

II. Aphunzi:

- Amvetsele kufotokoza za zilapi.
- Apenye cithunzi ca nyumba kuti cili ndi khomo.
- Amvetsele ku citsanzo.
- Apeleke mayankho a zilapi.
- Acite mpikisano m'magulu.

Zocita:

Pezani matanthauzo a zilapi izi.

1. Mumandimwa koma sindigwilika.
2. Ndili ndi miyendo 4, koma sindiyenda.
3. Mumagona ndi kalowa.

Mayankho:

1. Madzi
2. Thebo
3. Dzuwa

Muyeso Woyembekezeleka: Zilapi zakambidwa ndi kuyankhidwa moyenela.

Cidule: Mutu uwu unali kuona pakukamba ndi kuyankha zilapi.

KUWELENGA

Mutu 1: Kuzindikila Masilabe

Mutu Waung'ono 1: Kuzindikila Masilabe opangidwa ndi **mph-, nth-, nch-, ngw-, mny-,** m'mau okambidwa.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse masilabe opangidwa ndi malemba opatsidwa imodzi-imodzi mpaka onse oonetsedwa pa mwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila masilabe ntha, mpha, mphe, mphi, mpho, mphu.

**Lambulo:** Mutu uyu udzaona pa kuzindikila masilabe m'mau okambidwa, kusewela masewela owelenga masilabe, kupanga mau kugwilitsa nchito masilabe ndi kusewela masewela osintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

**Luso lapadela:** Kuzindikila ndi kugwilitsa nchito masilabe.

Mau Ofunika Kudziwa : Silabe, mvekelo.

Zida Zophunzitsila ndi Kuphunzilila: Zithunzi

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuzindikila masilabe m'mau okambidwa.
- Kusewela masewela amasilabe.

**Nchito A :** Kuzindikila ndi kugwilitsa nchito masilabe mu mau okambidwa.

I. Mphunzitsi :

- Onetsani cithunzi ca mphasa ndi zinthu zina zili ndi silabe lili ndi mvekelo la /mph/ mu silabe.
- Chulani zinthu zili pa cithunzi.
- Chulani masilabe ali mu liu mphasa.
  Citsanzo:
  Mpha ndi **sa**

- Zindikilani masilabe **mpha** ndi **mphe** pamodzi ndi aphunzi m'mau okambidwa**.**
  1. **Mpha**le – mpha
  2. **Mphe**po - mphe

II. Aphunzi:

- Apenye cithunzi ca mphasa ndi zinthu zina zili ndi masilabe ali oyamba ndi **/mph/.**
- Aone cithunzi ca mphasa ndi zinthu zina zili ndi silabe lili ndi mvekelo la /mph/ mu silabe.
- Achule zinthu zili pa cithunzi.
- Anene masilabe ali mu liu mphasa.
  Citsanzo:
  Mpha ndi **sa**
- **Azindikile masilabe mpha ndi mphe pamodzi ndi Mphunzitsi m'mau okambidwa.**
  3. **Mpha**le – mpha
  4. **Mphe**po - mphe

Zocita:

1. Akambe masilabe mpha mphe mphi mpho mphu ali m'mau awa;
   mphala, mphika, mphuno, mphemvu, mphongo.

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe azindikilidwa m'mau okambidwa moyenela.

Nchito B : Kusewela masewela owelenga masilabe**.**

I. Mphunzitsi:

- Gwilitsani nchito chati ili ndi zithunzi za mphika ndi mphuno kuyamba phunzilo.
- Chulani mau mphika ndi mphuno.
- Sonyezani kupeza nambala ya masilabe mu mau okambidwa poomba m'manja pa silabe lililonse.
- Thandizani aphunzi kucita sewelo loomba m'manja.
  Citsanzo

mphika – kuomba kawili(2). mphi, kuomba 1 ndi ka kuomba 2.

II. Aphunzi:

- Apenye zithunzi za mphika ndi mphuno.
- Achule mau mphika ndi mphuno.
- Akambe masilabe pha phe phi pho phu .
- Amvetsele kumapezedwe a nambala ya masilabe pa liu poomba m'manja pa silabe lililonse.
- Aombe m'manja pa silabe lili lonse mu liu mphika ndi mphuno kupeza nambala ya masilabe.

  Zocita:

Apeze nambala ya masilabe m'magulu amau awa poomba m'manja.

1. Mphako 2. Mphelo 3. Mphila 4. Mphemvu 5. Mphumi

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela owelenga masilabe aseweledwa moyenela.

Nchito C : Kupanga mau okambidwa kulumikidza masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Chulani masilabe awa : mpha mphe mphi mpho mphu.
- Chulani masilabe ena monga le ndi mvu.
- Sonyezani kulumikidza masilabe.

  Citsanzo:

  Silabe **mpha** ndi **mvu**, ipanga mau **mphamvu**.

  Silabe **mphe** ndi **le,** ipanga **mphele.**
- Uzani aphunzi apange mau m'magulu ndipo muwathandize.

II. Aphunzi:

- Amvetsele kuchulidwa kwa masilabe awa : mpha mphe mphi mpho mphu.
- Achule masilabe ena monga le ndi mvu.

- Amvetsele kulumikidza masilabe kulondola zitsanzo.
- Apange mau m’magulu mothandizidwa ndi Mphunzitsi..

Zocita:

Pangani mau asanu (5) ndi masilabe awa;

Mpha mphe mphi mpho mphu

tso la mi mvu ngo

Mayankho:

Mphatso mphemvu mphila mphongo mphuno

Muyeso Woyembekezeleka: Mau okambidwa apangidwa polumikidza masilabe moyenela.

 **Nchito D :** Kusewela masewela osintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

I. Mphunzitsi:

- Chulani mau monga mphika, mphala ndi mphele.
- Sonyezani kusintha masilabe ndi kupanga mau ena.

  Citsanzo:

  mphaka kusintha silabe **mpha** ndi kuikapo silabe **mphi**, ipanga liu **mphika**.
- Pelekani citsanzo kucotsa silabe kupanga mau atsopano.

  Citsanzo

  Mnyamata kucotsa mnya, liu likhala mata.
- Uzani aphunzi asinthe ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano m’magulu

II. Aphunzi:

- Achule mau monga mphika, mphala ndi mphele.
- Alondole citsanzo cosintha masilabe ndi kupanga liu latsopano.
- Amvetsele ku citsanzo cakucotsa silabe kupanga liu latsopano.

- Asinthe ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano m'magulu mothandizidwa ndi mphunzitsi.

Muyeso Woyembekezeleka: Masewela opanga mau aseweledwa moyenela.

 **Cidule**: Mutu uyu unali kuona pa kuzindikila masilabe m'mau okambidwa, kusewela masewela owelenga masilabe, kupanga mau kugwilitsa nchito masilabe ndi kusewela masewela osintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau atsopano.

Mutu 2 : Kupanga Masilabe

Mutu Waung'ono 1 : Masilabe

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse kupanga masilabe pa kulumikidza makonsonanti amodzi ndi mavawelo mpaka onse oonetsedwa pa mwambapa atatha.Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo.

Mpha mphe mphi mpho mphu

 **Lambulo:** Mutu uyu udzaona pa kulumikidza makonsonati ndi mavawelo kupanga masilabe, kuwelenga chati la masilabe, kusankha masilabe, kusintha lembo ndi kulumikidza malembo ophatikizana koma omveka mosiyana ndi mavawelo.

 **Luso lapadela:** Kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

Mau Ofunika Kudziwa : Makonsonanti, mavawelo, kulumikidza, mamvekedwe.

Zida Zophunzitsila ndi Kuphunzilila: Zithunzi , Silabiki chati, ma fulashi khadi.

Mfundo Zophunzitsa

- Kulumikidza konsonati ndi vawelo.

- Kupanga silabe.
- Kuwelenga silabiki chati.
- Kusankha masilabe.
- Kusintha lembo.



Nchito A: Kupanga masilabe polumikidza makonsonanti ndi mavawelo.

I. Mphunzitsi:

- Sonyezani kapangidwe ka silabe polumikidza konsonanti ndi vawelo. kapangidwe ka silabe kugwilitsa nchito makonsonanti m p h ndi mavawelo a e i o u.
  mph kulumukidza **a** ipanga **mpha**
  mph ndi **e** ipanga **mphe**
- Welengani masilabe.
- Thandizani aphunzi kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

II. Aphunzi:

- Apenyetsetse kapangidwe ka silabe kugwilitsa nchito makonsonanti m p h ndi mavawelo a e i o u.
- Awelenge masilabe.
- Alumikidze makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe mothandizidwa ndi mphunzitsi
  Zocita:
  Lumikidzani makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.
  mpha mphe mphi mpho mphu
  la le li lo lu
  1. Mphala
  2. _____lo
  3. Mphi___

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe anapangidwa polumikidza makonsonanti ndi mavawelo moyenela.

Nchito B: Kuwelenga chati la masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Chulani masilabe mpha ntha ncha ngwa mnya**.**
- Welengani silabiki chati lili ndi masilabe ali ndi masilabe achulidwa.

Citsanzo:

makansonanti	a	e	i	o	u
mph	mpha	mphe	mphi	mpho	mphu

- Thandizani aphunzi kuwelenga motele onse masilabe ali ndi mvekelo zili mcigawo ici.

II. **Aphunzi:**

- Achule masilabe.
- Awelenge chati la masilabe .
- Awelenge chati la masilabe m'magulu.

Zocita:

Pezani masilabe osowa

1. Mpha mphe mphi mpho mphi
2. Ntha nthe nthi ntho ____
3. Ngwa ngwe __ ngwo ngwu

Muyeso Woyembekezeleka: Chati la masilabe lawelengedwa moyenela.

Nchito C: Kusankha masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Chulani mau ali ndi masilabe awili (2), atatu (3) ndi anai (4).
- Sewenzetsani mafulashi khadi ali ndi mau omwe ali ndi masilabe 2, 3 ndi 4.
- Thandizani aphunzi kuwelenga mau ali pa mafulashi khadi.
- Ikani mau m'magulu amasilabe 2, 3 ndi 4.
- Ombani m'manja kupeza nambala ya masilabe.

II. Aphunzi:

- Achule mau ali ndi masilabe awili (2), atatu (3) ndi anai (4).
- Aswenzetse mafulashi khadi omwe ali ndi masilabe 2, 3, 4.
- Awelenge mau ali pa mafulashi khadi.
- Aike mau m'magulu amasilabe amau ali ndi masilabe 2, 3 ndi 4.
- Aombe m'manja kupeza nambala ya masilabe.

Zocita:

1. lembani mau ali ndi masilabe atatu (3) mwa awa;
   mphako, nthongololo, nthakula, mnyamata, mnyumba, nthungulu

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe asankhidwa moyenela.

Nchito D : Kusintha lembo

I. Mphunzitsi:

- Achule mau monga nthala ndi Ngwila.
- Sonyezani aphunzi kusintha lembo lili koyambila n ndi kuikapo m.
  Nthala – **m**thala
- Uzani aphunzi asinthe mau m'magulu. Athandizeni pomwe apeza bvuto.

II. Aphunzi:

- Achule mau.
- Amvetsele kusintha lembo lili koyambila.

- Asinthe lembo loyamba ku liu m'magulu.Afunse pomwe apeza bvuto.

Zocita:

Pezani mau asanu (5) ndi kusintha lembo kupanga mau atsopano.

1. Mphel**e** sinthani lembo lili kothela e kuikako o.
   likhala ____
2. Mphak**o** sinthani o kuikako a liu latsopano _____
   Muyeso Woyembekezeleka: Malembo asinthidwa moyenela.

 **Nchito E:** Kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti monga ngw, nth ndi mny.
- Lumikidzani ndi mavawelo kupanga masilabe.
  Zitsanzo:
  Ngw ndi a ipanga silabe ngwa.
  Nth ndi a ipanga silabe ntha.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku zitsanzo.
- Apange masilabe.

Zocita:

Lumikidzani malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

a e i o u

ngw, nth, nch

Mayankho: Ngwa ngwe ngwi ngwo ngwu

Muyeso Woyembekezeleka: Malembo ophatikizana koma omveka mosiyana amakonsonanti ndi mavawelo alumikizidwa ndi kupanga masilabe moyenela.

**Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa kulumikidza makonsonati ndi mavawelo kupanga masilabe, kuwelenga chati la masilabe, kusankha masilabe, kusintha lembo ndi kulumikidza malembo ophatikizana koma omveka mosiyana ndi mavawelo.

Mutu Waung'ono 2: Mau

**Lambulo:** Mutu uyu udzaona pakulumukidza masilabe kupanga mau, kusintha ndi kucotsa silabe kupanga mau, kuzindikila masilabe ndi kuwelenga masilabe.

Luso lapadela1: Kulumikidza masilabe kupanga mau.

**Mau Ofunika Kudziwa:** Mphatso, mphusi, mphasa.

Zida Zophunzitsila ndi Kuphunzilila: Zithunzi , Silabiki chati, ma fulashi khadi.

Mfundo Zophunzitsa

- Kulumikidza masilabe.
- Kupanga mau.

**Nchito A:** Kulumikidza masilabe kupanga mau.

I. Mphunzitsi :

- Onetsani cithunzi ca mphasa.
- Funsani aphunzi achule dzina la mphasa.
- Sonyezani m'mene liu mphasa ingapangidwile kugwilitsa nchito masilabe mpha mphe mphi mpho mphu

sa se si so su

mpha ndi sa ipanga mphasa

- Funsani aphunzi apange mau ena ndi masilabe apatsidwa m'magulu.

II. Aphunzi :

- Apenyetsetse m'mene liu mphasa ingapangidwile kugwilitsa nchito masilabe.
- Apange mau ena ndi masilabe apatsidwa m'magulu.
- Awelenge mau opangidwa monga, mphaso, mphesi, mphusi.

Zocita:

Pangani mau anai (4) ndi masilabe awa;

Mpha mphe mphi mpho mphu

La le li lo lu

Mau

1. Mphala
2. Mphale
3. mphele
4. Mphelo

Muyeso Woyembekezeleka: Masilabe alumikidzidwa kupanga mau moyenela.

Nchito B: Kusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau.

I. Mphunzitsi:

- Welengani mau monga awa mphala, mphasa ndi mphuno.
- Sonyezani kucotsa silabe ndi kuikapo lina kupanga liu la tsopano.
  mphala kucotsa **mpha** kuipo **mphi ,** liu likhala **mphila**.
- Acotse silabe lili koyambila mau kupanga mau mosaikapo lina.
  Zitsanzo: **Ngwengwelele** kucotsa **Ngwe**, liu likhala **ngwelele**.
  Ngwenyama kucotsa **Ngwe** liu likhala **nyama**.

II. Aphunzi:

- Awelenge mau.
- Apange mau m'magulu kugwilitsa nchito mafulashi khadi.
  mphala, mphasa.
- Acotse silabe lili koyambila ndi kuikapo lina kupanga liu latsopano.
- Awelenge mau atsopano.

Zocita:

Aphunzi acotse silabe lili koyambila kwa liu ndi kuikapo lina kupanga liu latsopano.

mpha mphe mphi mpho mphu

mphala - mphila

mphele - ____le

mphaka - ____ka

1. Cotsa silabe kupanga liu lina.
   (i) Ngwenyama – nyama
   (ii) Ngwengwelele - ____

Mayankho:

1. Mphele – mphale
   Mphaka – mphika
2. (ii) Ngwengwelele - ngwelele

Muyeso woyembekezeleka: Masilabe asinthidwa ndi kucotsedwa moyenela.

Nchito C: Kuzindikila masilbe mu mau

I. Mphunzitsi :

- Welengani mau pa chati monga mphuno, nthele, nchenche, ngwilo ndi mnyengo.
- Lembani kamzele pa silabe lililonse m’mau.
- Zindikile silabe powelenga coimilila pa silabe lilonse m’mau.
- Citani mpikisano ozindikila masilabe m’mau.

II. Aphunzi:

- Awelenge mau pa chati.
- Alembe kamzele pa silabe lililonse m’mau.
- Azindikile silabe powelenga coimilila pa silabe lilonse m’mau.
- Acite mpikisano ozindikila masilabe m’mau.

Zocita:

Lembani masipelo amau awa.

1. Nthele
2. Mnyamata
3. Ngwilo

Muyeso woyembekezeleka: Masilabe m’mau azindikilidwa moyenela.

 **Nchito D :** Kuwelenga masilabe m’mau.

I. Mphunzitsi:

- Wonetsani chati ili ndi mau.
- Uzani awelenge mau.Awelenge coimilila pa silabe lili lonse.
- Aombe m’manja kuzindikila silabe.
- Uzani aphunzi achule nambala ya masilabe.

II. Aphunzi:

- Apenye mau ali pa chati.

- Awelenge mau.Aimilile pa silabe lililonse.
- Aombe m’manja kuzindikila silabe.
- Achule nambala ya masilabe.

  Zocita:

  Pezani nambala ya masilabe m’mau awa.

  1. Nthambi
  2. Mphemvu
  3. Ngwengwelele

Mayankho: 1. Masilabe 2, 2. Masilabe 2, 3. Masilabe 3

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga masilabe kwacitika moyenela.

**Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pakulumukidza masilabe kupanga mau, kusintha ndi kucotsa silabe kupanga mau, kuzindikila masilabe ndi kuwelenga masilabe.

Luso Lapadela 2: Kuwelenga mau mokweza kulondola kachulidwe ka mau koyenela.

I. Mphunzitsi:

- Ikani chati yomwe ili ndi zithunzi za zinthu monga mphasa, nthambo, nchenche, ndalama ya ngwee ndi mnyamata.
- Uzani aphunzi achule maina a zinthuzi.
- Awelenge maina a zinthu kugwilitsa nchito mafulashi khadi ndi chati mokweza mau.

II. Aphunzi:

- Achule maina a zinthuzi.
- Awelenge maina.
- Awelenge mau ena awili awili mokweza mau.

Zocita:

Aphunzi awelenge mau m’magulu kugwilitsa nchito mafulashi khadi.

Muyeso Woyembekezeleka: Mau awelengedwa moyenela.

Nchito C : Kuwelenga ndi kumvetsetsa ziganizo.

I. Mphunzitsi:

- Wonetsani chati lili ndi mau awa.
  Mphika, moto, mnyamata, galu, mphasa, pa, mnyanja, walowa, wakhala, pa, uli.
- Pelekani citsanzo ca ciganizo potenga mau kucokela pa chati ndi kupanga ciganizo.
  Citsanzo:
  Mphika uli pa moto.
- Welengani ziganizo zina zocokela ku mau ali pa chati .
- Afunseni afotokoze zomwe amvapo pa ziganizo.

II. Aphunzi:

- Awelenge mau ali pa chati.
- Londolani citsanzo.
- Awelenge ziganizo.
- Afotokoze zomwe amvapo pa ziganizo.

Zocita:

Awelenge ziganizo m’magulu.

Muyeso Woyembekezeleka: Ziganizo zawelengedwa ndi mafunso ayankhidwa moyenela.

Nchito D : Kuwelenga ndi kumvetsa zolembedwa mziganizo.

I. Mphunzitsi:

- Ikani mafulashi khadi ali ndi mau osiyana siyana kutsogolo.
- Welengani mau ali pa mafulashi khadi.
- Patsani aphunzi zolembedwa mziganizo m'magulu.

  Atate anyamula mphale, mwana ndi cigubu pa njinga.

  Amalume ao a Ngwenya ali kupsela nthongololo.
- Welengani kulondola zopumila ndi kusonyeza mawelengedwe oyenela.
- Funsani aphunzi afotokoze mawelengedwe anu.Funsani mafunso ena.
- Uzani aphunzi awelenge onse pamodzi, m'magulu ndi awili awili, komanso m'modzi m'modzi.

II. Mphunzi :

- Apenye mau pa mafulashi khadi .
- Apenye zolembedwa mziganizo m'magulu.

  Atate anyamula mphale, mwana ndi cigubu pa njinga.

  Amalume ao a Ngwenya ali kupsela nthongololo.
- Atsatile kuwelenga polata ndi cala.
- Afotokoze mawelengedwe amphunzitsi. Ayankhe mafunso yoonetsa kuti amvetsetsa zowelengedwa.
- Awelenge onse pamodzi, m'magulu ndi awili awili, komanso m'modzi m'modzi.

Zocita:

Tsilizani ziganizo ndi mau awa.

njinga	nchenche	mphale

1. Atate ananyamula mphale, ____ ndi cigubu pa ____.
2. Jambula cithunzi ca nchenche.Ulembe ciganizo pa cithunzi.

   _____ ibweletsa matenda.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga zolembedwa mziganizo zitatu zawelengedwa moyenela.

 **Nchito E:** Kuzindikila zolembedwa zili ndi mvekelo zosiyana siyana ndi zolumikidza.

I. Mphunzitsi:

- Sewenzetsani mafulashi khadi ali ndi mvekelo /n/, /t/ ndi /h/.
- Zindikilani mvekelo imodzi-imodzi.
- Chulani mau ali ndi mvekelo /nth/.
- Uzani aphunzi achule mvekelo zonse pamodzi /nth/.
- Auzeni achule mau ali ndi mvekelo zophatikiza /nth/.
- Welengani mau, muimilile mkafika pa mvekelo zophatikizidwa.

II. Aphunzi:

- Penyani mvekelo zili pa mafulashi khadi /n/, /t/ ndi /h/.
- Azindikile mvekelo imodzi-imodzi.
- Achule mau ali ndi mvekelo /nth/.
- Achule mvekelo zonse pamodzi /nth/.
- Achule mau ali ndi mvekelo zophatikiza /nth/.
- Awelenge mau, aimilile akafika pa mvekelo zophatikizidwa.

Zocita:

Sankhani mau ali ndi mvekelo zophatikizidwa.

1. Mphila
2. Mnyamule
3. Nthele

Muyeso Woyembekezeleka: Kulumikiza makonsonanti ndi mavawelo kupanga mau, ndi kuwelenga mau kwacitidwa moyenela

 **Cidule:** Mutuyu unali kuona pa kuwelenga masilabe, kuwelenga mau mokweza ndi kuwelenga nkhani kulondola mawelengedwe woyenela.

MATANTHAUZO A MAU

Mutu 4: Maina

Mutu Waung'ono 1 : Maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa.

 **Ciyambi:** Mutu uyu unali kuona pakupanga, kulinganiza, kusewela masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.

Luso lapadela: Kupanga maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.

 **Mau ofunika kudziwa**: Dzina, maina, ambiri, oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Zithunzi, mafulashi khadi, machati

Mfundo Zophunzitsa

- Kupanga maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.
- Kulinganiza dzina ndi maina.
- Kusewela masewela woculukitsa ndi kucepetsa maina.

 **Nchito A:** Kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.
Zindikilani kuti poculukutsa maina, munga gwilitse nchito mvekelo kapena silabe monga **a, ma, mi, zi ndi ena.**

I. Mphunzitsi:

- Gwilitsani nchito zinthu kapena zithunzi za zinthu zili ndi mvekelo izi;
  /mph/, /nth/, / mny/, / ngw/, /nch/

- chulani maina a zinthu.

  Mphika nthoci mnyamata mphonda ngwilo ngwee

- Sonyezani kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

  Citsanzo:

  Mphika – miphika

  Nyumba – manyumba

- Auzeni aphunzi apange maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

II. Aphunzi :

- Achule maina a zinthu zili pa cithunzi zili ndi mvekelo izi ;

  /mph/, /nth/, / mny/, / ngw/, /nch/

  Mphika nthoci mnyamata mphonda ngwee

- Sonyezani kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

  Citsanzo:

  Mphika – miphika

  Nyumba – manyumba

- Apange maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

  Zocita:

  Pangani maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

  1. Mtsikana – atsikana
  2. Mnyamata - anyamata
  3. Mtengo – mitengo

Muyeso Woyembekezeleka: Maina oculukitsidwa apangidwa moyenela.

Nchito B: Kupanga maina osaculuka kucokela ku maina oculuka.

I. Mphunzitsi:

- Gwilitsani nchito mtsikana, mnyamata ndi mtengo kuphunzitsa phunzilo ili.

- Pelekani citsanzo cosonyeza kupanga maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

  Citsanzo:

  1. Atsikana – mtsikana
  2. Anyamata – mnyamata
  3. Mitengo – mtengo

  - Uzani aphunzi apange maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa m'magulu. Thandizani aphunzi.

II. Aphunzi :

- Achule maina; mtsikana, mnyamata, mtengo.
- Aphunzi achule maina oculukitsidwa.
- Apange maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

Zocita:

Pangani maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

1. Magalimoto - _____
2. Masukulu - _____
3. **Makapu** - _____

Muyeso Woyembekezeleka: Maina osaculukitsidwa apangidwa moyenela.

Nchito C : Kulinganiza maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.

I. Mphunzitsi:

- Sonyezani zithunzi za zinthu zoculukitsidwa ndi zoculukitsidwa.
- Uzani aphunzi achule maina.

miphika, anyamata, mabuku.

- Sonyezani kulinganiza cinthunzi cimodzi ndi zambili.
- Uzani aphunzi atenge cithunzi ca nyumba ca fulashi khadi ndikupita kukaika pa cithunzi ca manyumba. Alinganize tele zinthu zonse.

II. Aphunzi :

- Aone zithunzi zoculukitsidwa ndi zosaculukitsidwa.
- Achule maina.
- Atsatile kulinganiza kwa cithunzi cimodzi ndi zambili kwa Mphunzitsi.
- Alinganize cithunzi cimodzi ndi zambili.
- Atenge cithunzi ca nyumba ca fulashi khadi ndikupita kukaika pa cithunzi ca manyumba. Alinganize tele zinthu zonse.

Zocita:

Linganizani maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa.

1. Munthu - anthu
2. Mwana - midzi
3. Mlendo - acona
4. Cona - ana
5. Mudzi - alendo

Muyeso Woyembekezeleka: Maina osaculukitsidwa alinganizidwa ndi maina oculukitsidwa moyenela.

Nchito D : Kusewela masewela a maina osaculukitsidwa kapena oculukitsidwa.

I. Mphunzitsi :

- Gawilani aphunzi mafulashi khadi ali ndi maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa osiyana siyana.

- Welengani maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa .
- Sewela masewela a maina osaculukitsidwa kapena oculukitsidwa. Mukachula liu la dzina losaculukitsidwa , gulu limodzi lipeleke yankho la dzina loculukitsidwa. Mupeleke mamalikisi pa yankho lilonse loyenela.Gulu limene lidzatenga mamalikisi yambili, lapamba masewela.

II. Aphunzi:

- Apenye mau ali pa mafulashi khadi osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa.
- Awelenge maina osaculukitsidwa ndi oculukitsidwa.
- Asewele masewela m'magulu.

Muyeso Woyembekezeleka: Kusewela masewela a maina osaculukitsidwa kapena osaculukitsidwa kwacitika moyenela.

Cidule: Mutu uyu unali kuona pakupanga, kulinganiza, kusewela masewela a maina oculukitsidwa ndi osaculukitsidwa.

MVETSELO

Mutu 1: Mvetselo

Mutu Waung'ono 1: Mfundo Yaikulu.

Lambulo: Mutuyu udzaona pa mfundo yaikulu, kupfupikitsa nkhani, kuzindikila lingalilo ndi coona ca nkhani.

Luso lapadela: Kuzindikila ndi kufotokoza mfundo yaikulu pa uthenga omwe amva.

Zida Zophunzilila ndi Kuphunzilila: Mabuku owelenga, mafulashi khadi.

Mau ofunika kudziwa: Nkhani, zoona, uthenga, maganizo.

Mfundo Zophunzitsa

- Kuzindikila mfundo yaikulu.
- kufotokoza mfundo yaikulu.

 **Nchito A:** Kuzindikila ndi kufotokoza mfundo yaikulu pa uthenga omwe amva.

I. Mphunzitsi :

- Fotokozan nkhani yaipfupi.

Chalesi ndi mwana omvela. Amatsatila zolankhula wamkulu. Cifukwa ca ici, amalume ake anamgulila njinga. Amakwela popita kusukulu ndi ku chalichi.

- Funsani mafunso osiyana siyana monga , anali mwana womvela ndani?
- Uzani aphunzi afotokoze zomwe amva pa nkhani.
- Funsani aphunzi afotokoze mfundo yaikulu pa nkhani.

II. Aphunzi :

- Amvetsele ku nkhani yaipfupi.
- Afotokoze zomwe amva pa nkhani.
- Ayankhe mafunso osiyana siyana monga, anali mwana womvela ndi Chalesi.
- Afotokoze mfundo yaikulu pa nkhani.

Zocita:

Tsilizani ziganizo izi.

1. _____ anali mwana womvela.
2. Anamgulila njinga a _____ ake.
3. Amakwele njinga popita ku ____ ndi ku chalichi.

Muyeso woyembekezeleka: Mfundo yaikulu yazindikilidwa ndi kufotokozedwa moyenela.

Nchito B: Kupfupikitsa uthenga.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani cithunzi ca mnyamata ali ndi njinga.
- Funsani aphunzi zimene aona pa cithunzi.
- Welengani nkhani iyi.
  Chalesi ndi mwana omvela. Amatsatila zolankhula wamkulu. Cifukwa ca ici, amalume ake anamgulila njinga. Amakwela popita kusukulu ndi ku chalichi.
- Uzani aphunzi awelenge.
- Fotokozani mfundo yaikulu.

II. Aphunzi :

- Apenye pa cithunzi ca mnyamata ali ndi njinga.
- Akambe zimene aona pa cithunzi.
- Amvetsele ku khani.
- Awelenge nkhani.
- Azindikile mfundo yaikulu.

Muyeso Woyembekezeleka: Uthenga wapfupikitsidwa moyenela.

Mutu Waung'ono 2 : Coona ndi Lingalilo

Luso Lapadela : Kusiyanitsa coona ndi lingalilo

Nchito A: Kuzindikila lingalilo la nkhani

I. Mphunzitsi :

- Onetsani zinthu monga buku, cola, delesi ndi nsapato.
- Mufotokoze kuti delesi ili ndi la maonekedwe abwino kwambili dziko lonse.

- Fotokozani kuti ao ndi lingalilo cabe cifukwa kuli madelesi ena opambana maonekedwe a delesi ilo.
  Mucite tele ndi buku, cola ndi nsapato.
- Welengani nkhani.
- Funsani aphunzi kuti apeze mau oonetsa malingalilo cabe.

II. Aphunzi :

- Aone zinthu monga buku, cola, delesi ndi nsapato.
- Amvetsele kuzofotokoza za maonekedwe a delesi.
- Amvetsele ku zofokoza kuti ndi lingalilo cabe limene mphunzitsi wanena, cifukwa kuli madelesi ena opambana maonekedwe a delesi ilo.
- Awelenge nkhani.
- Apeze mau kapena ziganizo zoonetsa malingalilo cabe.

Zocita:

M’magulu, awelenge nkhani ndi kupeza mau kapena ziganizo zoonetsa malingalilo cabe.

Muyeso Woyembekezeleka: Lingalilo mu nkhani lazindikilidwa moyenela.

 **Nchito B:** Kuzindikila coona mu nkhani

I. Mphunzitsi :

- Uzani aphunzi awelenge ziganizo zili pa chati.
  1. Galu ali ndi miyendo anai (4).
  2. Nyumba ili ndi khomo.
- Mufotokoze kuti izi ndi zoona ndipo ndi zooneka ndi maso.
- Uzani aphunzi akambe zoona zina.
- Welengani nkhani mu buku lowelenga.

- Funsani aphunzi kuti apeze zonena zoona.

II. Aphunzi :

- Awelenge ziganizo zili pa chati.

  Galu ali ndi miyendo anai (4).

  Nyumba ili ndi khomo.

- Amvetsele kufotokoza kwa mphunzitsi kuti ziganizo zifotokoza zoona.
- Akambe zoona zina.
- Awelenge nkhani mu buku lowelenga.
- Apeze zonena zoona zili mu nkhani.

Zocita:

Aphunzi awelenge nkhani ndi kupeza ziganizo zonena zoona mu nkhani zwili (2).

**Mwacidule:** Mutuyu unali kuona pa mfundo yaikulu, kupfupikitsa nkhani, kuzindikila lingalilo ndi coona ca nkhani.

Mutu 2 : Mvetso

Mutu Waung'ono : Coona Ca Nkhani

**Ciyambi:** Mutuyu udzaona pa coona ca nkhani., kufotokoza zomwe zawelengedwa, kuyankha mafunso ndi kufotokoza mwatsatane tsatane zomwe zinacitika mu nkhani.

Luso lapadela : Kupeleka uthenga wapapfupi omwe wafotokozedwa mu nkhani . (mu ziganizo ziwili (2) kapena zitatu (3)).

Zida Zophunzitsila ndi Kuphunzilila: Chati, mafulashi khadi.



Mau Ofunika kudziwa: Nkhani, kolela, zinyalala, nkhando, zapapfupi.

Mfundo yophunzitsa

- Kufotokoza zomwe zawelengedwa.

 **Nchito A:** Kufotokoza zomwe zawelengedwa.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani cithunzi ca nchenche.
- Uzani aphunzi afotokoze zimene aona.
- Welengani nkhani.
  Nchenche ikonda kukhala pa malo aubve monga a zinyalala. Anthu afunika kutentha zinyalala, kutaya mu bini ndi mu nkhando. Ici cithandiza kupewa matenda monga a kolela.
- Funsani mafunso pa nkhani yawelengedwa.
- Auzeni aphunzi afotokoze zomwe zawelengedwa.

II. Aphunzi:

- Apenye zili pa cithunzi.
- Afotokoze zimene aona.
- Amvetsele ku nkhani.
- Ayankhe mafunso pa nkhani yawelengedwa.
- Afotokoze zomwe zawelengedwa.

Zocita:

Jambula cithunzi ca nchenche ndi kulemba ziganizo ziwili za papfupi.

Muyeso woyembekezeleka: Uthenga wowelengedwa wafotokozedwa moyenela.

 **Nchito B:** Kuyankha mafunso pa zomwe zawelengedwa.

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani.
  Nchenche ikonda kukhala pa malo aubve monga a zinyalala. Anthu afunika kutentha zinyalala, kutaya mu bini ndi mu nkhando. Ici cithandiza kupewa matenda monga a kolela.
- Funsani mafunso monga mwamvapo ciani pa nkhani? Ndi ciani cikonda kukhala pa malo aubve? Nanga matenda a kolela angapewedwe bwanji?
- Awelenge nkhani mu buku lowelenga la mphuzi.

II. Aphunzi:

- Awelenge nkhani.
- Ayankhe mafunso yofunsidwa ndi mphunzitsi.
- Awelenge nkhani mu buku lowelenga la mphuzi.

Zocita:

Yankhani mafunso

1. Kodi nchenche ikonda kukhala pa malo otani?
2. Chula malo komwe zinyalala zifunika kutidwa.
3. Ndi matenda otani angapewedwe?

Muyeso oyembekezeleka: Mafunso ayankhidwa moyenela.

 **Nchito C :** Kufotokoza mwatsatane tsatane momwe zinacitikila mu nkhani.

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani.

Kuphika zitumbuwa ndi cinthu cosabvuta. Zofunika kuti muphike zitumbuwa ndi ufa wa fulaulo, mafuta ophikila, shuga, mcele ndi isiti. Mungagule izi ku sitolo.

- Funsani aphunzi mafunso.
- Auzeni afotokoze mwatsatane tsatane zinthu zomwe zifunika kuphika zitumbuwa.
- Uzani aphunzi amvetsele ku nkhani yowelengedwa.

  Kupanga galimoto loseweletsa ndi cinthu cosabvuta. Zofunika kuti mupange galimoto ili ndi botolo la pulasitiki monga momwe munali maheu, tubwinikililo ndi waya waung'ono.
- Funsani aphunzi mafunso osiyana siyana.
- Auzeni afotokoze mwatsatane tsatane zinthu zomwe zifunika kupanga

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani yowelengedwa.
- Ayankhe mafunso.
- Afotokoze mwatsatane tsatane zinthu zomwe zifunika kupanga galimoto loseweletsa.

Zocita:

Yankhani mafunso awa.

1.Jambula galimoto.

2. Lemba zinthu zomwe zifunika kupanga galimoto la mawaya.

Muyeso Woyembekezeleka: Zocitika mu nkhani zafotokozedwa mwatsatane tsatane.

Cidule: Mutuyu unali kuona pa zoona zili mu nkhani, kufotokoza zomwe zawelengedwa, kuyankha mafunso ndi kufotokoza mwatsatane tsatane zomwe zinacitika mu nkhani.

KULEMBA

Mutu 1: Malembedwe

Mutu Waung'ono 1: Kulemba Malembo

**Ciyambi:** Mutuyu udzaona pakujambula ndi kulemba malembo. Kulemba mau ndi ziganizo mu malembo okhazikika. Kulemba ziganizo mosiya mpata pakati pa mau.

Luso lapadela: Kulemba malembo

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Chati la malembo, chati la mau, chati la ziganizo, mafulashi khadi.

**Mau Ofunika Kudziwa:** Kulemba**,** malembo, aliphabeti, kumwamba, pansi.

Mfundo yophunzitsa

- Malembedwe a malembo akuluakulu.

**Nchito A :** Kujambula malembo.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani chati la malembedwe oyenela a malembo akuluakulu.
- Lembani pa bolodi.
- Uzani aphunzi alembe lembo limodzi limodzi kulondola m'mene mulembela. *Zindikilani kuthandiza aphunzi ali ndi bvuto pa malembedwe oyenela.*

II. **Aphunzi:**

- Apenyetsetse malembo ali pa chati.
- Apenyetsetse malembedwe ya mphunzitsi pa bolodi.
- Alembe lembo limodzi limodzi kulondola m'mene Mphunzints alembela.

Zocita:

1.Lembani malembo akulu akulu.

A B C D E F G H I J K L M N O P Q R S T U V W X Y Z

Muyeso woyembekezeleka: Malembo ajambulidwa ndi kulembedwa moyenela**.**

 **Nchito B :** Kulemba malembo

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi aimbe nyimbo ya mavawelo iliyonse.
- Pelekani citsanzo colemba malembo ang'ono ang'ono ya aliphabeti.Aphunzi apenyelele ndi kulemba malembedwe oyenela a malembo.

  a b c d e f g h I j k l m n o p q r s t u v w.

  Penyelelani m'mene alembela aphunzi.Athandizeni.
- Lembani malembo ali ndi micila yopita pansi.Fotokozani malembedwe ake ndipo aphunzi amalembedwe.

  g j p q y
- Lembani malembo yali ndi micila yopita kumwamba.Aphunzi alembe.

  K h b l t

  ZINDIKILANI : kuti muyenela kupenyelela ndi kuthandiza aphunzi kulemba malembo moyenela.Malembo ayenela kukhazikika pa mzele.

II. Aphunzi:

- Aimbe nyimbo ya mavawelo iliyonse.
- Apenyelele citsanzo colemba malembo ang'ono ang'ono ya aliphabeti ya apa kesi (lower case).
- Alembe malembo moyenela.

  a b c d e f g h I j k l m n o p q r s t u v w.

  Penyelelani m'mene alembela aphunzi.Athandizeni.
- Apenyelele malembedwe a malembo ali ndi micila yopita pansi ndipo alembe.

  g j p q y
- Apenyelele malembewe a malembo ali ndi micila yopita kumwamba ndipo alembe.

K h b l t

Zindikilani kuti muyenela kupenyelela ndi kuthandiza aphunzi kulemba malembo moyenela.Malembo ayenela kukhazikika pa mzele.

Zocita:

1. Lembani malembo ali ndi micila yopita pansi.
2. Lembani malembo ali ndi micila yopita kumwamba.

Mayankho:

1. **g j p q y**
2. **k h b l t**

Muyeso Woyembekezeleka: Malembo alembedwa moyenela.

Mutu Waung'ono 2: Malembedwe okhazikika

Nchito : Kulemba mau yooneka ndi yowelengeka mosabvuta m'malembedwe okhazikika.

I. **Mphunzitsi:**

- Onetsani chati yomwe ili ndi mau olembedwa mobvuta kuwelenga.
- Onetsani cati lili ndi mau olembedwa moyenela.
- Funsani aphunzi zamalembedwe amenewa.
- Fotokozani malembedwe oyenela, amalembo otayana ndi okhazikika.
- Uzani aphunzi alembe ndipo muyang'anile malembedwe ao.
- Lembani ciganizo molongosoka.
- Uzani aphunzi naonso alembe mau ndi ciganizo molongosoka.

II. Aphunzi:

- Apenye pa chati ili ndi mau olembedwa mobvuta kuwelenga.
- Afotokoze zamalembedwe awa.
- Apenye pa cati ili ndi mau olembedwa moyenela.
- Afotokoze zamalembedwe amenewa.
- Amvetsele ndi kupenyetsetsa malembedwe oyenela amalembo otayana a okhazikika.
- Alembe ndipo mphunzitsi ayang'anile malembedwe ao.

Zocita:

Lembani mau awa moyenela. Malembo muyalembe motayana.

1. Balalika
2. Chadiza
3. Gulugufe
4. Nyani
5. Phulantenga

Muyeso Woyembekezeleka: Mau alembedwa mokhazikika moyenela.

Mutu Waung'ono 3: Mipata ya mau

 **Nchito D :** Kulemba mau mosiya mpata.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani chati lili ndi malembedwe osasiya mpata.

  Citsanzo:

  Ganizaniwapitakukaonaagogo.
- Welengani ciganizo.
- Uzani aphunzi awelenge.
- Funsani zolakwika.
- Fotokozani malembedwe oyenela osiya mpata pakati pa mau.

- Lembani ciganizo moyenela.
- Patsani ziganizo zolembedwa mosasiya mpata pakati pa mau ku aphunzi m’magulu.
- Auzeni alembe molongosoka.

II. Aphunzi:

- Onetsani chati lili ndi malembedwe osasiya mpata.
- Welengani ciganizo.
- Uzani aphunzi awelenge.
- Funsani zolakwika.
- Fotokozani malembedwe oyenela osiya mpata pakati pa mau.
- Lembani ciganizo moyenela.
- Patsani ziganizo zolembedwa mosasiya mpata pakati pa mau ku aphunzi m’magulu.
- Auzeni alembe molongosoka.

Zocita:

Lembani ziganizo ndi kusiya mipata.

1. Mphunzitsiwalowamkalasi.
2. Amalumeakwelanjinga.

Muyeso Woyembekezeleka: Ziganizo zalembedwa ndi mipata yasiyidwa moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pakujambula ndi kulemba malembo.Kulemba mau ndi ziganizo mokhazikika. Kulemba ziganizo mosiya mpata pakati pa mau.

KULEMBA

Mutu 1: Cimangilizo

Mutu Waung’ono 1: Kujambula

Ciyambi: Mutuyu udzaona pakufotokoza maganizo kupyolela mu kujambula.

Luso lapadela: Kufotokoza maganizo kupyolela mu kujambula.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: ZIthunzi.

**Mau Ofunika Kudziwa:** Nkhani, kujambula, kufotokoza.

Mfundo yophunzitsa

- Kujambula zithunzi.

**Nchito A :** Kujambula zocitika kupanga nkhani.

I. **Mphunzitsi:**

- Kambani nkhani yaipfupi.
- Funsani aphunzi akambe nkhani ziwili zazipfupi.
- Fotokozani kuti nkhani zingakambidwe kugwilitsa nchito zithunzi.
- Onetsani zithunzi zinai (4) za nkhani.
- Welengani nkhani ndipo aphunzi aike zithunzi mundondomeko yolondola tsatane-tsatane wa nkhani.
- Aphunzi jambule zithunzi kutsatila nkhani.

II. **Aphunzi :**

- Amvetsele ku nkhani yaipfupi.
- Akambe nkhani ziwili zazipfupi.
- Amvetsele kufotokoza kwa Mphunzitsi pa kalembedwe ka nkhani kugwilitsa nchito zithunzi.
- Apenye zithunzi zinai (4) za nkhani.
- Awelenge nkhani ndipo aphunzi aike zithunzi mundondomeko yolondola tsatane-tsatane wa nkhani.
- Ajambule zithunzi kutsatila nkhani.

Zocita:

Pangani nkhani pakujambula zithunzi.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula kwacitika moyenela.

 **Mwacidule:** Mutuyu unali kuona pakufotokoza maganizo kupyolela mu kujambula.

CAPAMUTU 5 KUMVETSELA NDI KULANKHULA

Mutu: Zilapi ndi mau opinda lilime (Tongue Twisters)

Mutu waung'ono: Mau opinda lilime (Tongue twisters)

 **Ciyambi**: Mutu waung'ono uyu udzaona pa mau opinda lilime, malankhulidwe ake ndi zolinga zosiyana-siyana za mau opinda lilime.

Luso lapadela: Kuloweza mau opinda lilime

 **Mau ofunika kudziwa**: Zilapi, kupinda, lilime, kuloweza, kuceza, kufulumila, tanthauzo, kulondola, kuthandiza, luso, zosangalatsa.

Zida zophunzitsila ndi zophunzilila: Mabuku a aphunzi, mabuku a zilapi ndi a mau opinda lilime .

Mfundo Yophunzitsa:

- Kuphunzitsa aphunzi mau opinda lilime ndi malowezedwe ake.

 **Nchito :** Kuloweza Ndi Kubwezela Kunena Mau Opindika Lilime .

I . Mphunzitsi:

- Lankhulani ciganizo ca mau opinda lilime modekha kwa aphunzi ndipo muwafunse zomwe amvapo.
- Bwezani kunena ciganizoco mofulumila ndi Kufunsanso aphunzi zomwe amvapo.
- Fotokozani tanthauzo la mau opinda lilime kwa aphunzi

1. Mau opinda lilime ndi ziganizo zopangidwa kukhala zobvuta kalankhula mofulumila ndi molondola mau cifukwa ca kufanana kwa mamvekedwe a mau m'ziganizozo.

2. Mau opinda lilime amagwilitsidwa nchito kukhala masewela a mau, kuphunzila kulankhula, kuceza ndi zosangalatsa.

3. Yamathandiza kupititsa patsogolo maluso a kachulidwe ka mau, kuwelenga mofulumila ndi kulankhula zofunika kulemba.

4. Lankhulani ciganizo ca mau opinda lilime cimodzi mofulumila ndi kuuza aphunzi kuti acilankhulenso mofulumila.

Citsanzo:

Mnkhwele wamankhwala wagwa mphwai ndi kutaya mnkhwani pomva mtswatswa wa nkhwali mnkhalango.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ndi kukambilana momwe aphunzitsi alankhulila mau opinda lilime.
- Ayamikile zolankhula aphunzitsi.
- Ayetselele Kulankhula mau opindika lilime.
- Alankhule mau opinda lilime osiyana-siyana m'magulu.

Zocita:

Kambilanani mau opindika lilime osiyana-siyana m'magulu anu.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuloweza ndi kubweleza kunena mau opinda lilime kwacitika moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa mau opinda lilime, malankhulidwe ake ndi zolinga zosiyana-siyana za mau opinda lilime.

KUWELENGA

Mutu: Kuzindikila Masilabe

Mutu waung'ono : Kuzindikila Masilbe opangidwa ndi malemba awa; **mts--, mdz-, mkw-, phw- , thy**- , m'mau okambidwa.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

Mtsa mtse mtsi mtso mtsu.

**Ciyam**bi: Mutu uyu udzaona pakupanga Masilabe kucokela ku mau okambidwa ,kusewela masewela akuwelenga Masilabe omwe ali mu mau pakuomba m'manja ndi masewela akupanga mau ena pakusintha ndi kucotsa Masilabe kupanga mau atsopano.

Luso Lapadela: Kuzindikila Masilabe m'mau olankhulidwa.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: fulashi khadi, chati ya Masilabe.

**Mau Ofunikila Kudziwa:** Masilabe, vawelo, Mfundo zophunzitsa .

Mfundo zophunzitsa:

- Kuzindikila Masilabe m'mau okambidwa
- Kutsewela masewela owelenga nambala ya Masilabe mliu

**Nchito A: Kuzindikila Masilabe m'mau okambidwa (mts, mdz, phw, mkw, thy)**

I. Mphunzitsi:

- Nenani mau

- Funsani aphunzi Masilabe omwe apezeka mu mau okambidwa.
- Sonyezani Masilabe omwe apezeka m'mau okambidwa

Citsanzo:

1. Mtsikana ---- mtsi / ka /na (Masilabe atatu)

II. Aphunzi :

- Amvetsele ku mau okambidwa
- Apeze Masilabe m'mau okambidwa m'magulu ao
- Azindikile Masilabe m'mau okambidwa m'magulu awili-awili.

 **Zocita:**

Pezani Masilabe m'mau awa okambidwa.

1. Mtsuko

2. Mtsasa

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila Masilabe mu Mau okambidwa kwacitika moyenela

 **Nchito B: Kusewela masewela owelenga nambala ya Masilabe mliu (mts, mdz, mkw, phw, thy)**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Nenani mau
- Citani ndi kusonyeza mocitila masewela osiyana-siyana akupanga Masilabe.

Citsanzo:

Kumtsekela = ku --ombani m'manja, mtse --ombani m'manja, ka --ombaninso m'manja-pamodzi aphunzi azaomba katatu

- Udzani aphunzi kuti aombe m'manja akazindikila silabe mliu

1. Mdzandipeza = /mdza/, /ndi/ , /pe/, /za/= kuomba m'manja kanai.

2. Mdzukulu = /mdzu/,/ku/,/lu/. = kuomba m'manja katatu

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku mau
- Acite masewela osiyana-siyana akupanga ndi Kudzindikila Masilabe pakuomba m'manja.
- Aombe m'manja akamva silabe ndi kuwelenga nambala ya Masilabe mliu.
- Acite masewela awa m'magulu awili- awili.

 **Zocita:**

Lembani nambala ya Masilabe mliu.

1. Mdzathu

2. Ndimdziwa

Muyeso Woyembekezeleka: Kusewela masewela akuwelenga masilabe mliu pakuomba m'manja kwacitika moyenela

 **Nchito C: Kupanga mau okambidwa kugwilitsa nchito Masilabe—(mts , mdz, mkw, thy phw)**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Pelekani zitsanzo zolumikidza Masilabe ndi kupanga mau okambidwa.

Citsanzo:

1. Thyo / ka/ ipanga thyoka

2. Mkwe / kwe / sa/ apanga mkwekwesa

II. Aphunzi:

- Aonelele zitsanzo zopelekedwa ndi Mphunzitsi.
- Alumikize Masilabe kupanga mau okambidwa.

 **Zocita:**

Lumikizani Masilabe awa kupanga mau okambidwa.

1. /Thyo/, /ke /,/la/ apanga ----------

2. /Ci/, / thye/, /thye/ apanga----------

Muyeso Woyembekezeleka: Kupanga mau olankhulidwa kugwilitsa nchito masilabe kwacitika moyenela

 **Nchito D: Kusewela Masewela A Kucotsa Silabe Ku Liu Ndi Kuikako Ina Kupanga Mau Atsopano ---mts , mdz, mkw, thy phw.**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi :

- Nenani mau
- Onetselani kucotsa silabe ndi kuikako Ina kupanga mau atsopano.

Zitsanzo:

1. Kanya = phwanya = cotsani /ka/ ikani / phwa/

2. Switi = phwiti = cotsani /swi/ ikani /phwi/ .

II. Aphunzi :

- Amvetsele mau kucokela kwa mphunzitsi .
- Ayeselele kupanga mau atsopano pakucotsa silabe ndi kuikako Ina.

 **Zocita:**

Pangani mau ena atsopano pakucotsa silabe ndi kuikako Ina.

1. Ngwee = phwee = cotsani /Ngwe/ ikani /phwe/.

2. Waphwanya = ndaphwanya = cotsani /wa/ ikani /nda/.

Muyeso Woyembekezeleka: Kucita masewela a kucotsa silabe ku Liu ndi kuikako Ina kupanga mau atsopano kwacitidwa moyenela.

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pakupanga Masilabe kucokela ku mau okambidwa ,kusewela masewela akuwelenga Masilabe omwe ali mu mau pakuomba m'manja ndi masewela akupanga mau ena pakusintha ndi kucotsa Masilabe kupanga mau atsopano.

Mutu 2 : Ubale wa Lembo ndi Mvekelo.

Mutu waung'ono 1 : Masilabe ---mts , mdz, mkw, thy phw.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

 **Ciyambi :** Mutu uyu udzaona pa Kulumikiza makonsonanti ndi mavawelo kupanga Masilabe, kuwelenga silabiki chati, kusankha Masilabe kucoka m'mau, kusinthanitsa malembo kupanga mau ndi Kulumikiza gulu la makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

 **Mau Ofunika Kudziwa** : Masilabe , makonsonanti, mavawelo.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: mafulashi khadi, chati ya Masilabe.

Mfundo Zophunzitsa :

- Kupanga masilabe polumikiza makonsonanti ndi mavawelo.
- Kuwelenga Masilabe opangidwa.

 **Nchito A: Kupanga Masilabe Pa kulumikiza Makonsonanti Ndi Mavawelo. ---mts , mdz, mkw, thy phw.**

I. Mphunzitsi:

- Lembani mvekelo la tsiku ndi mavawelo
- Sonyezani kulumikiza mavawelo ku makonsonanti opatsidwa kupanga Masilabe.

Zitsanzo :

a e i o u

/Mkw/ = mkwa mkwe mkwi mkwo mkwu

II. Aphunzi:

- Aone mvekelo la tsiku lolembedwa.

- Apange Masilabe polumikidza malembo ndi mavawelo m’magulu ao polondola citsanzo kucokela kwa mphunzitsi.

 **Zocita:**

Pangani Masilabe pogwilitsa nchito mamvekelo ndi mavawelo opatsidwa .

a e i o u

1. /mts/ =

2. /mkw/ =

Masilabe apangidwa kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo moyenela.

 N**chito B: Kuwelenga silabiki chati---mts , mdz, mkw, thy phw.**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Onetsani chati ya masilabe kwa aphunzi.
- Sonyezani mawelengedwe a Masilabe pa chati.
- Udzani aphunzi kuti awelenge Masilabe ya pa chati.

Citsanzo

	a	e	i	o	u
Mts	Mtsa	Mtse	Mtsi	Mtso	Mtsu

I. Aphunzi :

- Aone chati ya Masilabe
- Awelenge Masilabe kucokela pa silabiki chati.
- Acite izi m'magulu ao kapena awili-awili.

 **Zocita:**

Welengani silabiki chati m'magulu

Muyeso Woyembekezeleka : Kuwelenga silabiki chati kwacitidwa moyenela.

 **Nchito C: Kusankha Kapena Kupeza Masilabe Kucokela Ku Mau. ---mts , mdz, mkw, thy phw.**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi :

- Konzekelani mau pa mafulashi khadi
- Sonyezani aphunzi momwe angathe Kuzindikila Masilabe.

Citsanzo:

1. Mdzikoli = /mdzi/,/ko/, /li /= muli Masilabe atatu

II. Aphunzi :

- Azindikile Masilabe ali mau
- Anene Masilabe amene apezeka m'mau

 **Zocita:**

Zindikilani Masilabe omwe ali m’mau awa.

1. Phwanyika

2. Waphwanya

Muyeso Woyembekezeleka : Kusankha Masilabe Kucokela M’mau Kwacitika Moyenela.

Nchito D: Kucotsa Silabe La Mau Ndi Kuikako Ina.(Letter Substitution) ---mts , mdz, mkw, thy phw.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amalemba amodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi :

- Nenani mau
- Sonyezani kucotsa lembo ku mau ndi kuikako Lina.

Zitsanzo:

1. Waphwanya = taphwanya = cotsani /w/ ikani /t/

2. Phwiti = switi = cotsani /ph/ ikani /s/

II. **Aphunzi :**

- Amvetsele ku mau okambidwa ndi mphunzitsi
- Acotse lembo ku mau ndi kuikako Ina kupanga mau atsopano

Zocita:

Cotsani lembo loyambilila ku mau ndi kuikako Ina kupanga mau atsopano.

1. Mdzathu

2. Mdzakhala

3. Mdzabwela

Muyeso Woyembekezeleka: Kucotsa lembo ku mau kuikako Ina kupanga mau atsopano kwacitidwa moyenela

NCHITO E: Kulumikiza Malembo Ophatikizana Amakonsonanti Koma Amamvekedwe osiyana Ndi Mavawelo Kupanga Masilabe. ---mts , mdz, mkw, thy phw.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi :

- Lembani makonsonanti ophatikizana pa bolodi.
- Sonyezani Kulumikiza makonsonanti ophatikizana ndi mavawelo kupanga Masilabe.

Citsanzo:

a e i o u

Mkwa mkwe mkwi mkwo mkwu

Phwa phwe phwi phwo phwu

II. Aphunzi :

- Amvesele ndi kuona makonsonanti ophatikizana omwe alembedwa pa bolodi
- Alumikize makonsonanti ophatikizana aja ndi masilabe m'magulu ao.

Zocita:

Lumikizani makonsonanti ophatikizana awa ndi mavawelo kuti mupange Masilabe.

a e i o u

1. Mkw
2. Phw

Muyeso Woyembekezeleka : Kulumikiza makonsonanti ophatikizana ndi mavawelo kupanga Masilabe kwacitika moyenela.

MUTU 2 : Kupanga Mau

Mutu Waung'ono 2: Mau **---mts- , mdz-, mkw-, thy-, phw-.**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse masilabe opangidwa ndi malembo ali pamwambapa imodzi –imodzi mpaka onse atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila masilabe opangidwa ndi **mts- mtsa, mtse, mtsi, mtso, mtsu**

 **Ciyambi**: Mutu waung'ono uyu udzaona pa Kulumikiza masilabe kupanga mau, masewela akusintha ndi kucotsa masilabe kupanga mau, Kuzindikila Masilabe m'mau.

Luso Lapadela: Kulumikiza masilabe kupanga mau.

 **Mau Ofunikila Kudziwa:** Masilabe, mau

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Chati ya Masilabe, fulashi khadi

Mfundo Zophunzitsa:

- Kulumikiza masilabe
- Kusintha ndi kucotsa Masilabe kupanga mau.

Nchito A: Kulumikiza Masilabe Kupanga Mau. ---mts , mdz, mkw, thy phw.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Lembani masilabe
- Sonyezani kulumikiza Masilabe kupanga mau

Zitsanzo:

mtsa/ na apanga **mtsana**

mtsi, / ka / / na / ipanga **mtsikana**

II. Aphunzi :

- Apenyelele molumikidzila Masilabe kupanga mau.
- Alumikize Masilabe opatsidwa kupanga mau m'magulu ao.

Zocita: Lumikizani Masilabe awa ndi kupanga mau

1. Mtsa + sa =
2. Mtsi + ka + na =
3. mtsa+ na =
4. Mtso + nyo

Muyeso Woyembekezeleka : Kulumikiza masilabe kupanga mau kwacitika moyenela.

Nchito B: kusintha Masilabe kuikako ena kupanga mau atsopano. . ---mts , mdz, mkw, thy phw.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Konzekelani mau pa mafulashi khadi
- Funsani aphunzi kusintha silabe loyamba kapena laciwili kuikapo Ina kupanga mau atsopano

Zitsanzo:

1. Mtsikana = kukana --- cotsani /mtsi/ ikani /ku/

2. Mdzinja = manja --- cotsani /mdzi/ ikani /ma/

II. Aphunzi :

- Aone zomwe aphunzitsi ao ali kucita
- Naonso m'magulu ao asinthe silabe ndi kuikapo Ina kupanga mau atsopano

**Zocita:**

Pangani mau atsopano pakucotsa silabe ndi kuikapo Ina.

1. Mdzathu

2. Mdzukulu

3. Thyola

Muyeso Woyembekezeleka : Kusintha masilabe ku mau kuikapo ena kupanga mau atsopano kwacitika moyenela.



Nchito C: Kuzindikila Masilabe Mu Mau. ---mts , mdz, mkw, thy phw.

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Onetsani mau omwe alembedwa pa mafulashi khadi
- Funsani aphunzi kuti aombe m'manja pakuzindikila Masilabe m'mau opatsidwa

Zitsanzo:

1. Mtsuko = /mtsu/ ombani m'manja, /ko/ ombani m'manja . Pamodzi muzaomba m'manja kawili.

2. Phwando = /phwa/ ombani m'manja, /ndo/ ombani m'manja. Pamodzi muzaomba m'manja kawili.

II. Aphunzi :

- Awelenge mau opatsidwa.
- Azindikile Masilabe m'mau
- Aombe m'manja kulingana ndi Masilabe ali m'mau.



Zocita:

Zindikilani ndi kulemba Masilabe omwe ali m'mau awa.

1. Phwanyika

2. Phwetekele

3. Thyokela

Muyeso Woyembekezeleka : Kuzindikila Masilabe m'mau kwacitika moyenela.

Nchito D: Kuwelenga Masilabe M’mau .

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse Masilabe amvekelo imodzi mpaka onse oonetsedwa pamwambapa atatha. Munsimu mwaonetsedwa mophunzitsila Masilabe

I. Mphunzitsi:

- Konzekelani mau pa mafulashi khadi
- Funsani aphunzi kuti awelenge Masilabe omwe ali m’mau

Zitsanzo:

1.mdzabwela = mdza + bwe + la = Masilabe atatu

2. Ndimdziwa = ndi + mdzi + wa = Masilabe atatu

II. Aphunzi:

- Apenyelele zomwe aphunzitsi Ali kucita
- Awelenge ndi kupeza nambala ya Masilabe omwe ili m’mau m’magulu ao.



Zocita:

Welengani manambala amasilabe omwe apezeka m’mau opatsidwa.

1. Mtsikana

2. Mdzukulu

3. kumtseka

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga nambala ya Masilabe kucokela m’mau opatsidwa kwacitika moyenela.

 **Mwacidule :** Mutu uyu unali kuona pa mvekelo la lembo, kuzindikila ndi kupeza lembo, kulumikiza lembo ndi vawelo kupanga silabe, kulumikiza Masilabe kupanga mau, komanso kuwelenga nambala ya Masilabe m'mau.

MUTU 3: KUWELENGA MOFULUMILA

 **Nchito B: kuwelenga mau**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse mau omwe ali ndi mvekelo mts, mdz,mkw,thy,phw. Yetsesani kuti aphunzi akwanilitse kuwelenga mau awa popanda bvuto lililonse.

I. Mphunzitsi:

- Nenani mau
- Lembani mau pa chati kapena pabolodi ndi sonyeza kuwelengele aphunzi polondola mawelengedwe abwino (model reading)
- Udzani aphunzi kuti awelenge mau.

Zitsanzo:

1. Mtsikana
2. Phwiti
3. Inaphwanyika

II. Aphunzi:

- Awelenge mau mokuwa m'magulu ao
- Awelenge mau ndi machulidwe oyenela awili- awili.

 **Zocita:**

Welengani mau awa mokuwa ndiponso mofulumila m’magulu awili–awili

1. Thyola
2. Cithyethye
3. Anamkwiyila

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga Mau kwacitika moyenela.

 **Nchito C: Kuwelenga Ndi Kumvetsa Ziganizo. ---mts , mdz, mkw, thy phw.**

ZINDIKILANI: Mphunzitsi aphunzitse mau omwe ali ndi mvekelo mts, mdz,mkw,thy,phw. Yetsesani kuti aphunzi akwanilitse kuwelenga mau ndi ziganizo momwe mau amukati akhale ndi masilabe opangidwa ndi mvekelo zonse zopatsidwa pamwambapa.

I. Mphunzitsi:

- Lembani ziganizo pa bolodi
- Udzani aphunzi kuti awelenge ziganizo
- Funsani aphunzi kuti apeleke matanthauzo a ziganizo.

II. Aphunzi :

- Aone ziganizo zolembedwa pa bolodi.
- Awelenge ziganizo zolembedwa
- Apeleke matanthauzo a ziganizo zolembedwa.

 **Zocita:**

Pelekani matanthauzo a ziganizo izi.

1. Mtsikana Ali kuphika cakudya
2. Onani anyamata Ali kuteya mpiri wa miyendo.

3. Anyamata ndi atsikana apita kukathyola nkhuni.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga ndi kupeleka matanthauzo a ziganizo moyenela.

 **Nchito D: Kuwelenga Kankhani Ka Mizele Iwili Kapena Isanu.**

I. Mphunzitsi:

- Lambani nkhani ya cidule yokwanila mizele iwili kapena itatu
- Welengani nkhani pomwe aphunzi akulondola.
- Funsani aphunzi kuti awelenge nkhani imeneyo.

II. Aphunzi :

- Amvetsele kawelengedwe ka nkhani kucokela kuli mphunzitsi.
- Awelenge nkhani onse mkalasi
- Awelenge nkhani awili-awili.

 **Zocita:**

Welengani nkhani iyi awili- awili.

Malita ndi mwana wanzelu kwambili. Acita bwino’ kwambili mu mayeso ake. Lelo malita watenga nambala wanu mkalasi lao.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga nkhani ya cidule kwacitika moyenela.

 **Nchito E: Kuzindikila Zolembedwa Zili Ndi Mvekelo Zosiyana -Siyana Ndi malemba olumikizana (Decoding Text With Variety Of Sounds And Blends)**

I. Mphunzitsi:

- Sewenzesani makhadi Ali ndi mvekelo mts, mdz, mkw, ndi phw.

- Zindikilani mvekelo imodzi -imodzi pa nthawi.
- Udzani aphunzi kuti Achule mau Ali ndi mvekelo zophatikizana izi.
- Pelekani nkhani momwe muli mvekelo zonse za tsiku ndipo powelenga zindikilani mamvekelo awa mts, mdz, mkw, ndi phw.

II. Aphunzi :

- Zindikilani mvekelo mts, mkw, phw, ndi mdz pamakhadi oonetsedwa.
- Achule mau omwe Ali ndi mvekelo mts, mdz, mkw, ndi phw.
- Awelenge nkhani yopatsidwa ndi Kuzindikila mvekelo zonse zopasidwa pa tsiku.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila mvekelo mnkhani kwacitidwa moyenela.

CIGAWO: MVETSO

Mutu 1: Mvetso ya kumvetsela

Mutu Waung'ono 1: Colinga ceni-ceni

Luso Lapadela: Kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva.

Ciyambi: Mutu uyu udzaona pa kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga umene wamveka, kufupukitsa uthenga, kuzindikila colinga ca nkhani ndi kuzindikila zoona za nkhani.

Mau Ofunika Kudziwa: Colinga, Kusonyeza, Uthenga, Kufupukitsa, Nkhani, Zoona

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila: Mabuku a aphunzi , Machati a Nkhani.

Mfundo Zophunzitsa:

- Phunzitsani aphunzi m'mene angazindikilile colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva.
- Phunzitsani aphunzi m'mene angafupikitsile uthenga.
- Phunzitsani aphunzi m'mene angazindikilile colinga ca nkhani ndi m'mene angazindikilile zoona za nkhani.

 **Nchito A: Kuzindikila Ndi Kusonyeza Colinga Ceni-Ceni Ca Uthenga Umene Wamveka.**

I. Mphunzitsi:

- Nenani nkhani yaifupi yomwe ili ndi uthenga omveka bwino

Citsanzo:

Maliya ndi mwana waulemu. Makolo ake amukonda kwambili. Iye akabwela kucokela ku sukulu , amatunga madzi ndi kusuka mbale. Uyu ndi mwana wocititsa cidwi kwambili.

- Kambilanani colinga ceni-ceni ca uthenga umene uli munkhaniyi.
- Nenani nkhani ina yaifupi yomwe ili ndi uthenga womveka bwino. Udzani aphunzi kuti azindikile colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva m'nkhaniyo.

II. Aphunzi:

- Amvele nkhani yofotokezedwa ndi mphunzitsi
- Azindikile colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva m'nkhani.
- Anene nkhani m'magulu ao yomwe ili ndi uthenga womveka bwino'.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga m'nkhani kwacitika moyenela.

 **Nchito B: Kufupukitsa nkhani.**

I. Mphunzitsi:

- Phunzitsani aphunzi m'mene angafupikitsile nkhani.
- Fotokozani kwa aphunzi kuti pofupikitsa uthenga timatenga mfundo zeni-zeni za nkhani.
- Pelekani citsanzo comveka bwino ca kufupikitsa uthenga ponena nkhani yaifupi ndi kunena mfundo zeni-zeni za nkhaniyo.

II. Aphunzi :

- Amvesele zolankhula mphunzitsi
- Awelenge nkhani yopatsidwa.
- Ayetsese kufupikitsa nkhani pogwilitsa nchito mfundo zeni-zeni za nkhani.

Muyeso Woyembekezeleka: Dongosolo yakufupukitsa nkhani yacitika moyenela.

Mutu Waung'ono 2: Cilungamo Ndi Zoganiza.

 **Ciyambi :** Mutu waung'ono uyu udzaona pa zacilungamo ndi zoganiza za munthu kucokela mnkhani.

 **Mau Ofunikila Kudziwa:** Cilungamo, maganizo.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Buku ya nkhani, chati ya nkhani.

Mfundo Zophunzitsa:

- Cilungamo ndi zoganiza mnkhani.
- Kusiyanitsa pa zacilungamo ndi zoganiza mnkhani.



Nchito A: Kupeza Zoganiza Kucokela Mnkhani

I. Mphunzitsi:

- Lembani nkhani pa bolodi
- Welengani nkhani ku aphunzi

Citsanzo

Ayisi kilimu ndi cakudya cabwino mu calo conse. Koma ine ndikonda mtundu wopangidwa ndi cokoleti.

- Funsani aphunzi mafunso awa kuti mumvele zoganiza Zao.

1. Kodi munthu uyu anali kuganiza ciani mnkhaniyi?

2. Cifukwa ninji ayisi kilimu anthu ambili aikonda?

3. Kodi Inu muikonda ayisi kilimu?

4. Ndicifukwa nciani muikondela?

II. Aphunzi :

- Awelenge nkhani.
- Ayankhe mafunso pakupeleka maganizo ao pa nkhani.
- Akambilane ndi kugawana maganizo ao pa nkhani.

Muyeso Woyembekezeleka: Kupeza zomwe munthu aganiza pa nkhani zacitika moyenela.



Nchito B: Kupeza Zacilungamo Mnkhani

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani kwa aphunzi.

Citsanzo

Dzuwa inalengedwa ndi mulungu. Iyo imacokela kumawa ndi kulowela ku madzulo. Koma anthu ambili akhulupilila kuti dzuwa siyiyenda .

- Funsani aphunzi pa za nkhani yowelengedwa.

1. Kodi zacilungamo mu nkhaniyi ndi zotani?

2. Kodi ndi zoona kuti dzuwa icokela ku mawa?

3. Kodi ndi cilungamo kuti dzuwa siyiyenda?

II. Aphunzi :

- Awelenge nkhani
- Akambilane pa nkhani yomwe awelenga
- Ayankhe mafunso ndi Kulankhula cilungamo pa zomwe Zalembedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kupeza cilungamo mnkhani yolembedwa kwacitidwa moyenela.

Mwacidule : Mutu uyu unali kuona pa kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga umene wamveka, kufupukitsa uthenga, kuzindikila colinga ca nkhani ndi kuzindikila zoona za nkhani.

Mutu 2: Mvetso Ya Kuwelenga

Mutu Waung'ono : Zoona Za Nkhani

Luso Lapadela: Kupeleka uthenga ofotokozedwa mokwana mndime (Ziganizo ziwili kapena zitatu)



Ciyambi: Mutu uyu udzaona pa kunena zomwe zawelengedwa ,Ocita sewelo, malo ocitikila sewelo ndi m'mene sewelo linacitikila kucokela ku ciyambi mpaka kumapeto, kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa pophatikizapo

poyankha mafunso otele; (Ciani? Ndani? Kuti? Liti? Motani?) ndi kunena mwatsatane-tsatane wa zocitika mnkhani.

**Mau Ofunikila Kudziwa:** mvetso, zoona, cilungamo.

Zida Zophunzitsila Ndi Kuphunzilila: Mchati ya nkhani, Mabuku a nkhani.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kunena (kufotokoza) zomwe zawelengedwa.
- kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa.
- kunena mwatsatane-tsatane wa zocitika mnkhani.

**Nchito A: Kunena Zomwe Zawelengedwa**

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani yosangalatsa yomwe ifotokoza za Ocita sewelo
- Uzdani aphunzi kuti nawonso awelenge nkhani yomwe mphunzitsi wawelenga
- Funsani aphunzi mafunso kucokela ku nkhani yomwe awelenga.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani yowelengedwa ndi mphunzitsi
- Awelenge nkhani yomwe mphunzitsi wawelenga.
- Anene zomwe amvela atawelenga nkhani.

Muyeso Woyembekezeleka: Kunena zomwe zawelengedwa kwacitika moyenela.

**Nchito B: Kuyankha Mafunso Kucokela Ku Zomwe Zawelengedwa**

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani yaifupi kwa aphunzi.

- Funsani aphunzi kuti awelenge nkhani yomweyo
- Udzani aphunzi kuti awelenge nkhani m'magulu awili-awili.
- Funsani mafunso kucokela ku nkhani yowelengedwa.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani yowelengedwa
- Awelenge nkhani onse pamodzi
- Awelenge nkhani awili-awili
- Ayankhe mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa kwacitika moyenela.



Nchito C: Kunena Mwatsatane-Tsatane Wa Zocitika Mnkhani

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani yaifupi yoyenelela pomwe aphunzi akumvetsela modekha.
- Fotokozani tsatane-tsatane wa nkhani yomwe mwawelenga.
- Uzani aphunzi kuti nawonso awelenge nkhani yaifupi yoyenelela ndipo amvetsetse nkhaniyo.
- Udzani aphunzi kuti Afotokoze tsatane-tsatane wa nkhani yomwe awelenga kucokela ku ciyambi mpaka kuothela.

II. Aphunzi:

- Amvelele ku nkhani yowelengedwa
- Amvetsele tsatane – tsatane wa nkhani wofotokozedwa ndi mphunzitsi
- Anene tsatane-tsatane wa zocitika m'nkhani yomwe awelenga kucokela ku ciyambi mpaka kothela
- Awelenge nkhani yaifupi ndi Kufotokoza tsatane – tsatane wa nkhani.

Muyeso Woyembekezeleka: Kunena tsatane-tsatane wa zocitika mnkhani kwacitika moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa Kunena zomwe zawelengedwa, kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa ndi kunena tsatane-tsatane wa zocitika mnkhani.

Mutu : Malembedwe

Mutu Waung'ono 1: Kapangidwe ka lembo

Ciyambi : Mutu waung'ono uyu udzaona pa kapangidwe ndi kujambula malembo.

Luso Lapadela : Kulemba malembo

Mau Ofunikila Kudziwa : Malembedwe, malembo.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila : Chati ya malembo, pensulo, mapepala.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuphunzitsa mapangidwe a lembo.
- Malembedwe a malembo akulu ndi ang'ono.

Nchito A: Kujambula Malembo

I. Mphunzitsi:

- onetsani aphunzi kabuku ka malembedwe a malembo.
- onetsani ndi kusonyeza kagwilidwe ka pensulo polemba.
- phunzitsani molembela lembo iliyonse kwa aphunzi pa mapepala ao.

Zitsanzo:

e e e e e e e e e e e e e e e e e e e e e

k k k k k k k k k k k k k k k k k k k k k

m m m m m m m m m m m m m m m m

II. Aphunzi :

- Amvetsele kwa Mphunzitsi molembela malembo.
- Ayetselele kulemba malembo pa mapepala ao.
- Alembe malembo akulu paokha ndiponso ang'ono m'njila yolungama.

 **Zocita:**

Jambulani malembo awa.

1. a a a a a a a

2. b b b b b b b

3. c c c c c c c

Muyeso Woyembekezeleka: kujambula ndi kulemba malembo kwacitika moyenela.

 **Nchito B: Kulemba Malembo**

I. Mphunzitsi :

- onetsani aphunzi kabuku ka malembedwe a malembo.
- onetsani ndi kusonyeza kagwilidwe ka pensulo polemba.
- phunzitsani molembela lembo iliyonse kwa aphunzi pa mapepala ao.

Zitsanzo:

a a a a a a a

b b b b b b b

c c c c c c c

II. Aphunzi :

- Amvetsele kwa Mphunzitsi molembela malembo.
- Ayetselele kulemba malembo pa mapepala ao.
- Alembe malembo akulu paokha ndiponso ang'ono m'njila yolungama.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula ndi kulemba malembo kwacitika moyenela.

Mutu Waung'ono 2: Kujambula Mau m'malembedwe okhazikika

 **Ciyambi:** Mutu waung'ono uyu udzaona pakujambula mau m'malembedwe okhazikika

Luso Lapadela: Kulemba mau mnjila yokhazikika.

 **Mau Ofunikila Kudziwa:** Malembedwe, kujambula, kukhazikika.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila: Machati ya malembedwe, pensulo, mapepala.

Mfundo Zophunzitsa:

- Malembedwe okhazikika
- Kujambula mau m'malembedwe okhazikika

 **Nchito A: Kujambula Mau Mumalembedwe Abwino Ndiponso Okhazikika.**

I. Mphunzitsi:

- Onetsani mau olembedwa pa pepala.
- Udzani aphunzi kuti ajambule mau aja m'malembedwe oyenela.

Zitsanzo:

1. Mdzathu
2. Mdzandipeza
3. Mdzabwela

II. Aphunzi:

- Aone mau olembedwa pa pepala.
- Alembe mau aja m'malembedwe abwino kulondola lamulo La malembedwe.

 **Zocita:**

Jambulani ndi kulemba mau awa.

1. Mtsikana, mtsinje, mtsinika

2. Nkhuku, nkhani, nkhuni, nkhululu.

Muyeso Woyembekezeleka: Kulemba mau m'malembedwe abwino kwacitika moyenela.

Mutu Waung'ono 3: Mipata Ya Mau.

 **Ciyambi:** Mutu waung'ono uyu udzaona pa kujambula ziganizo m'malembedwe abwino ndiponso okhazikika pakusiya mipata.

Luso Lapadela: Kusiya mipata m'mau polemba.

 **Mau Ofunikila Kudziwa**: Mau, mipata.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila: Makhadi ya mau, chati ya ziganizo.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kalembedwe ka ziganizo
- Mipata ya mau



Nchito : Kujambula Ziganizo M'malembedwe okhazikika Pa Kusiya Mipata.

I. Mphunzitsi:

- Onetsani ziganizo zomwe zilibe mipata pakati pa mau.
- Pelekani zitsanzo pakufotokoza bwino-bwino mosiyila mipata.

Citsanzo:

1. Mtsikanaalikutungamadzi.

= Mtsikana Ali kutunga madzi

II. Aphunzi:

- Aone ziganizo zolembedwa ndipo azindikile mau pomwe apelela pakuonetsa mipata.
- Apenyelele pa zitsanzo zopatsidwa zakuonetsa ziganizo zopanda mipata.



Zocita:

Onetsani mipata ya mau pa kulemba ziganizo izi.

1. Anyamataanaphwanyamtsukodzulo.

2. Atateanagulankhumbadzulo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula ziganizo m'malembedwe abwino pakusiya mipata kwacitika moyenela.

 **Mwacidule :** Mutu uyu unali kuona pa kapangidwe ka malembo, malembedwe okhazikika, kulemba mau pakusiya mipata ndi kujambula ziganizo mnjila yokhazikika.

MUTU 2: CIMANGILIZO

Mutu Waung'ono: Nkhani Yapafupi

 **Ciyambi**: Mutu uyu uzaona pakujambula zinthunzi zomwe zidzapeleka uthenga womangilizidwa pamodzi.

Luso Lapadela: Kulemba nkhani yapafupi

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Phensulo, Pepala, Makileyoni.

 **Mau Ofunikila Kudziw**a: Zithunzi, Uthenga, Kujambula.

Mfundo Zophunzitsila:

- Fotokozelani aphunzi kuti tingathe kufotokoza malingalilo pakulemba nkhani yapafupi yomwe tiganiza.
- Patsani citsanzo camalingalilo omwe angalembedwe mkankhani kapafupi.

 **Nchito: Kulemba Nkhani Yapafupi**

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti alembe kankhani kapafupi pa cinthu comwe akonda kwambili
- Pelekani citsanzo ca nkhani yapafupi

Nkhani

Bechani ndi mwana wosamvela.

Kawili-kawili amacita ndeu ndi anzake powatema myala,

Dzulo, mphunzinzitsi anampanda ndi kumpatsa cilango kamba kakuba mapensulo a anzake

II. Aphunzi:

- Amvetsele nkhani yokambidwa ndi mphunzitsi.
- Alembe nkhani yao-yao yapafupi

Muyeso Woyembekezeleka: Kulemba nkhani yaifupi kwacitika moyenela.

 **Mwacidule:** Mutuyu unali kuona pa kulemba nkhani yapafupi yao-yao aphunzi

CAPAMUTU 6: KULOWEZA MAU OPINDA LILIME

CIGAWO: KUMVETSELA NDI KULANKHULA

 **Ciyambi:** Cigawo ici cidzaona pa kumvetsela ndi kulankhula zomwe ndi nthambi za maluso a kachulidwe ka mau ndi kasankhidwe ka mau ogwilitsa nchito polankhula. Cigawoci cidzaonanso pa kuwelenga mofulumila, matanthauzo a mau ndi mvetso ya kumvetsela ndi ya kuwelenga. Cidzaonanso pa malembedwe owelengeka ndi okhazikika.

Mutu: ZIlapi ndi mau opinda lilime

Mutu waung'ono: Mau opinda lilime

 **Ciyambi:** Mutu waung'ono uyu udzaona pa mau opinda lilime, malankhulidwe ake ndi zolinga zosiyana-siyana za mau opinda lilime.

 **Luso Lapadela:** Kuloweza mau opinda lilime

Mau ofunika kudziwa:

Zilapi, ndagi, kupinda, lilime, kuloweza, kuceza, kufulumila, tanthauzo, kulondola, kuthandiza, luso, zosangalatsa.

Zida zophunzitsila ndi zophunzilila: Mabuku a aphunzi owelenga, mabuku a zilapi ndi a mau opinda lilime .

Mfundo zophunzitsa: Kuphunzitsa aphunzi mau opinda lilime ndi malowezedwe ake.

 **Nchito: Kuloweza mau opinda lilime**

I Mphunzitsi:

- Lankhulani ciganizo ca mau opinda lilime modekha ndiponso mofulumila kwa aphunzi ndipo muwafunse zomwe amvapo.
- Fotokozani tanthauzo la mau opinda lilime kwa aphunzi (Mau opinda lilime ndi ziganizo zopangidwa kukhala zobvuta kalankhula mofulumila ndi molondola mau cifukwa ca kufanana kwa mamvekedwe a mau m'ziganizozo. Mau opinda lilime amagwilitsidwa nchito kukhala masewela a mau, kuphunzila kulankhula, kuceza ndi zosangalatsa. Yamathandiza kupititsa patsogolo maluso a kachulidwe ka mau, kuwelenga mofulumila ndi kulankhula zofunika kulemba).
- Lankhulani ciganizo ca mau opinda lilime cimodzi mofulumila ndi kuuza aphunzi kuti acilankhulenso mofulumila.

  Mau opinda lilime:

  Citsanzo:

  Mnkhwele wamankhwala wagwa mphwai ndi kutaya mnkhwani pomva mtswatswa wa nkhwali mnkhalango.
- Kambilanani momwe aphunzi alankhulila mau opinda lilime.
- Uzani aphunzi kuti alankhule mau opinda lilime yomwe adziwa.
- Kambilanani zolankhula zao.
- Lankhulani mau opinda lilime osiyana-siyana ndi aphunzi.
- Uzani aphunzi m'modzi-m'modzi kuti alankhule mau opinda lilime omwe mukukambilana nao.

II Aphunzi:

- Amvetsetse pomwe mphunzitsi akulankhula mau opinda lilime ndi kuyankha mafunso.
- Kumvetsela ku tanthauzo la mau opinda lilime.
- Kulankhulanso mau opinda lilime okambidwa ndi mphunzitsi.
- Kukambilana ndi mphunzitsi momwe mau opinda lilime akambideila.
- Alankhule mau opinda lilime m'modzi-m'modzi pamodzi ndi mphunzitsi.
- Kukambilana ndi mphunzitsi **m**omwe alankhulila mau opinda lilime.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuloweza mau opinda lilime kwacitika moyenela.

**Mwacidule:** Mutu uyu unali uzaona pa mau opinda lilime, malankhulidwe ake ndi zolinga zosiyana-siyana za mau opinda lilime.

CIGAWO: KUWELENGA

Mutu: Kuzindikila Masilabe

Mutu Waung'ono: Kuzindikila mvekelo **mtsw-, mphw-, nkhw-, mnkhw-**

**Lambulo:** mutu waung'ono uyu udzayang'ana pa kuzindikila masilabe m'mau olankhulidwa, kucita masewela owelenga masilabe, kupanga mau olankhulidwa pogwilitsa nchito masilabe ndi kucita masewela opanga mau.

Luso lapadela: Kuzindikila masilabe ndi kupanga mau pogwilitsa nchito masilabe M**tswa, mtswe, mtswi.**

Mphwa, mphwe, mphwi.

Nkhwa, nkhwe, nkhwi.

Mnkhwa, mnkhwe, mkhwi

**Mau ofunika kudziwa:** Masilabe, mau, chati, makhadi

Zida zophunzitsila ndi zophunzilila:

Chati ya masilabe, mabuku a aphunzi owelenga ndi makhadi ya masilabe.

Mfundo zophunzitsa:

- Kuzindikila masilabe omwe apanga mau.
- Kuzindikila malembo omwe apanga masilabe.

- Kupanga mau pogwilitsa nchito masilabe.

 **Nchito A: Kuzindikila masilabe m’mau olankhulidwa**

I Mphunzitsi:

- Lankhulani mau osiyana-siyana ndi kuuza aphunzi zigawo za mauwo kuti ndiye masilabe.

  Citsanzo:

  Mu liu ‘mtswatswa’ muli masilabe awili (2), mtswa - tswa.

- Lankhulani mau osiyana-siyana pamodzi ndi aphunzi ndi kuyagawa-gawa.

  Citsanzo:

  Kamtswatswako Ka - mtswa - tswa - ko

- Uzani aphunzi kuti alankhule mau awo-awo, kuyagawa-gawa ndi kuwelenga nambala ya masilabe omwe alimo.
  - **Citani cimodzi-modzi ndi mau ena osiyana-siyana.**

II Aphunzi:

- Kumvetsela pomwe mphunzitsi akufotokoza masilabe.
- Alankhule mau osiyana-siyana ndi kuyagawa-gawa.
- Alankhule mau awo-awo, kuyagawagawa ndi kuwelenga nambala ya masilabe m'mauwo.

 **Nchito B: Kucita masewela owelenga masilabe**

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kuwelenga nambala ya masilabe m’mau olankhulidwa mwa kuwomba m'manja kulingana ndi nambala ya masilabewo.

  Citsanzo:

mnkhwele	mnkhwe ----- le	(kuomba kawili ------ 2).
mnkwani	mnkhwa ----- ni	(kuomba kawili ------ 2).

- Uzani aphunzi kuti acite masewela owelenga nambala ya masilabe omwe ali m'mau poomba m'manja.

II Aphunzi:

- Aonetsetse pomwe mphunzitsi akupeleka citsanzo ca nambala ya masilabe m'mau poomba m'manja.
- Acite masewela owelenga nambala ya masilabe m'mau poomba m'manja.

- **Citani cimodzi-modzi ndi mau omwe ali ndi masilabe ena onse otsalila.**

	a	e	i	o	u
mtsw	mtswa	mtswe	mtwsi	mtswo	mtswu
mphw	mphwa	mphwe	mphwi	mphwo	mphwu
nkhw	nkhwa	nkhwe	nkhwi	nkhwo	nkhwu
mnkhw	mnkhwa	mnkhwe	mnkhwi	mnkhwo	mnkhwu

Muyeso Woyembekezeleka: Kucita masewela owelenga masilabe kwacitika moyenela.

Nchito C: Kupanga mau olankhulidwa pogwilitsa nchito masilabe.

I Mphunzitsi:

- Pangani mau olankhulidwa pogwilitsa nchito masilabe. Citsanzo: mtswatswa, mtswetswetswe, mtswitswi.

II Aphunzi:

- Apange mau pogwilitsa nchito masilabe.



Nchito D: Kucita masewela opanga mau

I Mphunzitsi:

- Pangani mau osiyana-siyana kucokela ku masilabe olankhulidwa.
  Citsanzo:
  mtswatswa – mphatswa, mtswetswetswe – tswetswe.
- Uzani aphunzi kuti apange mau osiyana-siyana kucokela ku masilabe olankhulidwa.

II Aphunzi:

- Amvetsele modekha kwa mphunzitsi pomwe akupanga mau kucokela ku masilabe.
- Apange mau osiyana-siyana kucokela ku masilabe olankhulidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila masilabe kucokela ku mau olankhulidwa kwacitidwa moyenela.



Mwacidule: Aphunzi aphunzila kuzindikila masilabe, kucita masewela owelenga nambala ya masilabe kucokela ku mau olankhulidwa, kupanga mau kucokela ku masilabe olankhulidwa ndi kucita masewela opanga mau olankhulidwa.

Mutu: Kupanga Masilabe

Mutu Waung'ono 2: Masilabe

Luso Lapadela: Kulumikidza makonsonanti ndi mavawelo kupanga masilabe.

Mau ofunika kudziwa: Makonsonanti, mavawelo, Kulumikidza.

 **Nchito A: Kupanga masilabe kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo.**

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kupanga masilabe polumikidza makonsonanti ndi mavawelo.
  Citsanzo:
  Mphw ---- a mphwa.
  Mphw----e mphwe.
- Uzani aphunzi kuti apange masilabe ena mofanana.

	a	e	i	o	u
mtsw	mtswa	mtswe	mtswi	mtswo	mtswu
mphw	mphwa	mphwe	mphwi	mphwo	mphwu
nkhw	nkhwa	nkhwe	nkhwi	nkhwo	nkhwu
mnkhw	mnkhwa	mnkhwe	mnkhwi	mnkhwo	mnkhwu

II Aphunzi:

- Kumvetsela ndi akuonetsetsa pomwe mphunzitsi akupeleka citsanzo ca kupanga masilabe pogwilitsa nchito makonsonanti ndi mavawelo.
- Apange masilabe ena pogwilitsa nchito makonsonanti ndi mavawelo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kulumikidza masilabe kupanga mau kwacitka moyenela.

Nchito B: Kuwelenga chati ya masilabe

	a	e	i	o	u
mtsw	mtswa	mtswe	mtswi	mtswo	mtswu
mphw	mphwa	mphwe	mphwi	mphwo	mphwu
nkhw	nkhwa	nkhwe	nkhwi	nkhwo	mkhwu
mnkhw	mnkhwa	mnkhwe	mnkhwi	mnkhwo	mnkhwu

I Mphunzitsi:

- Citani citsanzo ca kuwelenga masilabe pa chati ya masilabe.

  Citsanzo:

  Kuwelenga, kucokela dzanja lamanzele kupita ku dzanja lamanja, kucokela kumwamba kupita pansi, mopendeka (diagonal), zigizagi.
- Uzani aphunzi kuti adzawelenge masilabe pa chati ya masilabe m'modzi-m'modzi.
- Ikani aphunzi awili-awili ndi kuwapatsa timachati ting'ono-ting'ono kuti awelenge.

II Aphunzi:

- Aonetsetse zomwe mphunzitsi akucita popanga masilabe pa chati ya masilabe.
- Awelenge masilabe pa chati ya masilabe.
- Awelenge masilabe pa timachati ting'ono-ting'ono ali awili-awili.

  Muyeso Woyembekezeleka: kuwelenga masilabe kucokela pa chati ya masilabe kwacitika moyenela.

Nchito C: Kusankha masilabe

I. Mphunzitsi:

- Sonyezani aphunzi kusankhani masilabe kucokela pa makhadi ya malembo, masilabe ndi mau .
- Uzani aphunzi kuti asankhe masilabe kucokela pa makhadi ya malembo, masilabe ndi mau.

  Citsanzo:

  Uzani aphunzi kuti asankhe masilabe pa makhadi otsatilawa:

  tema, mwa, mwala, kh, phu, ndende, mbi, mtswa, mtsw, njuzi, ny, ng', ng'o, mphwa, mf, khwe, bwino, thyo, vwe, gwi, dwambe.

mnkhwele	vwe	nyemba	nkhwa	Mnkhw	mphwi	nthyo
mwa	gwi	mtswa	mph	nd	ng'o	mwala
ng'	tyo.	mnkhwani	njuta	nkhwe	bv	ng'ombe
dwambe	kh	ndende	kwi	phula	nthy	mnkhwe

II Aphunzi:

- Aonetsetse zomwe mphunzitsi akucita posankha makhadi ya malembo, masilabe ndi mau.
- Asankhe masilabe kucokela pa makhadi ya malembo, masilabe ndi mau moyenela.

Muyeso Woyembekezeleka: Kusankha masilabe kucokela pa makhadi ya malembo, masilabe ndi mau kwacitika moyenela.

Nchito D: Kusintha Masilabe

I Mphunzitsi:

- Phunzitsani kasinthidwe ka malembo ku masilabe.

  Citsanzo:

  “mphwa” ngati mwacotsako “mphw” ndi kuikako “phw” iknala “phwa”.

- Uzani aphunzi kuti asinthe malembo ndi kupanga masilabe atsopano.

II Aphunzi:

- Kumvetsela mofatsa pomwe mphunzitsi akupeleka citsanzo ca kusintha masilabe ndi kupanga mau atsopano.
- Asinthe malembo ku masilabe ndi kupanga masilabe atsopano.

Muyeso Woyembekezeleka: kusintha masilabe mu mau kwacitika moyenela.

 **Nchito E:** Kulumikidza makonsonanti omwe sapanga mvekelo limodzi ndi mavawelo kupanga masilabe.

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca makonsonanti omwe sapanga mvekelo limodzi ndi kupanga masilabe poikako mavawelo.

  Citsanzo:

  mphwa, ngwe, thyo, mthyu, mkwi.

- Uzani aphunzi kuti apange masilabe awo pogwilitsa nchito makonsonanti omwe amveka mosiyana popanga masilabe.

II. Aphunzi:

- Aonetsetse citsanzo ca makonsonanti omwe sapanga mvekelo limodzi poikako mavawelo ndi kupanga masilabe.

- Apange masilabe kugwilitsa nchito makonsonanti omwe sapanga mvekelo imodzi poikako mavawelo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kusinthanitsa malembo ku masilabe ndi kupanga masilabe atsopano kwacitika moyenela.

**Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona pa kupanga masilabe kucokela ku makonsonanti ndi mavawelo, kuwelenga chati ya masilabe, kusankha masilabe kucokela ku makhadi ya malembo, masilabe ndi mau ndi kusintha malembo ku masilabe kuti yapange masilabe yatsopano.

Mutu2: Kupanga Mau

Mutu waung'ono 2: Mau (mtswi/mphwi/nkhw/mnkhw)

**Lambulo**: Mutu waung'ono uyu udzaona pa kulumikidza masilabe ndi kupanga mau kusintha ndi kucotsa masilabe ndi kuwelenga nambala ya masilabe.

Luso lapadela: Kulumikidza masilabe ndi kupanga mau.

**Mau ofunika kudziwa:** Kulumikidza, Kusintha, kucotsa, tsopano

Zida zophunzitsila ndi zophunzilila: Makhadi, chati, masilabe, mphunzi

Mfundo zophunzitsa:

- Kulumikidza masilabe ndi kupanga mau.
- Kusintha ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano.
- Kuzindikila masilabe m'mau ndi kuwelenga nambala ya masilabe m'mau.

**Nchito A:** Kulumikidza masilabe ndi kupanga mau (mtswi/mphw/nkhw//mnkhw)

I Mphunzitsi:

- Sonyezani kulumikidza masilabe kucokela pa chati ya masilabe ndi kupanga mau.

- Lumikidzani masilabe kucokela ku makhadi ya masilabe ndi kupanga mau.
- Uzani aphunzi kuti alumikidze masilabe kucokela pa chati ya masilabe ndi ku makhadi ya masilabe ndi kupanga mau.

II Aphunzi:

- Aonetsetse kalumikidzidwe ka masilabe kucokela pa chati ya masilabe ndi kupanga mau.
- Alumikidze masilabe kucokela ku makhadi ya masilabe ndi kupanga mau.

- Alumikidze masilabe kucokela pa chati ya masilabe ndi ku makhadi ya masilabe ndi kupanga mau.

Muyeso Woyembekezeleka: Kulumikidza masilabe ndi kupanga mau kwacitika moyenela.



Nchito B: Kusintha ndi kucotsa masilabe

I **Mphunzitsi:**

- Sinthani ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano.
  Citsanzo:
  “nkhwangwa” mukacotsa “nkhwa” ndi kuikako “mnkhwa” ikhala “mnkhwangwa”, “zamankhwala”, mukacotsako “za” ikhala “mankhwala”.
- Uzani aphunzi kuti asinthe ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano moyenela.

II Aphunzi:

- Aonetsetse citsanzo ca kusintha ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano.

- Asinthe ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano.

Muyeso Woyembekezeleka: Kusintha ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano kwacitika moyenela.

 **Nchito C: Kuzindikila masilabe m’mau.**

I Mphunzitsi:

- Phunzitsani m’mene aphunzi angazindikilile masilabe m’mau.
  Mwacitsanzo, konsonanti iliyonse yomwe ili ndi vawelo kutsogolo kwake imachedwa kuti silabe.
  Citsanzo:
  mu liu lakuti “lunkhwakwa” muli masilabe atatu (3) “lu”, “nkhwa” ndi “kwa”.
- Uzani aphunzi kuti azindikile masilabe m’mau opatsidwa.
  Mau:
  Cinkhwa, nkhwakwa, nkhwangwa, nkhwali, nkhwekwe, nkhwewakwewa, mnkhwani, mankhwala, bilimankhwe, nkhwazi.

II Aphunzi:

- Amvetsele kwa mphunzitsi m'mene angazindikilile masilabe m'mau.

- Azindikile masilabe m’mau opatsidwa ndi m’mabuku owelenga.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila masilabe m’mau kwacitika moyenela.

 **Nchito D:** Kuwelenga nambala ya masilabe

I Mphunzitsi:

- Lembani mau pa bolodi ndi kuwelenga nambala ya masilabe m’mau olembedwawo.
- Citsanzo:
  “bilimankhwe” muli masilabe anai (4): bi – li – ma - nkhwe.

- Uzani aphunzi kuti alankhule mau, anene ndi kulemba nambala ya masilabe m’mauwo.

II Aphunzi:

- Alankhule mau, anene ndi kulemba nambala ya masilabe m’mauwo.

Meyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga nambala ya masilabe m’mau kwacitika moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kulumikidza masilabe ndi kupanga mau, Kusintha ndi kucotsa masilabe ndi kupanga mau atsopano, kuzindikila masilabe m’mau ndi kuwelenga nambala ya masilabe m’mau.

Mutu 3: Kuwelenga Mofulumila

Mutu Waung’ono 1: Kuwelenga mau mokweza.

Lambulo: Mutu uyu udzaona pa kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau koyenela.

Luso Lapadela 2: Kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka moyenela.

Mau ofunika kudziwa: Nthano, bolodi, kufulumila.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Makhadi ya mau, timabuku ta nthano, mabuku a aphunzi.

Mfundo Zophunzitsa: Kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka bwino.

-

Nchito: Kuwelenga mau

I **Mphunzitsi:**

- Pelekani citsanzo ca kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka koyenela powelenga mau pa bolodi ndi pogwilitsa nchito timabuku ta nthano.
- Uzani aphunzi kuti awelenge mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka moyenela monga m'citsanzo.
- Ikani aphunzi awili-awili ndi kuwauza kuti awelenge mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka bwino monga mcitsanzo ca mphunzitsi.

II. Aphunzi:

- Amvetsele modekha pomwe Mphunzitsi akupeleka citsanzo ca kuwelenga Mofulumila.
- Awelenge mau mofulumila ndi kachulidwe Ka mau koyenela monga m'citsanzo.
- Awelenge mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka koyenela.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka bwino kwacitika moyenela.

Luso Lapadela 3: Kuwelenga ndime mokweza ndi kachulidwe ka mau komveka bwino.

Mau Ofunika Kudziwa: Nthano, bolodi, kufulumila.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Makhadi ya mau, timabuku ta nthano, mabuku a aphunzi.

Mfundo zophunzitsa: Kuwelenga mau mofulumila ndi kachulidwe ka mau komveka bwino.

Nchito A: Kuwelenga ndi kumvetsa ziganizo

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kuwelenga ndime mofulumila.
- Welengani ndime pamodzi ndi aphunzi ndipo funsani aphunzi mafunso kucokela mu ndime yowelengedwa.

II Aphunzi:

- Kumvetsela pomwe mphunzitsi akupeleka citsanzo ca kuwelenga ndime mofulumila.

- Awelenge ndi kuyankha mafunso kucokela ku ndime yowelengedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga ndime mofulumila, kuimvetsetsa ndi kuyankha mafunso kucokela m'ndimeyo kwacitika moyenela.

Nchito B: Kuwelenga ndime kucoka pa ziganizo ziwili (2) kufika pa ziganizo zisanu (5) (kuwelenga kwa gulu, kubwelezela zomwe wina wawelenga kale, kuwelenga awili-awili).

I Mphunzitsi:

- Welengani ndime momveka bwino pomwe aphunzi akumvetsela modekha.
- Welengani Pamodzi ndi aphunzi (Choral Reading).
- Uzani aphunzi kuti adzibwelezela zomwe mphunzitsi akuwelenga (Echo Reading).
- Uzani aphunzi kuti awelenge awili-awili (Paired Reading).

II Aphunzi:

- Amvetsele modekha pomwe mphunzitsi akupeleka citsanzo ca kuwelenga.
- Awelenge pomodzi ndi mphunzitsi.
- Adzibwelezela zomwe mphunzitsi akuwelenga
- Awelenge pamodzi ndi mphunzitsi, abwelezele zomwe mphunzitsi akuwelenga ndiponso awelenge awili-awili.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga ndime kucoka pa ziganizo ziwili (2) kufika pa ziganizo zisanu (5), kuwelenga kwa gulu, kubwelezela zomwe wina wawelenga kale, kuwelenga awili-awili kwacitika moyenela.

Nchito C: Kuwelenga momveka ndime yomwe ili ndi mamvekelo ndi malembo osiyana-siyana.

I Mphunzitsi:

- Lembani malembo, masilabe ndi mau omwe ali ndi mamvekelo osiyana-siyana.
  Mwacitsanzo:
  Malembo:
  mtsw, mkw, thy, mdw, nkh, khw.
  Masilabe: mtswa, mphwa, nkhwe, mnkhwe, mkwi, thyo, ndwa, nkhu, khwe.
  Mau:
  mtswatswa , mphwai, nkhwekwe, mnkhwele,mkwiyo, thyola, nkhunda, khwenga.
- Welengani ndi kumvetsetsa mau opangidwa kucokela ku masilabe omwe apangidwa ndi malembo amamvekedwe osiyana-siyana.
- Uzani aphunzi kuti alembe, awelenge ndi kumvetsetsa mau opangidwa kucokela ku masilabe omwe apangidwa ndi malembo amamvekedwe osiyana-siyana.

II Aphunzi:

- Aonetsetse m'mene mphunzitsi akulembela malembo, masilabe ndi mau omwe ali ndi mamvekelo osiyana.
- Awelenge ndi kumvetsetsa mau omwe ali ndi mamvekelo osiyana.
- Alembe, awelenge ndi kumvetsetsa mau opangidwa kucokela ku masilabe omwe apangidwa ndi malembo amamvekedwe osiyana-siyana.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuwelenga momveka ndime yomwe ili ndi mamvekelo ndi malembo osiyana-siyana kwacitika moyenela .

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kuwelenga mau mofulumila pogwilitsa nchito kachulidwe ka mau komveka bwino.

CIGAWO: MAU.

Mutu : Maina

Mutu Waung'ono : Maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.

**Lambulo:** Mutu uyu udzaona pa kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa , kupanga maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa, Kulinganiza maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa ndi kusinthanitsa zocitikazi ndi kucita masewela a maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.

Luso Lapadela: Kupanga maina oculukitsidwa ndi maina osaculukitsidwa (**Mtsw, mphw, nkhw, mnkhw**).

**Mau Ofunika Kudziwa:** Dzina , maina, kuculukitsa, cimodzi, kuzindikila

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Chati ya maina, .

Mfundo Zophunzitsa: Kazindikilidwe ka maina eni-eni ndi maina wamba

**Nchito A**: Kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa .

I **Mphunzitsi:** .

- Sonyezani kunga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa .

Mwacitsanzo:

1. Mtsogoleli —-- atsogoleli

2. mphunzitsi —-- aphunzitsi

- Pamodzi ndi aphunzi, pangani maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.
- Uzani aphunzi kuti apange ndi kulemba maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

II Aphunzi:

- Aonetsetse momwe mphunzitsi akupangila maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.
- Pamodzi ndi mphunzitsi, apange maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.
- Apange ndi kulemba maina oulukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku Maina osaculukitsidwa kwacitika moyenela.



Nchito B Kupanga Maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kupanga maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

Citsatnzo

1. Amnkhwele ….. mnkhwele
2. Amphawi ….. m'mphawi

- Pangani maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa pamodzi ndi aphunzi.
- Uzani aphunzi kuti apange maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.

II Aphunzi:

- Aonetsetse m'mene mphunzitsi akupangila maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa.
- Apange maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa pamodzi ndi mphunzitsi.
- Apange dzina la cinthu cimodzi kucokela ku maina a zinthu zambili.

Muyeso Woyembekezeleka: Kupanga maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa kwacitika moyenela.

 **Nchito C: Kulinganiza maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa**

I Mphunzitsi:

- Sonyezani kulinganiza maina osaculukitsidwa comwe cili ku dzanja lamanzele ndi maina oculukitsidwa omwe ali ku dzanja lamanja.

  Citsanzo:

  1. mkwekwesa—-- mikwekwesa 2. mphunzitsi —- aphunzitsi
- Pamodzi ndi aphunzi, linganizani maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.

- Uzani aphunzi kuti alinganize maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.

II Aphunzi

- Aonetsetse m'mene mphunzitsi akulinganizila maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.
- Aonetsetse momwe mphunzitsi akulinganizila dzina la cinthu cimodzi ndi maina ambili

  Muyeso Woyembekezeleka: Kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa kwacitika moyenela.

 **Nchito D:** Kucita masewela a maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.

I. Mphunzitsi:

- Ikani aphunzi m’magulu a asanu.
- Ikani makhadi ya maina oculukitsidwa ndi makhadi a maina osaculukitsidwa pansi pa gulu lililonse kuti aphunzi adzipikisana posankha makhadi yofunika kuti asankhe maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.

- Uzani aphunzi kuti asankhe makhadi ya maina osaculukitsidwa ndi makhadi ya maina oculukitsidwa.

II. Aphunzi

- Akhale m'magulu a asanu-asanu.
- Alandile makhadi a maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa.
- Asankhe makhadi ya maina oculukitsidwa ndi makhadi ya maina osaculukitsidwa .

Muyeso Woyembekezeleka: kucita masewela osankha maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa kwacitika moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kupanga maina oculukitsidwa kucokela ku maina osaculukitsidwa, kupanga maina osaculukitsidwa kucokela ku maina oculukitsidwa, kulinganiza maina osaculukitsidwa ndi maina oculukitsidwa ndi kulinganiza maina oculukitsidwa ndi maina osaculukitsidwa.

CIGAWO: MVETSO

Mutu 1: Mvetso ya Kumvetsela

Mutu Waung'ono 1: Colinga ceni-ceni

Lambulo: Mutu uyu udzaona pa kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga umene wamveka, kuzindikila ndi Kupeleka maganizo pa uthenga umene wamveka ndi kufupukitsa uthenga.

Luso Lapadela: Kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva.

Mau Ofunika Kudziwa: Maganizo, lingalilo, maganizo, kusonyeza, uthenga, kufupikitsa, nkhani, zoona

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: mabuku a aphunzi

Mfundo zophunzitsa:

- Phunzitsani aphunzi m’mene angazindikilile colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva, m’mene angafupikitsile uthenga, m’mene angazindikilile colinga ca nkhani ndi m’mene angazindikilile zoona za nkhani.

 **Nchito A: Kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga umene wamveka.**

I. Mphunzitsi:

- Nenani nkhani yaifupi yomwe ili ndi uthenga omveka bwino.

  Citsanzo:
  Ukhondo ndi ofunika kwambili.
  Tiyenela kusesa panyumba masiku onse.Tikatelo tidzateteza matenda ambili monga cifuwa ndi kolela. Anthu aukhondo amakhala athanzi labwino nthawi zonse.
- Pamodzi ndi aphunzi, kambilanani colinga ceni-ceni ca uthenga umene uli m'nkhaniyi.
- Nenani nkhani ina yaifupi yomwe ili ndi uthenga womveka bwino.
- Uzani aphunzi kuti azindikile colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva m’nkhaniyo.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani yaifupi yomwe mphunzitsi adzanena.
- Pamodzi ndi mphunzitsi, akambilane colinga ceni-ceni ca uthenga umene uli m'nkhani.
- Amvetsele ku nkhani ina yaifupi yomwe ili ndi uthenga womveka bwino.
- Azindikile colinga ceni-ceni ca uthenga umene amva m’nkhani.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila ndi kusonyeza colinga ceni-ceni ca uthenga umene wamveka kwacitika moyenela.

 **Nchito B:** Kufupikitsa uthenga

I. Mphunzitsi:

- Fotokozani kwa aphunzi kuti pofupikitsa uthenga timatenga mfundo zeni-zeni za nkhani.
- Pelekani citsanzo comveka bwino ca kufupikitsa uthenga ponena nkhani yaifupi ndi kunena mfundo zeni-zeni za nkhaniyo.
- Kambilanani ndi aphunzi momwe mungafupikitsile uthenga wa nkhani potengamo mfundo zeni-zeni.
- Uzani aphunzi nkhani yomveka bwino ndipo muwauze kuti aifupikitse popeleka mfundo zeni-zeni.

II. Aphunzi

- Amvetsele modekha pomwe mphunzitsi akufotokoza m'mene angafupikitsile uthenga.
- Amvetsele mofatsa pomwe mphunzitsi akusimba nkhani yaifupi ndi Kufupikitsa uthenga.
- Akambilane ndi mphunzitsi momwe angafupikitsile uthenga wa nkhani potengamo mfundo zeni-zeni.
- Abweleze kunena nkhani yomwe mphunzitsi wanena ndi kuifupikitsa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kufupukitsa uthenga kwacitika moyenela

Mutu Waung'ono 2: Zoona ndi malingalilo.

 **Lambulo:** Mutu Waung'ono uyu udzaona pa kuzindikila malingalilo m'nkhani ndi kuzindikila zoona za nkhani.

Luso Lapadela: Kusiyanitsa zoona ndi malingalilo.

Mau Ofunika Kudziwa: Malingalilo, kusiyanitsa, zoona, nkhani, kuzindikila.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Makhadi ya nkhani, mabuku a aphunzi owelenga.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kuphunzitsa tanthauzo la liu "Malingalilo".
- Kuphunzitsa za malingalilo pa nkhani yokambidwa.. .

Nchito A: Kuzindikila malingalilo m'nkhani.

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca nkhani ndipo kambilanani ndi aphunzi pozindikila malingalilo m'nkhaniyo.
- Kambilanani ndi aphunzi ndipo apeleke maganizo ao pa colinga ca nkhaniyo.
- Nenani nkhani ina yofanana ndi citsanzo ndipo uzani aphunzi kuti apeleke maganizo ao pa kuzindikila colinga ca nkhaniyo.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku citsanzo ca nkhani.
- Akambilane ndi mphunzitsi pa malingalilo a nkhani yokambidwa.
- Apeleke maganizo ya kuzindikila colinga ca nkhani yonenedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuzindikila colinga ca nkhani kwacitika moyenela.

Nchito B: Kuzindikila zoona za nkhani

I. Mphunzitsi:

- Nenani nkhani yaifupi ya ziganizo zoti aphunzi anu amvetse.

 **Mwacitsanzo**:

Kalulu ndi kanyama kocenjela kwambili.

Iko kamanamiza nyama zinzake nthawi zambili.

Kalinso ndi liwilo loculuka zedi. Makutu ake ndi atali-atali ndipo mcila wake ndi waufupi. Kamakonda kudya udzu wochedwa kasendandulu.

- Kambilanani ndi aphunzi zoona za nkhani yomwe yokambidwa.
- Uzani aphunzi kuti anene zoona za nkhani yomwe amva.

II. Aphunzi:

- Amvetsele ku nkhani yaifupi yokambidwa ndi mphunzitsi.
- Akambilane ndi mphunzitsi pa zoona za nkhani yomwe amva.
- Anene zoona za nkhani yomwe amva.

Muyeso woyembekezeleka: kuzindikila malingalilo m'nkhani ndi kuzindikila zoona za nkhani kwacitika moyenela.

Mutu 2: Mvetso ya Kuwelenga

Mutu waung'ono : Zoona za nkhani

 **Ciyambi:** Mutu uyu udzaona pa kunena zomwe zawelengedwa (Ocita sewelo, malo ocitikila sewelo ndi m'mene sewelo linacitikila kucokela ku ciyambi mpaka kumapeto…), kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa kuphatikizapo (Ciani? Ndani? Kuti? Liti? Motani?) ndi kunena zocitika m'nkhani molondola.

Luso lapadela: Kupeleka uthenga wofotokozedwa mokwana m'ndime (Ziganizo ziwili kapena zitatu)

Mfundo zophunzitsa:

- Kufotokoza zomwe zawelengedwa

- kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa
- kunena zocitika m'nkhani molondola.

 **Nchito A: Kufotokoza zomwe zawelengedwa**

I. Mphunzitsi:

- Welengani nkhani yosangalatsa yomwe ifotokoza za Ocita sewelo, malo komwe sewelo linacitikila ndi m’mene sewelo linacitikila kucokela pa ciyambi mpaka ku mapeto.
- Kambilanani ndi aphunzi za nkhani yomwe yawelengedwa.
- Ikani aphunzi m'magulu ang'ono-ang'ono.
- Uzani aphunzi kuti awelenge nkhani yomwe mphunzitsi wawelenga mcitsanzo ca kuwelenga.

II. Aphunzi:

- Amvetsele nkhani yomwe yawelengedwa ndi mphunzitsi yofotokoza za Ocita sewelo, malo komwe kunacikila sewelo ndi momwe sewelo linacitikila kucokela pa ciyambi mpaka kumapeto.
- Akambilane ndi mphunzitsi za nkhani yomwe yawelengedwa.
- **M'magulu a asanu-asanu, a**welegenso nkhani yomwe mphunzitsi wawelenga.

Muyeso Woyembekezeleka: Kufotokoza zomwe zawelengedwa kwacitika moyenela.

 **Nchito B: Kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa**

I. Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kuwelenga nkhani yaifupi yoyenelela kwa aphunzi.
- Welengani pamodzi ndi aphunzi.

- Uzani aphunzi kuti awelenge nkhani m’magulu a awili-awili.
- Funsani mafunso kucokela ku nkhani yowelengedwa.

II. Aphunzi:

- Amvetsele kwa mphunzitsi pomwe akuwelenga nkhani.
- Awelenge nkhani pamodzi ndi mphunzitsi
- Awelenge nkhani ali awili-awili .
- Ayankhe mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa.

Muyeso Woyembekezeleka: Kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa kwacitika moyenela.



Nchito C: Kunena zocitika m'nkhani molondola.

I. **Mphunzitsi:**

- Welengani nkhani yaifupi yoyenelela pomwe aphunzi akumvetsela modekha.
- Kambilanani ndi aphunzi zomwe zawelengedwa m'nkhani.
- Fotokozani nkhani yomwe mwawelenga molondola.
- Uzani aphunzi kuti awelenge nkhani yaifupi yoyenela ndipo aimvetsetse.

- Uzani aphunzi kuti Afotokoze nkhani yomwe awelenga kucokela ku ciyambi mpaka kumapeto.

II Aphunzi:

- Amvetsele modekha kwa mphunzitsi pomwe akuwelenga nkhani.
- Akambilane ndi mphunzitsi pa zomwe zawelengedwa m'nkhani.
- Afotokoze zocitika m'nkhani molondola.
- Afotokoze zocitika m’nkhani yomwe awelenga molondola.

Muyeso Woyembekezeleka: Kufotokoza zocitika m'nkhani molondola kwacitika moyenela.

Mwacidule: Mutu uyu unali kuona pa kufotokoza zomwe zawelengedwa, kuyankha mafunso kucokela ku zomwe zawelengedwa ndi kufotokoza zocitika m’nkhani molondola.

CIGAWO: KULEMBA

Mutu: Malembedwe

Mutu waung’ono1: Mapangidwe a Lembo

Ciyambi: Mutu uyu udzaona pa kujambula malembo, kulemba malembo, kulemba mau m’malembedwe okhazikika ndi kujambula ziganizo m’malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

Luso Lapadela: Kulemba malembo

Mau Ofunika Kudziwa: Malembedwe, owelengeka, okhazikika, mpata, kujambula.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Coko, phensulo, mabuku olembamo aphunzi.

Mfundo zophunzitsa:

- Kusonyeza majambulidwe a malembo kucokela koyambila polemba mpaka kumapeto poonetsa mayendedwe a dzanja lomwe lili ndi colembela.
- Malembedwe a malembo opatsidwa.
- Kujambula ziganizo m’malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

 **Nchito A:** Kujambula malembo

I Mphunzitsi:

- Pelekani citsanzo ca kulemba malembo awa : **m, t, s, w / m, p, h, w / n, k, h, w / m, n, k, h, w /** m’malembedwe okhazikika m’mizela olembedwelatu pa bolodi.
- Uzani aphunzi kuti ajambule malembo monga m'citsanzo ca mphunzitsi pa bolodi.
- Ongolelani aphunzi pomwe akujambula malembo pa bolodi.
- Uzani aphunzi kuti ajambule malembo omwe alembedwa pa bolodi m'mabuku ao olembamo.

II Aphunzi:

- Aonetsetse pomwe mphunzitsi akulembela malembo m'malembedwe okhazikika m'mizela olembedwelatu pa bolodi.
- Ajambule malembo monga m'citsanzo ca mphunzitsi pa bolodi mothandizidwa ndi mphunzitsi..
- Ajambule malembo omwe alembedwa pa bolodi m’mabuku ao olembamo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula malembo kwacitika moyenela.

 **Nchito B:** Kulemba malembo

I Mphunzitsi:

- Sonyezani m’mene malembo alembedwela m’malembedwe okhazikika m’mizela olembedwelatu pa bolodi.
- Onetsani aphunzi mayambidwe a kulemba malembo kucokela koyambila mpaka kumapeto.
- Uzani aphunzi kuti adzalembe malembo m’mizela ali pa bolodi.
- Uzani aphunzi kuti alembe malembo opatsidwa m'mabuku ao olembamo.

II Aphunzi:

- Aonetsetse m'mene mphunzitsi akulembela malembo pa bolodi m'mizela olembedwelatu.
- Aonetsetse mayambidwe a kulemba lembo kucokela koyambila mpaka kumapeto kwa lembo.
- Uzani aphunzi kuti adzalembe malembo m'mizela omwe ali pa bolodi.
- Alembe malembo omwe apatsidwa m'mabuku ao olembamo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kulemba malembo kwacitika moyenela.

Mutu Waung’ono 2: Malembedwe okhazikika

Luso Lapadela: Kulemba mau owelengeka m’malembedwe okhazikika.

**Ciyambi**: Mutu waung’ono uyu udzaona pa kujambula mau owelengeka m’malembedwe okhazikika m’mizela opangidwilatu pa bolodi.

**Mau Ofunika Kudziwa: M**au, kujambula, mizela, owelengeka, okhazikika.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Coko, mapensulo, mabuku olembamo aphunzi.

Mfundo Zophunzitsa:

- Kujambula mau m’malembedwe okhazikika.

Nchito: Kujambula mau owelengeka m’malembedwe okhazikika.

I Mphunzitsi:

- Lembani mau pa bolodi m’mizela pomwe aphunzi akuonetsetsa mayendetsedwe a dzanja lomwe likulemba.
- Uzani aphunzi kuti adzajambule mau owelengeka m’malembedwe okhazikika m’mizela pa bolodi mothandizidwa ndi mphunzitsi.
- Uzani aphunzi kuti ajambule mau owelengeka m’malembedwe okhazikika m’mizela m’mabuku ao olembamo.

II Aphunzi:

- Aonetsetse m'mene mphunzitsi akulembela mau pa bolodi.
- Ajambule mau owelengeka m'malembedwe okhazikika pa bolodi mothandizidwa ndi mphunzitsi.
- Ajambule mau owelengeka m’malembedwe okhazikika m’mizela m’mabuku ao olembamo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula mau owelengeka m’malembedwe okhazikika kwacitika moyenela.

Mutu Waung’ono 3: Kusiya mipata pakati pa mau.

Ciyambi: Mutu waung’ono uyu udzaona pa kujambula ziganizo m’malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

Luso Lapadela: Kusiya mipata pakati pa mau.

Mau Ofunika Kudziwa: Kujambula, ziganizo posiya mipata, pakati, mau.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Coko, mapensulo, mabuku owelenga a aphunzi, mabuku olembamo aphunzi.

Mfundo zophunzitsa:

- Kujambula ziganizo m’malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

 **Nchito**: Kujambula ziganizo m’malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

I Mphunzitsi:

- Lembani ziganizo m’malembedwe okhazikika pa bolodi pomwe aphunzi akuonetsetsa.
- Lankhulani za mipata yomwe mukusiya polemba ziganizo.
- Uzani aphunzi kuti adzajambule ziganizo m’malembedwe okhazikika m’mizela pa bolodi, (mphunzi m’modzi ciganizo cimodzi), mothandizidwa ndi mphunzitsi.
- Kambilanani za majambulidwe a ziganizo zomwe aphunzi ajambula pa bolodi.
- Uzani aphunzi kuti ajambule ziganizo m’malembedwe okhazikika m’mizela omwe ali m’mabuku ao olembamo posiya mipata pakati pa mau.

II Aphunzi:

- Aonetsetse m'mene mphunzitsi akulembela ziganizo m'malembedwe okhazikika m'mizela olembedwelatu pa bolodi.
- Amvetsele kwa mphunzitsi za mipata yomwe akusiya polemba ziganizo.
- Ajambule ziganizo m'malembedwe okhazikika m'mizela olembedwelatu pa bolodi mothandizidwa ndi mphunzitsi.
- Kambilanani ndi mphunzitsi za majambulidwe a ziganizo zomwe ajambula m'mizela olembedwelatu pa bolodi.
- Ajambule ziganizo m’malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau m'mabuku ao olembamo.

Muyeso Woyembekezeleka: Kujambula ziganizo m'malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau kwacitika moyenela.

**Mwacidule:** Mutu waung'ono uyu unali kuona pa kujambula malembo, Kulemba malembo, kulemba mau owelengeka m'malembedwe okhazikika ndi Kujambula ziganizo m'malembedwe okhazikika posiya mipata pakati pa mau.

Mutu 2: Cimangilizo

Mutu Waung'ono: Nkhani Yapafupi

 **Ciyambi**: Mutu uyu uzayanga'na pakujambula zinthunzi zomwe zidzapeleka uthenga womangilizidwa pamodzi.

Luso Lapadela: Kulemba nkhani yapafupi m'mizele iwili kapena itatu

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila: Phensulo, Pepala, Makileyoni.

**Mau Ofunikila Kudziw**a: Zithunzi, Uthenga, Kujambula.

Mfundo Zophunzitsila:

- Fotokozelani aphunzi kuti tingathe kufotokoza malingalilo pakulemba nkhani yapafupi yomwe tiganiza.
- Patsani citsanzo camalingalilo omwe angalembedwe mkankhani kapafupi.

 **Nchito: composing a simple story**

I. Mphunzitsi:

- Uzani aphunzi kuti alembe kankhani kapafupi pa cinthu comwe akonda kwambili m'mizele iwili kapena itatu

- Pelekani citsanzo ca nkhani yapafupi

Nkhani

Kupanga congo mkalasi ndi koipa.

Kumasokonezana polemba

Ena amalemba zomwe anzao akamba mcongo cija.

II. Aphunzi:

- Amvetsele nkhani yokambidwa ndi mphunzitsi.
- Alembe nkhani yao-yao yapafupi

Muyeso Woyembekezeleka: Kulemba nkhani yaifupi kwacitika moyenela.

 **Mwacidule:** Mutu uyu unali kuona kulemba nkhani yapafupi yao-yao aphunzi

BIBLIOGRAPHY

Ministry of Education. (2023). *Early Childhood Education Syllabus (3-5 Years) Level 1 – 3. Lusaka:* Curriculum Development Centre

Ministry of Education. (2023). *2023 Zambia Education Curriculum Framework. Lusaka:* Curriculum Development Centre

Ministry of General Education. (2019). *Early Childhood Development and Education: Guide on Production of Low-Cost Play, Teaching and Learning Materials*. Lusaka: Directorate of Early Childhood Education.

Ministry of General Education. (2015). Early Childhood Education Teachers' Diploma Syllabus. Lusaka: Directorate of Teacher Education and Specialised Services.

Ministry of Education, Science, Vocational Training and Early Education. (2013). National Literacy Framework. Lusaka: Curriculum Development Center.

Ministry of Education, Science, Vocational Training and Early Education. (2013). *Early Childhood Education Syllabi (3-6 Years) Level 1 – 3.* Lusaka: Zambia Education Publishing House.

Ministry of Education. (1977). *Zambian Languages Orthography.* Lusaka: National Educational Company of Zambia (NECZAM)

Ministry of Education. (1977). Educating Our Future Policy. Lusaka: Institutional supplier limited.

Ministry of Education. (1996). Educating Our Future: National Policy on Education. Lusaka: ZEPH. Available at http://www.moge.gov.zm/?wpfb_dl=55